فیضانِ بسم اللہ

# Faizan-e-

# بسم اللہ

Oyambitsa
Lamasulidwa m'chichewa ndi

Sheikh-e-Tariqat Amir-Ahl-e-Sunnat Il fondatore di Dawatelslami Allama Moulana Abu Bilal
**MUHAMMAD ILYAS**
Attar Qadiri Razavi

فَیضانِ بِسۡمِ اللّٰه

# Faizan-e-بِسۡمِ اللّٰه

## *MADALITSO A* بِسۡمِ اللّٰه

### VOLUYOMU 1

Shaykh-e-Tariqat, Ameer-e-Ahl-e-Sunnat,
Muyambisi wa Dawat-e-Islami, 'Allamah Maulana Abu Bilal

Muhammad Ilyas Attar

Qadiri Razavi دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَه

# Madalitso a Sunnah

Kumasulira mchichewa kwa Faizan-e-Bismillah

◆

## ALL RIGHTS RESERVED

Copyright © 2023 Maktaba-tul-Madinah

Palibe gawo lililonse la bukhuli limene lingazasindikizidweso, kusungidwa mu kachitidwe kochotsa kapena kufalitsa mwa maonekedwe alionse kapena mwa njira iliyonse, kudzera mzamagesi,makina, kujambula kapena mwinamwake kopanda chilolezo cholemba kuchokela kwa Maktaba-tul-Madinah.

**buku:** loyamba

**Lamasulidwa ndi 4:** Nthambi yomasulira ya (Dawat-e-Islami)

**wosindikiza:** Maktaba-tul-Madinah

## NTHANDIZO

Ngati mungafune kuthandiza kusindikiza buku la chipembedzo kapena kabuku ka Isal-e-Sawab kwa abale omwe anakusiyani, khalani omasuka ndi kulumikizana nafe.

**Maktaba-tul-Madinah**

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah Mahallah Saudagran, Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

✍ **E-mail:** maktabaglobal@dawateislami.net – maktaba@dawateislami.net

✆ **Phone:** +92-21-34921389-93

**Fax:** + 92-21-34125858

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَ الصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الْمُرْسَلِيْنَ
اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ ؕ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ ؕ

# Dua powerenga Buku

Werengani Du'a li (pemphero) musanayambe kuwerenga buku lokhuza za chipembedzo kapena phunziro la Chisilamu, muzakumbukira zonse zomwe mwaphunzira اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ:

اَللّٰهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَانْشُرْ
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَاالْجَلَالِ وَالْاِكْرَام

## Kumasulira

**E Allah, titsegulilen ife makomo achidziwitso komanso nzeru, tichitilen chifundo, Eh inu Wolemekeza kwambiri komanso Waulemelero opambana.**

*(Al-Mustaṭraf, vol. 1, p. 40)*

**Chidziwitso:** Werengani Salat_Alan-Nabi ﷺ kamodzi musanayambe komanso mukamaliza kunena Du'a li.

# Zamkati mwapatali patali

Faizan-e-Sunnat

Kuyamikiridwa kochokera kwa ma Mufti komanso Ophunzira wolemekezeka........................................x-xiv
Zolinga 23 zowerengera Bukuli.......................................................................................... xv-xvi
Mawu oyamba .......................................................................................................... xvii-xviii
Mphatso yochokera kwa Attar.......................................................................................... xix
Zolemba za Omasulira....................................................................................................... xx

**Madalitso a بِسْمِ اللّٰه ............................................................................................... 1-112**

**Makhalidwe a pokudya mu Chisilamu ........................................................................ 113-414**
Makhalidwe a pakudya ...................................................................................... 113-215
Zakudya za Ziwanda....................................................................................... 217-226 99
Mafanizo................................................................................................................ 227-366
Madani Muzakarah .............................................................................................. 367-397
Kalata yochokela kwa Attar kupita kwa mwana wake okondedwa ................................................ 399-405
Haji Mushtaq Attari .................................................................................................. 407-414

**Kupambana kwa njala ................................................................................415-522 52**
Mafanizo .................................................................................................................... 481-522

**Madalitso a Ramadan ........................................................................................ 523-905**
Kupambana kwa Ramadan ..................................................................................... 523-568
Malamulo a Kusala (Hanafi) ................................................................................ 569-656
Madalitso a Tarawih ........................................................................................... 657-676
Madalitso a Layla-tul-Qadr ..................................................................................... 677-702
Madalitso a I'tikāf ................................................................................................... 703-768
Madalitso a Eid-ul-Fitr ............................................................................................ 769-796
Kupambana kwa kusala kwa Nafl .............................................................................. 797-848
Mafanizo 12 a anthu osala .................................................................................. 849-870 41
Mafanizo olimbikisa a Mu'takifīn ............................................................................ 871-905

40 Hadith zakupambana kwa Salat-'Alan-Nabi ................................................................ 906-913 22
Ngale za Madani zopelekela Dars kuchokela mu Faīzān-e-Sunnat ........................................... 914-916
Njira zopelekelra Dar kuchoka mu Faīzān-e-Sunnat .............................................................. 917-921
Kalembedwe .............................................................................................................. 922-926
Tchati chomasulira ...................................................................................................... 927-928
Bibliography ............................................................................................................ 929-936
Index ......................................................................................................................... 937-950

اَلْحَمْدُ لِلّٰہِ رَبِّ الْعٰلَمِیْنَ وَ الصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰی سَیِّدِ الْمُرْسَلِیْنَ
اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰہِ مِنَ الشَّیْطٰنِ الرَّجِیْمِ ؕ بِسْمِ اللّٰہِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْمِ ؕ

# Mawu mwachidule okhudza mlembi

Mu m'bado ulionse, Allah عَزَّوَجَلَّ anatumidza Munthu opatulika kwa Ummah wa Mtumiki okondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم yemwe anakwaniritsa udindo oitanira anthu ku Chilungamo ndikuwatchinjiriza kuchoka ku zoipa. Anthu olungamawa anaphunzitsa asilamu anzawo malingaliro oti: 'Ndiyenera ndilimbikire kuzisintha ndekha komanso anthu a dziko lonse lapansi اِنْ شَآءَاللّٰه (Mulungu akalola)'.

M'modzi mwa anthu agwiro komanso ophunzira amenewa ndi Shaykh-e-Tariqat Amir-e-Ahl-e-Sunnat, yemwe adayambisa bungwe la Dawat-e-Islami Allamah Maulana Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razvi Ziyaee دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَه. Iwowa anabadwa tsiku lachitatu pa 26 Ramadan 1369 A.H. (12 july 1950) mu m'zinda wa Bab-ul-Madinah (Karachi), Pakistan. Chimwalilire cha bambo awo iwowa ali khanda, Shaykh wa adakumana ndi mavuto ambiri a zachuma, koma iwowa sadataye mtima ndipo anapeza njira zovomerezeka (halaal) zothandizira banja lawo. Kuchokera ali a chichepere, ankakonda kupita ku Mzikiti kukapemphera komanso kuwerenga ndi kumvetsera NA'ATS. Atakula, iwo adali kucheza kwambiri ndi Akatswiri a Ahl-e-Sunnat komanso kuwerenga mabuku a chipembedzo, kotero adaphunzira kopambana komanso adadzindikira zambiri zokhudza chipembedzo. Patadutsa nthawi, iwowa adadzakhala otsogolera pa mzikiti ndipo adavutika kwambiri polimbikitsa "Maitanidwe ku chilungamo". Posangalatsidwa ndi machitidwe, umunthu, machedzedwe komanso khumbo lake lolarikira, anthu ambiri, makamaka achinyamata anakhala abwenzi ake owonadi.

Mu September, chaka cha 1981, adayambitsa Madani kampeni ya Dawat-e-Islami ndi thandidzo lochokera kwa omutsatira a Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Allah عَزَّوَجَلَّ adawadalitsa ndi chidwi pakutetedza chikhulupiliro cha Asilamu ndi kuwakonza mmachitidwe awo. Iwowa amatha kuyenda mu galimoto kapena pa njanji kupita ku madera akutali

komanso akumudzi komanso m'mizinda momwe amakalalikira. Akamapita kokafalitsa uthenga mu dera lililonse la Bab-ul-Madinah (Karachi), kapenanso kukagwira ntchito iliyonse ya chipembedzo, amanyamuliratu chakudya chawo, ngakhale mchere umene komanso madzi ndi cholinga choti asakampemphe aliyense chilichonse. Pena, amatha kukanidzidwa kufalitsa uthenga mu Mzikiti, koma iwowa samakhumudwa.

M'masiku oyambilira, akamaliza kufalitsa uthenga, amabwelera kunyumba kutada ndipo amatha kuyenda makilomita asanu kapena asanu ndi imodzi chifukwa chakuti zokwera za pa ulendo zinkamusiira pa njira ndipo analibe ndalama zokwelera Taxi. Pena amatha kukwedzedwa galimoto ndikuchepetsa mtunda. Iwo anali kunyodzedwa komanso kuchitidwa chipongwe, koma mu zonsezi sanataye mtima ndipo adapitiliza kudzipeleka ku cholinga chawo ngakhale adali kukumana ndi mavuto komanso zipsinjo. Pansi pa utsogoleri wake wa dongosolo komanso wa uzimu, bungwe la Dawat-e-Islami lidaonekela ngati gulu la dziko lonse lapansi, losagwirizana ndi za ndale, la Qur'an komanso Sunnat. Ndipo pakali pano likutumikira Chisilamu m'magawo oposera makumi asanu ndi anayi (90) omwe ena mwa iwo ndi monga Jami'at-tul-Madinah, Madrasa-tul-Madinah, Dar-ul-Madinah, Dar-ul-Ifta Ahl-e-Sunnat, Al-Madina-tul-Ilmiyyah, Maktaba-tul-Maduna, Majlis-e-Tarajim, Majlis I.I., Majlis Madani Qafilah, Majlis Madani In'amat komanso Madani Channel. Mu chisomo cha Allah عَزَّوَجَلَّ, uthenga wa Dawat-e-Islami unafikira maiko oposela zana limodzi mphambu makumi asanu ndi atatu mphambu zisanu ndi ziwiri (187) a dziko lapansi.

Mwakuyesetsa pa okha komanso upangiri wa mawu ake olimbikitsa Sunnat omwe ankapeleka mma IJTIMA'AT a Dawat-e-Islami, iwo anabweretsa kusintha m'miyoyo ya miyanda miyanda ya Asilamu, makamaka asilamu achichepere Amuna komanso Akazi. Achinyamata ambiri ochimwa analapa ku machimo awo ndi kutsatira Sunnah zosiyanasiyana m'miyoyo yawo. Onse omwe sankapemphera sanangoyamba kupemphera, koma anapita patsogolo kwambiri ndikukhala otsogolera mmizikiti; ana osamvera komanso a mwano adayamba kumvera ndi kulemekedza makolo awo; omwe adali kuyenda m'chigwa cha m'dima wosakhulupilira anadalitsidwa ndi kuwala kwa kukhulupilira; omwe adali kusilira kukongola kwa mayiko aku ulaya anada mkhawa ndi kulakalaka kupenya kukongola kwa Ka'abah yoyera komanso chimphika chobiliwira cha pa Mzikiti olemekezdeka wa Madina; omwe anali kudandaula komanso achisoni ndi zam'dziko zokha, adamvesetsa malingaliro a Madani oganizira za moyo wawo wa

pambuyo pake; omwe anali kukonda kuwerenga mabuku a zachikondi anakopeka ndi kuwerenga mabuku a akatswiri a Ahl-e-Sunnat; omwe adali kukonda maulendo anayamba kuyenda ndi MADANI QAFILAHs; omwe adali oipa anakhala asilamu otsata chipembedzo pochita za MADANI IN'AMAT; Azimayi omwe adali kukonda kupita m'masitolo ogulitsa, malo osangalatsa, makalabu a usiku komanso malo owonetsera kanema adatsatira kavalidwe kovomelezeka m'chipembedzo; omwe cholinga chawo chinali kupeza chuma chambiri cha mdzikoli adatengera cholinga cha Madani, "Ndiyenera ndilimbikile kudzisintha ndekha komanso anthu a dziko lonse lapansi اِنْ شَآءَاللّٰه (Mulungu akalola)". Mwachidule "Maitanidwe ku chilungamo" adalimbikitsidwa kwambiri, kubweretsa madalitso a Sunnah paliponse.

Chinthu chofunikira kwambiri ndi chakuti adasintha malingaliro a anthu miyanda miyanda kudzera mu mphamvu ya munthu payekha komanso gulu munthawi yochepa kwambiri. Molimbikitsidwa ndi kulimbika kwake, anyamata komanso atsikana mazana mazana achisilamu akukhala akatswiri a chipembedzo ku Jami'a-tul-Madinah ndi cholinga choti apambane mu moyo wa dziko la pansiri komanso mmoyo omwe uli pambuyo pake, nkusiyana ndi kupanga tsogolo mu ntchito iliyonse ya dziko lapansi. Ana mazana mazana akuphunzira mawerengedwe olondora a Qur'an yolemekedzeka ndipo akukhala ma Huffaz. Inalipo nthawi yomwe zinali zovuta kwa athu akulu akulu kuti akwaniritse I'tkaf mmasiku khumi (10) omalizira a Ramadan, koma pano anyamata mazana mazana samangokwanilitsa kwa masiku khumi (10) koma kwa mwezi onse wa Ramadan kupanga I'tkaf. Ambiri mwa ma MU'TAKIFIN amayendanso ndi ma MADANI QAFILAH mu usiku komanso pa tsiku la Eid akangomaliza I'tkaf mmalo mobwelera m'makomo mwawo. Anthu mazana mazana omwe anali kumeta mosalongosoka komanso amakonda kuvala zovala za chikunja adakongoletsa nkhope zawo ndi ndevu komanso mitu yawo ndi nduwira, kuonetsa chikondi ku Sunnah za Mtumiki okondedwa komanso odalitsidwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم). Mosakaikira, zonsezi zikusonyeza kuti Amir-e-Ahl-e-Sunnat دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَه anabweretsa kusintha m'mitima mwa anthu miyanda miyanda pa dziko lonse lapansi, ndiponso anatsitsimutsa makhalidwe abwino a chisilamu mu zaka za zana la 15 (15th century).

Koma ndi chisomo cha Allah عَزَّوَجَلَّ yekha kuti kupambana konseku kukwaniritsidwe. Powonjezera ku zomwe adalalikira komanso MADANI MUZAKARAH, iwo adalembaso mabuku oposera zana limodzi ndi makumi awiri ndi asanu (125), omwe

ambiri anatanthauziridwa muziyankhulo zosiyanasiyana ndipo adafika m'maiko ambiri. Mwa chisomo cha Allah عَزَّوَجَلَّ, iwo ali otanganidwa kulembanso mabuku ena chifukwa chakuti zolemba za chipembedzo zinakhalano gawo la moyo wawo. Motengera ndi zophunzitsa za Qur'an yolemekezeka, ma Hadith odalitsika onenedwa ndi otsogolera opembedza komanso olungama, iwo adatolera ngale za Madani zosawelengeka m'mabuku awo. Ili mmanja mwanu ndi kumasulira kwa M'chichewa kwa Luso lake *Faizan-e-Sunnat* (vol. 1). Ndi buku lotchuka lomwe limalimbikitsa Sunnah, powerenga zomwe, miyanda miyanda ya azimayi ndi azibambo adayamba kuponda njira ya Umulungu. Pofuna kukwanilitsa kufunidwa kwa bukuli ndi anthu mu dziko lonse, ndondomeko yosindikidza bukuli ikupitilirabe pafupifupi chaka chonse. Kulemba buku kutha kuoneka ngati chinthu cha chizolowezi, koma kulimbikisa miyanda miyanda ya anthu ogonjera kwa Mtumiki kuti awerenge mabukuwo ndi kulondoloza zomwe akuphunzitsa, ndi chinthu chachilendo mwam'theradi.

Timpemphe Allah عَزَّوَجَلَّ kuti aonjezere chidwi kwa olemba mwa chidziwitso komanso ntchito zolungama. Timpemphe Allah عَزَّوَجَلَّ kuti amudalitse ndi moyo wautali komanso wathanzi ndipo amutetedze kwa adani komanso onse omuchitila nsanje.

اٰمِیْن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِیّٖن صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم

**Majlis-e-Tarājim (Dawat-e-Islami)**

Ramadan-ul-Mubārak, 1434 AH

July, 2013

# Kuyamikiridwa[1] kochokera

# kwa ma Mufti komanso Ophunzira olemekezeka

[1] *Kuyamikaku kunachitika mu chi Urdu. Otanthauzila anawatanthauza kupita ku chichewa.*

## Kuyamika

Kuyamikira kuchokera kwa othandizira wa Dawat-e-Islami, katswiri wa maphunziro ‘Allamah Maulana Muhammad Isma’il Qadiri Razvi Nuri مُدَّظِلُّهُ الْعَالِی. (Shaykh-ul-Hadis komanso Rais Dar-ul-Ifta, Dar-ul-Ulum Amjadiyyah Bab-ul-Madinah Karachi).

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الْمُرْسَلِيْنَ اَمَّا بَعْدُ

Ndinali ndi mwayi ophunzira magawo anayi a Faizan-e-Sunnat (volume 1 lomwe linatsindikizidwa mu chaka cha 1427 A.H.) lomwe linapangidwa ndi Amir-e-Ahl-e-Sunnat, yemwe adayambitsa Dawat-e-Islami ‘Allamah Maulana Muhammad Ilyas Attar Qadiri مُدَّظِلُّهُ الْعَالِی. Iwowa amavomelezedwa padziko lonse kuti adapeleka ntchito zazikulu zokhudza chipembedzo cha chisilamu. Chifukwa cha Khama lawo losatopa, asilamu miyanda miyanda, makamaka achichepere, anayamba kutsata njira yoopa Mulungu ndi kuwatsogolera ena mu njira ya Mulunguyi. Lero, gulu la Madani Qafilah la Dawat-e-Islami limapezeka mkati ndi kunja kwa Pakistani. Uthenga omwe ndili nawo pakali pano ndi wakuti uthenga wa Dawat-e-Islami wafikira mmaiko okwanira makumi asanu ndi limodzi (60) apa dziko lapansi.

Mu bukuli, iwo anatolera ngale za chidziwitso ndi mawu anzeru omwe munthu angathe kuwapeza pokhapokha ataphunzira mabuku mazana mazana. Bukuli ndi lothandiza kwambiri pakupeza chidziwitso cha malamulo a Shariah komanso a uzimu, اَللّٰهُمَّ زِدْ فَزِدْ. Kuonjezara kwa ndime zamu Qur’an, hadith, zoyankhula za oyera mtima komanso mafanizo osangalatsa analimbikitsa kukongola kwa bukuli. Zolemba zochokela mmabuku oyambilira zopelekedwa ndi ma hadith, nkhani komanso malamulo, anapangitsa bukuli kukhala lofunika kwambiri kwa ma Ulama. Moonjezera, ndili okondwera pakuona kuti bukuli lilinso ndi ma fanizo a akatswiri komanso anthu oyera mtima a Ahl-e-Sunnat, kuonetsa chikondi chomwe opanga bukuli ali nacho kwa iwo. Umodzi mwa ma ubwino a bukuli ndiwakuti mibado ya mtsogolo izadzindikira ntchito za chipembedzo zomwe anthu oyera mtima komanso akatswiri a Ahl-e-Sunnat adapanga. Ndimpemphe Allah عَزَّوَجَلَّ kuti amulipire mphoto yemwe adapanga bukuli chifukwa cha kuyesetsa kwakukulu ndipo athe kulora msilamu aliyense kuwerenga bukuli ndi kuphunzitsa ena kuchoka ku bukuli.

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

Dar-ul-Ulum Amjadiyyah

17 Muharram 1428 / 6-2-2007

## Kuyamika

Kuyamikira kuchokera kwa Sharaf-e-Millat, Ustaz-ul-Ulama Shaykh Allamah Maulana Muhammad Abdul Hackim Sharaf Qadiri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه.

بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ ط نَحْمَدُهُ وَنُصَلِّيْ عَلٰى رَسُوْلِهِ الْكَرِيْم

Zinayankhulidwa mu Hadith yodalitsika kuti: "مَنْ اَحْيَا سُنَّتِيْ بَعْدَ مَا اُمِيْتَتْ فَلَهٗ اَجْرُ مِئَةِ شَهِيْدٍ" "Kwa yemwe angadzutse Sunnah yaine yomwe inaiwalidwa, pali mphatso yofanana ndi ya anthu zana limodzi (100) omwe anafera chikhulupiliro." Mukuwala kwa Hadith yomwe yakambidwayi, yeselani kulingalira mphoto ya chiwerengero chachikulu cha ofera chikhulupiliro yomwe idzapatsidwe kwa Amir-e-Dawat-e-Islami Allamah Maulana Muhammad Ilyas Attar Qadiri دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَة komanso olalikira a Dawat-e-Islami amene Khama lawo lidalimbikitsa anthu miyanda miyanda kuti adzipemphera mwa kathithi komanso kutengera Sunnah za mtumiki okondedwa komanso odalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Kupambana kwakukuluku kunakwanilitsidwa kudzera mu Khama komanso ntchito za Amir-e-Dawat-e-Islami, makamaka muzoyankhula zake komanso buku lake *'Faizan-e-Sunnat.'*

M'maganizo mwanga, bukuli ndi loyenda malonda kwambiri ku Pakistan. Chiyankhulo chake ndi chosavuta komanso chopatsa upangiri komanso njira yolalikira. Kutsogolo kwanga kuli voliyumu yoyamba ya *Faizan-e-Sunnat* lomwe lidasindikizidwa mu chaka cha 1427 A.H. Bukuli lili ndi mitu inayi

1. Madalitso a بِسْمِ اللّٰه
2. Makhalidwe a pokudya mu Chisilamu
3. Kupambana kwa njala
4. Madalitso a Ramadan

Chinthu choyamikilika cha bukuli ndi chakuti, magwero a maumboni a mabukuli apelekedwaso ndi ndime zamu Qur'an, ma hadith komanso malamulo a Sharia kuonjezera kufunikira kwa bukuli. Lerolino pamene m'dima wa zikhulupiliro komanso chikhalidwe chosakhala chachisilamu ukufalikira paliponse m'dzina la kudziletsa komanso kukulitsa malingaliro, kufunika kofalitsa ziphunzitso komanso Sunnah za mtumiki oyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kwaonjezelekanso kuwirikiza mazana mazana.

Dhul-Hijjah 1428 A.H. / 28 December 2006

## Kuyamika

Kuyamikira kuchokera kwa Khayr-ul-Azkiya, Ustaz-ul-Ulama-wal-Maskhaikh, Jami' Ma'qul-o-Mnquil, Shaykh Allamah Maulana Khuwajah Muzaffar Husayn Sahib DAMAT BARAKATUHUMU-UL-ALLIYAH (Shaykh-ul-Hadis Dar-ul-Ulum Nur-ul-Haq, Chara Muhammad Pur, Faizabad – UP, Al-Hind)

بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ ط نَحْمَدُهٗ وَنُصَلِّيْ عَلٰى رَسُوْلِهِ الْكَرِيْمِ

Mu Chisomo cha Allah عَزَّوَجَلَّ, amene wasayina m'musimu ali ndi mwayi oyamikira mabuku amtengo wapatali a akatswiri ambiri a Ahl-e-Sunnat makamaka kuonjezera Fakhur-ul-Amasil, Bahr-ul-Ulum Shaykh 'Allamah Mufti Afzal Husayn Sahib Mongiri (Dean wakale, Manzar-e-Islam, Bareilly Sharif). Ndinayamikira pafupifupi mabuku ake onse omwe anatsindikizidwa ku India. Pomwe nkulu wa bungwe la Dawat-e-Islami MAJLIS Ulama and Mashaikh Adapereka *Faizan-e-Sunnat* (yomwe inatsindikizidwa mu chaka cha 1427, Buku Loyamba) kwai ine, ndinasangalara kwambiri, ndipo ndidapeleka chiyamikirochi.

Qur'an yopatulika, (ndondomeko yatunthu ya moyo) ili ndi ma "اَمْرٌ وَنَهْىٌ" (malamulo) ambiri owongolera anthu ku njira yowongoka. Kunena kuti "لَقَدْ كَانَ لَكُمْ فِيْ رَسُوْلِ اللّٰهِ اُسْوَةٌ حَسَنَةٌ", Allah عَزَّوَجَلَّ anatchula chitsanzo chowala, ndipo ananena kuti ndikofunikira kwambiri kuti munthu atsatire chitsanzo ichi. Mwanjira ina, Qur'an yopatulika ndi buku lalikulu komanso lolemekedzeka, ndipo zilingati zonena komanso zochita za Mtumiki opatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi mafotokozedwe ake othandizira. Potsatira chitsanzo chowalachi, munthu olengedwa kuchokera ku dothi amakhala ndi makhalidwe a angelo. Zonena komanso zochita za Mtumiki opatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم zinafalitsidwa mmabuku ambiri ama Hadith ndi mabuku ena a asilamu oyera mtima komanso akatswiri.

Gwetsani mvula ya chisomo komanso chifundo kwa Amir-e-Ahl-e-Sunnat, yemwe adayambitsa Dawat-e-Islami, odzipeleka ku Madinah, Allamah Maulana Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razvi Ziyaee دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَة amene watolera bwino maluwa onunkhilawa ndikuwapeleka maluwa wa mu maonekedwe a *'Faizan-e-Sunnat'* kwa amene mitima yawo imagwedwedzeka pokumbukira mtumiki olemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Pamene bukuli

lidatulukira ndi kuphweka kwa chinenero chake ndi kuyenda bwino kwa malemba ake, anthu anayamba kudutsamo ndi misonzi komanso mtima onse.

Pamene buku loyamba lidapelekedwa kwa ine, ndinasangalatsidwa nalo mokuti ndinaliwelenga mobwereza bwereza komanso mogwetsa misozi ndili mu Wudu. Buku lake latsopanoli ndi lokongola komanso lothandiza kwambiri. Maumboni ochokera m'mabuku oyambilira, zoonjezera komanso zosintha zinaonjezera ubwino komanso kukongola kwa bukuli. Komanso, kuphatikiza kwa zochitika zotsitsimutsa chikhulupiliro za Madani Qafilah olimbikitsa Sunnah a gulu la Dawat-e-Islami, lomwe lili gulu la dziko lonse lapansi komanso losagwirizana ndi za ndale Qur'an ndi Sunnah, ndi mbali yapaderadera ya bukuli.

Mukudziwa kwanga, bukuli linagulitsidwa kwambiri ku Pakistan. Bukuli linadziwika kwambiri m'maiko ena apa dziko lonse munthawi yochepa kwambiri. Ndaphunziranso kuti pali ena odzipereka a Dawat-e-Islami omwe adaphunzira masamba onse 1500 a *'Faizan-e-Sunnat'* (buku la Urdu) m'masiku 15 ndipo enanso mu sabata imodzi chabe. Izi zikuonetsa ubwino komanso kalembedwe kogwira mtima ka bukuli.

Ndi pempho langa kwa Msilamu aliyense kuti agule ndi kusunga bukuli mmakomo mwawo, ndi kulipeleka ngati mphatso kwa ena. Enaso alipeleke bukuli kwa mwana wawo kapena mchemwali wawo ngati malowolo pa tsiku la ukwati wake. Kwa ochita bwino (Olemera), makamaka, ayenera agule bukuli mochuluka ndi kukalipeleka ku mizikiti komanso Madrassah. Olalikira onse Achizimayi ndi Achimuna a Dawat-e-Islami komanso anthu Wamba, ngakhaleso anthu apadera aphunzitse bukuli m'makomo, M'mizikiti, m'mashopu, m'mafakitale, m'misika komanso malo ena otanganidwa. Zinanenedwa mu hadith kuti amene angadzutse sunnah yoti inaiwalidwa amalandira mphotho ya anthu zana limodzi (100) omwe anafera chikhulupiliro posunga lonjezori kwa ife.

**Khuwajah Muzaffar Husayn Ravazi**

26 Muharram-ul-Haram 1428 A.H.

Shaykh-ul-Hadis Dar-ul-Ulum Nur-ul-Haq, Chara Muhammad Pur,

Faizabad-UP, Al-Hind

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَ الصَّلٰوةُ وَ السَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الْمُرْسَلِيْنَ
اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ ؕ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ ؕ

# Zolinga 23 zowerengera Bukuli

Mtumiki opatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananena kuti: "نِيَّةُ الْمُؤْمِنِ خَيْرٌ مِّنْ عَمَلِه", "Zolinga za Msilamu ndi zabwino kuposa zochita zake." *(Mu'jam Kabir, vol. 6, p.185, Hadis 5942)*

## Ngale ziwiri za Madani

- Popanda cholinga chabwino, palibe mphoto yomwe imapelekedwa pa ntchito yolungama.
- Pamene munthu apanga zolinga zabwino kwambiri, ndi pamenenso amapeza mphoto yaikulu.

## Zolinga

5. Nthawi iliyonse yomwe ndingawerenge bukuli, ndimayamba ndi kubwereza matamano, kufunira mafuno abwino Mtumiki (Mtendere ndi Madalitso zipite kwa iye), kudzitchinjiriza mwa Allah عَزَّوَجَلَّ komanso kunena Bismillah (powerenga mizere ya mawu a Arabic omwe aperekedwa pamwamba pa tsambali mudzakhala mukuchita pa zolinga zinayi zonsezi).
6. Ndimawerenga bukuli kuyambira pa chiyambi mpaka pamapeto pofuna kumusangalatsa Allah عَزَّوَجَلَّ
7. Mwakuthekera kwanga, ndimayesetsa kuwerenga bukuli ndili ndi Wuzu komanso nditayang'ana ku Qiblah.
8. Ndidzaona Ayah za mu Qur'an.
9. Komanso ma Hadith odalitsika.

10. (Powerenga bukuli) Nthawi iliyonse ndingawerenge dzina la Allah, ndimanena عَزَّوَجَلَّ.

11. Ndipo nthawi iliyonse ndingawerenge dzina la Mtumiki odalitsika komanso okondedwa ndimawerenga صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.

12. Kutsatira malangizo operekedwa mu nkhaniyo: "عِنْدَ ذِكْرِ الصَّالِحِيْنَ تَنَزَّلُ الرَّحْمَةُ" "Chisoni chimatsika mu nthawi yomwe anthu olungama atchulidwa." *(Hilyat-ul-Auliya, vol. 7, p. 335, Hadis 10750)* Ndidzatuta madalitso otchula anthu olungama pofotokoza mafanizo a oyera mtima kuchoka mu bukuli, kupita kwa ena.

13. (Pa kope langa) Ndidzatsindika zinthu zofunikira komanso Mfundo pofuna kuziwunikira.

14. Ndidzalemba Mfundo zofunikira ndikamawerenga.

15. Ndidzakopa ena kuti awerenge bukuli

16. Ndicholinga chokhazikika pa Hadith yoti: "تَهَادَوْا تَحَابُّوْا" "Perekani mphatso kwa wina ndi mzake, mudzakhala okondana pakati panu." *(Muwatta Imam Malik vol. 2, p. 407, Hadis 1731)* ndidzagula bukuli (limodzi kapena ambiri momwe ndingakwaniritsire) ndi kulipeleka ngati mphatso kwa ena. (Lipelekeni ngati mphatso kwa ophunzira komanso otsogolera, mudzalandira mphotho yaikulu اِنْ شَآءَ اللّٰه).

17. Ndipereka Sawab yowerengera bukuli ku Ummah onse.

18. Ndikapeza cholakwika chilichonse chokhudza Shariah, ndizadziwitsa osindikiza za kulakwikaku polemba (Uthenga wa pakamwa nthawi zambiri umakhala opanda phindu).

19. Ndidzaphunzitsa kuchoka mu bukuli mwa chizolowezi.

20. Ndidzawerenga bukuli kuyambira pa chiyambi mpaka pa mapeto chaka chilichonse.

21. Ngati sindikumvetsetsa lamulo linalake, ndidzafunsa akatswiri kuti anditambasulire ndi cholinga chokhazikika pa Ayah:

فَسۡـَٔلُوۡۤا اَهۡلَ الذِّكۡرِ اِنۡ كُنۡتُمۡ لَا تَعۡلَمُوۡنَ ﴿۴۳﴾

**O inu anthu! funsani omwe ali ozindikira mwa inu ngati inu musali kudziwa.**

*[Kanz-ul-Iman (Translation of the Qur'an)] (Part 14, Surah An-Nahl, verse 43)*

22. Ngati ndingapeze lamulo lovuta kumvetsa, ndizaliwerenga mobwereza bwereza.
23. Ndidzafalitsa ziphunzitso za chisilamu kwa omwe asakuzidziwa.

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَ الصَّلٰوةُ وَ السَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الْمُرْسَلِيْنَ
اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ ؕ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ ؕ

# Mawu oyamba

Kuchoka kwa: Shaykh-e-Tariq, Amir-e-Ahl-e-Sunnat, yemwe adayambitsa bungwe laDawat-e-Islami, Allamah Maulana Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Ravzi دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَه.

Mtumiki okondedwa komanso odalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Aliyense amene angalalikire za chiphunzisto cha chisilamu ku Ummah wanga ndi cholinga choti Sunnah ikhazikitsidwe kapena kuti zikhulupiliro za chinyengo zichotsedwe, azalowa kumwamba." *(Hilyat-ul-Auliya, vol. 10, p. 45, Hadis 14466)*. Ndi imodzi mwa ntchito za Madani a Dawat-e-Islami, gulu la dziko lonse lapansi komanso losagwirizana ndi za ndale la Qur'an komanso Sunnah, kwa msilamu aliyense kuti amvetsele kapena aphunzitse ma phunziro awiri tsiku lirilonse (ku Mzikiti angakhale kunyumba ndi malo ena). Pofuna kukwanilitsa zochita za Madani zokhudza ma phunziro, ndili ndi mwayi opeleka bukuli *'Faizan-e-Sunnat'* (volume 1) ndi zolinga zabwino. Phunzitsani kuchoka mu bukuli mochuluka. Ngati pangapezeke munthu yemwe wayamba kutsata njira ya Qur'an komanso Sunnah, inuso muzakhala opambana اِنْ شَآءَاللّٰه. Mtumiki olemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Ngati Mulungu adalitsa ngakhale munthu mmodzi ndi chiongoko chodzera mwa iwe, izi nzabwino kwa iwe kuposa ngamira zofiira." *(Sahih Muslim, p. 1311, Hadis 2406)*

*'Faizan-e-Sunnat'* (volume 1) ili ndi mitu inayi komanso masamba pafupifupi 1572 (mu Urdu version). Pamodzi ndi akatswiri komanso osankhidwa, chiwerengero chachikulu cha anthu Wamba nawonso alowa nawo gulu lolimbikitsa Sunnah la Dawat-e-Islami. Kuti anthu Wamba apindule, ndagwiritsa ntchito chiyankhulo chosavuta komanso ndasunga kalembedwe komveka bwino. M'malo ena, ndagwiritsa mwadala mawu ovuta komanso matanthauzo ake m'mabulaketi kuti abale ndi alongo achisilamu osaphunzira kwambiri asakumane ndi vuto powerenga mawu omwewo mmabuku ena a chisilamu.

Tachita zonse zothekera kuti tichotse zolakwika m'bukuli koma kuthekera kwa zolakwika sikungathetsedwe. Choncho, ngati mungapeze cholakwika chilichonse chosamphana ndi Sharia m'bukuli, chonde ndidziwitseni polemba, ndipo muzalandira malipiro oyenera. Sindingatsutsane mopanda nzeru mokomera malingaliro anga koma ndibwerera kumbuyo ndikuthokoza.

Ndili ndi ngongole yaikulu kwa akatswiri a Al-Madina-tul-Ilmiyyah, akatswiri a Chisunni opangidwa ndi nthambi ya Dawat-e-Islami, omwe aona liwu lirilonse la bukuli ndikupereka maumboni a mabuku oyambilira, kupititsa patsogolo kufunika kwake kwa alaliki achimuna komanso achikazi a Dawat-e-Islami komanso akatswiri olemba, olankhula komanso osindikidza mabuku. جَزَى اللهُ عَنَّا عُلَمَائَنَا اَحْسَنَ الْجَزَاءِ, ndiko kuti, Allah عَزَّوَجَلَّ alipire malipiro abwino kwa akatswiri athuwa.

## Du'a ya Attar

O Allah عَزَّوَجَلَّ! Amene angawerenge *Faizan-e-Sunnat* (volume 1) m'masiku 163, adalitsidwe ndi Imaan yokhazikika, masomphenya a Mtumiki woyela صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم panthawi ya masautso a imfa yake, chitonthozo m'manda mwake ndi pakuuka kwa akufa, chikhululuko popanda kuyankha mlandu chifukwa cha chifundo chanu ndi malo ku Jannat-ul-Firdaus okhala pafupi ndi mneneri wanu wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Mapemphero onsewa ayankhidwe kwa ine, akatswiri, ofufuza ndi onse amene adagwirizana pakumaliza bukuli, kuphatikidza nkulu komanso mamembala a Majlis Maktaba-tul-Madinah, ndi ogwira ntchito onse a Makataba-tul-Madinah. O Allah عَزَّوَجَلَّ, khululukirani Ummah onse.

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

11 Ramadhan-ul-Mubarak, 1427 A.H.

اَلۡحَمۡدُ لِلّٰهِ رَبِّ الۡعٰلَمِيۡنَ وَ الصَّلٰوةُ وَ السَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الۡمُرۡسَلِيۡنَ

اَمَّا بَعۡدُ فَاَعُوۡذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيۡطٰنِ الرَّجِيۡمِ ؕ بِسۡمِ اللّٰهِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِيۡمِ ؕ

# Mphatso yochokela kwa Attar

O Allah عَزَّوَجَلَّ! Landirani kuyesetsa kwanga kophatikiza *Faizan-e-Sunnat* (volume 1) pabwalo lanu ndipo mupereke malipiro ake, osati molingana ndi kulakwa kwanga koma molingana ndi chifundo chanu chosatha. O Allah عَزَّوَجَلَّ, fikitsani malipiro ake kuchokera kwa ine kupita kwa mneneri wanu okondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Kudzera mwa mneneri wanu okondedwa, tumizani mphoto yake kwa aneneri ena onse عَلَيۡهِ السَّلَام, ma Swahabah komanso Tabi'in رَضِىَ اللّٰهُ عَنۡهُمۡ, Aimma-e-Mujtahidin ndi akatswiri onse komanso oyera mtima رَحِمَهُمُ اللّٰه. O Allah عَزَّوَجَلَّ, fikitsani malipiro ake kwa Aimma-e-Mazahib-e-Arba'ah komanso Salasil-e-Arba'ah, makamaka kuphatikidza Sayyidunna Imam A'zam رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه, Sayyiduna Ghaus-e-A'zam رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه, Sayyiduna Mujaddid A'zam Imam Ahmad Raza Khan رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه, Sayyidi-o-Murshiqidi Qutb-e-Madinah Maulana Ziyauddin Madani A'zam رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه, makolo anga olemekezeka Mufti-e-Dawat-e-Islami Al-Haji, Al-Hafiz Muhammad Fruq Al-Attari Al-Madani رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه Bulbul-e-Rauza-e-Rasul Haji Muhammad Mushtaq Attari رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه, abale ndi alongo omwe adamwalira omwe adalumikizana ndi Dawat-e-Islami ndi ma jinn alionse achisilamu komanso anthu onse achisilamu. O Allah عَزَّوَجَلَّ, makamaka fikitsani malipiro ake kwa mlaliki aliyense wamwamuna ndi wamkazi wa Dawat-e-Islami amene amalandira mwayi ophunzitsa maphunziro awiri kuchokera mu Faizan-e-Sunnat tsiku lirilonse kwa masiku osachepera 40.

اٰمِيۡن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

11 Ramadhan-ul-Mubarak, 1427 A.H.

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِیْنَ وَ الصَّلٰوةُ وَ السَّلَامُ عَلٰی سَیِّدِ الْمُرْسَلِیْنَ

اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّیْطٰنِ الرَّجِیْمِ ط بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْمِ ط

# Zolemba za Omasulira

Okondedwa abale achisilamu, Majlis-e-Tarajim ya Dawat-e-Islami, nthambi yomwe ili ndi udindo otsindikidza mabuku akuluakulu ndi mabuku ang'ono ang'ono a Amir-e-Ahl-e-Sunnat yemwe adayambisa Dawat-e-Islami 'Allamah Maulana Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razvi دَامَتْ بَرَکَاتُهُمُ الْعَالِیَه muzinenero zosiyanasiyana zapadziko lapansi, ndiyosangalara kupereka buku la '*Faizan-e-Sunnat*' m'chichewa pa mutu wakuti '*Madalitso a Sunnah.*'

Ngakhale kuti kumasulira kulikonse ndi njira yotanthauzira, tayesetsa momwe tingathere kuti tipeleke lingaliro la olemba mu nzeru zake zenizeni. Kuti tithandidze katchulidwe ka zilembo za Chiarabu, tchati chomasulira chawonjezeredwa. Mawu a malamulo achisilamu sanamasuliridwe ngati chenjedzo chifukwa nthawi zambiri, liwu lachichewa silingalowe m'malo mwa mawu achisilamu. Komabe, mawu apelekedwa kumapeto kwa buku, kufotokoza momveka bwino mawu achisilamu. Kuti zithandize abale ndi alongo omwe azikaphunzitsa kuchoka m'bukuli, waonjezeredwaso mutu wachidule omwe uli ndi ma Hadith makumi anayi (40) onena za ubwino wa Salat-'Alan-Nabi. Kupitilila apo, index komanso zolemba zina zaperekedwaso.

Kumasuliraku kwakwaniritsidwa ndi chisomo cha Allah wamphamvu zonse, chisomo cha Mneneri wake olemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi thandizo la uzimu la Shaykh wathu wamkulu, yemwe adayambitsa Dawat-e-Islami, 'Allamah Maulana Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razvi دَامَتْ بَرَکَاتُهُمُ الْعَالِیَه. Ngati pali cholakwika chilichonse m'bukuli, kukhoza kukhala kulakwa kwa umunthu kumbali ya Majlis yomasulira, osati mbali ya mlembi wa bukhu loyambilira. Choncho ngati mupeza cholakwika chilichonse, tidziwitseni mwa kulemba pa adiresi kapena imelo iyi ndi cholinga cholandira mphotho (sawab).

**Majlis-e-Tarājim (Translation department)**

Alami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah Mahallah Saudagran,

Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

**Phone:** ☎ +92-21-34921389, 90, 91

**Email:** 🖃 translation@dawateislami.net

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَ الصَّلٰوةُ وَ السَّلَامُ عَلٰى سَيِّدِ الْمُرْسَلِيْنَ
اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ ؕ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ ؕ

# MADALITSO A بِسۡمِ اللّٰه

Mtumiki wa anthu onse, Mtendere wa m'mitima ndi m'maganizo mwathu, olowa manja ndi okoma mtima (*Mtendere ndi madalitso a Allah zipite kwa iye*) wanena kuti: "Amene anganifunire ine zabwino kamodzi, Allah adzamuchitira chisoni iyeyo kokwanira kakhumi" *(Swahih Muslim, vol 1, p. 175 Hadith 408)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب　　صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Chilimbikiro chili chosamalizika

Mtumiki wa Madalitso, M'khalapakati wa anthu, (*Mtendere ndi madalitso a Allah zipite kwa iye)* wanena kuti: "Ntchito yofunika iliyonse yomwe ingayambidwe popanda kunena "بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ", ntchito imeneyo idzakhala yosamalizika" *(Ad-Dar-rul-Mansur, vol 1, p. 26)*

## Pitirizanibe kuwerenga بِسۡمِ اللّٰه

Okondedwa abale anga Asilamu! Musanadye chilichonse, kumwa madzi kapena chakumwa chilichonse chovomerezeka, kupereka chakudya kapena madzi kwa ena, kuika zinthu pansi, kunyamula zinthu, kuchapa, kuphika, kusoma Quran, kuwerenga, kuphunzitsa, Kuyenda, kuyendetsa, Kuyima, kukhala pansi, kuyatsa magetsi, kuyatsa nkupamphepo, kuyala kapena kuyalula choyala pakudya, kupinda kapena kutambasula choyala pa kama, kutsekula kapena kutseka shopu, kudzola mafuta kapena zonunkhiritsa, kulalika kapena kuyankhula kwa anthu, poimba Qasweedah, kukongoletsa mmutu ndi nduwira, kuvala nsapato, kutsekula kapena kutseka chitseko, kutanthauza kuti tisanayambe kupanga ntchito iliyonse yovomerezeka, (pomwe

malamulo sadaletse) ndi chinthu cha madalitso poika kukhala chizolowezi kunena "بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم" ndi kupeza madalitso ake.

## Kuteteza zinthu kuchokera ku Majini (ziwanda)

Bwana wathu Safwan mwana wa Sulaym رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه akunena kuti: "Ziwanda zimagwiritsa ntchito zinthu ndi zovala za anthu. Nthawi ina iliyonse pomwe mmodzi wa inu akutenga zovala ndicholinga chofuna kuvala kapena akufuna kuvula ayenera kunena 'بِسْمِ اللّٰه' chifukwa dzina la Allah lidzakhala chotchinga kwa iyeyo. (Kutanthauza kuti chifukwa cha ubwino wa kunena mau oti بِسْمِ اللّٰه, ziwanda sizidzakwanitsa kugwiritsa ntchito zovalazo. *(Luqt-ul-Marjan, p. 98)*

Okondedwa abale anga Achisilamu! Chimodzimodzi monga ponyamula kapena kutula pansi chilichonse, munthu aliyense ayenera kuchipanga kukhala chizolowezi kunena "بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم", munthuyo adzakhala akutetedzedwa kuchokera ku ziwanda zoipa. اِنْ شَآءَ اللّٰه

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Nenani بِسْمِ اللّٰه molondola

Aliyense akamanena "بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم" ali okakamizidwa kuwonesetsa kuti lemba lirilonse likutchulidwa mmalo mwake moyenera m'matchulidwe. Powonjezera apo, ngati palibe chisokonezo chilichonse cha phokoso, ndizofunika kuti mawu a munthu onena amveke mokweza kuti mwini wakeyo amve zomwe akunenazo. Anthu ena amalakwitsa matchulidwe a malembo chifukwa cha kufulumira mkatchulidwe. Izi nzoletsedwa kuchita motere mwadala. Ngati tanthauzo litasintha chifukwa cha katchulidwe ka malembo kosalondola, lidzakhala tchimo kwa ochitayo.

Choncho kwa onse amene amanena molakwitsa chifukwa cha chizolowezi chonena mofulumira, ayenera kukonza katchulidwe komanso kanenedwe kawo. Ngati palibe chifukwa chenicheni chonenera بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم, munthu akhozanso kungonena kuti بِسْمِ اللّٰه

## Chisangalalo Chidapambana

Bwana wathu Jabir mwana wa Abdullah (Allah asangalale naye) wanena kuti: "pamene "بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم" inavumbulitsidwa, mitambo inathamangira cha ku m'mawa, mphepo idasiya kuwomba, m'nyanja mudagwa chisokonezo, zokhala ndi miyendo inayi zinamvetsera mwa tcheru, a satana adagendedwa kuchoka mlengalenga ndipo Allah Wachikwanekwane adati: Ndikulumbirira Ulemelero ndi Ufumu wanga! Ndidzadalitsa chinthu chimene "بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم" idzanenedwapo" *(Ad-Dur-rul-Mansur, vol. 1, p. 26)*

## Madalitso a بِسْمِ اللّٰه

"بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم" ndichigawo cha vesi 30 ya Surah An-Naml (Nyerere) mu gawo 19 la Quran. Komanso ndi vesi lokwanira la Quran lomwe linavumblitsidwa kukhala cholekanitsa pakati pa ma Surah a mu Quran.

## Kumvetsetseka kwa lemba 'Baa' mu بِسْمِ اللّٰه

Allah adavumbulutsa malemba Oyera ndi Mabuku kwa ena mwa Atumiki ake عَلَيْهِمُ السَّلَام. Kuchuluka kwa malemba oyera ndi Mabuku akukwana chikwi ndi mphambu zinayi (104). Mwa malemba ndi Mabukuwa, malemba makumi asanu (50) adavumbulutsidwa kwa Bwana wathu Shith عَلَيْهِ السَّلَام, makumi atatu (30) adavumbulitsidwa kwa Bwana wathu Idris عَلَيْهِ السَّلَام, khumi (10) kwa Bwana wathu Ibrahim عَلَيْهِ السَّلَام. Kupitiriza apo, vumbulutso la Taurat lisanafike, malemba khumi (10) anavumbulitsidwa kwa Bwana wathu Musa عَلَيْهِ السَّلَام. Kuwonjezera apo, mabuku ena akuluakulu okwana anayi anavumbukitsidwa:

1. Taurat yoyera inavumbulitsidwa kwa Bwana wathu Musa (Mose) عَلَيْهِ السَّلَام
2. Buku loyera la Zabur linavumbulitsidwa kwa Bwana wathu Dawud عَلَيْهِ السَّلَام
3. Buku loyera la Injil linavumbulitsidwa kwa Bwana wathu Isa (Yesu) عَلَيْهِ السَّلَام
4. Buku Loyera la Quran linavumbulitsidwa kwa Mtumiki Wolemekezeka Kwambiri Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم *(Al-Ihsan bittartib Sahih Ibn Hibban, vol.1, p. 28) (Hilyat-ul-Auliya, vol. 1, p. 222)*

Za mkati mwa mabuku ndi malemba oyera onsewa zikupezeka mu Quran ndipo chidule cha Quran yonse chikupezeka mu Surah Al-Faatiha. Chidule cha Surah Al-Faatihah chikupezeka mu بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِیۡم pamene chidule cha بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِیۡم chili mkati mwa lemba 'Baa'. Izi zikutitanthauzira kuti 'chilichonse chomwe chilipo, ndizochokera kwa ine (Allah عَزَّوَجَلَّ) wachikwanekwane, ndipo chilichonse chomwe chidzakhalepo, chidzakhala chochokera kwa ine (Allah عَزَّوَجَلَّ) Wachikwanekwane

صَلُّوۡا عَلَی الۡحَبِیۡب　　صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Dzina Lalikulu

Zikunenedwa kuchokera kwa Bwana Wathu Abdullah mwana wa Abbas رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہ kuti Mtsogoleri wa Okhulupirira Bwana wathu Uthman mwana wa Affaan رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہ ***adamufunsa Mtumiki Woyera Muhammad*** صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم za kupambana kwa بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِیۡم. Mtumiki Oyera Muhammad صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم adayankha kuti, "ndi limodzi mwa maina a Allah عَزَّوَجَلَّ ndipo ndiloyandikira ku Dzina lalikulu la Allah عَزَّوَجَلَّ, kuyandikira kwake kufanizira mtundu wakuda wa diso ndi mtundu woyera" *(Al-Mustadrak, vol. 1, p. 738, Hadith 2071)*

## Pemphero lopangidwa potchula Dzina Lalikulu limayankhidwa

Okondedwa abale anga Achisilamu! Pali zabwino zambiri ndi Dzina Lalikulu ndipo Dua yopangidwa imalandiridwa. Bambo olemekezeka wa A'la Hadrat Rais-ul-Mutakallimin, Maulana Naqi Ali Khan (mtendere wochokera kwa Wachifundo ukhale kwa iye) ananena kuti: "Ophunzira ena pa Chipembedzo adanena kuti بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِیۡم ndi Dzina Lalikulu Kwambiri. Olemekezeka Ghaus Shaykh Abdul Qadir Jilani adafotokoza kuti: بِسۡمِ اللّٰہ akawerengedwa ndi kunenedwa pa lilime la munthu odzadzidwa ndi Uzimu zilingati mawu akuti 'khala' amene ali mawu ochokera kwa Mulungu.

Okondedwa Abale anga Achisilamu! Kuti tikhale nawo madalitso m'ntchito zathu zolungama ndi zovomerezeka, tayenera kunena (kuwerenga) بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِیۡم tisadapange ntchitozo. Ngati mukulakalaka kupanga chizolowezi chonena بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡمٰنِ

الرَّحِيْم musadapange ntchito iliyonse yovomerezeka, yendani nthawi zonse ndi Maqafilah a Madani a Dawat-e-Islami Odzadzidwa ndi Sunnah pokhala nawo mgulu la abwenzi odzipereka a Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Pali zitsanzo zambiri komwe zovuta za abale a Chisilamu oyenda ndi Madani Qafilah ku Dawat-e-Islami zidakonzedwa ndi kuthetsedwa potsatira zabwino zopanga Dua mnyengo za Madani Qafilah.

## MPHUNO YOPINDIKA

Iyi ndi nkhani yayifupi yomwe idachitika kwa Msilamu mzathu wa mamuna. Iye adanena kuti "fupa la mphuno yanga lidapindika. Ndidakhala ndikumva kuwawa kwa mutu ndi maso kwa nthawi yaitali. Ndidaganiza zokapanga opareshoni pa chipatala cha Nishtar chimene chili ku Madina-tul-Auliya, Multan. Mwamwayi pa ulendo wanga wopita ku Pakpattan ndinayenda limodzi ndi Qafilah zodzadza ndi Sunnah zaku Madani-Dawat-e-Islami ngati anthu omukonda mtumiki Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.

Ndidali nditamvako kale kuti mapemphero opanga mu nthawi ya Madani Qafilah amayankhidwa, ndiye ndinapempha kwa Allah motere;'O ALLAH potengere zabwino za Dawat-e-Islami Madani Qafilah, ndiwongoleni fupa la mphuno yanga! Patapita masiku wochepa a Madani Qafilah ndinadzadzidwa ndi chisangalaro powona kuti mphuno yanga siidalinso yopindika koma yoongoka ndikukhala bwinobwino chifukwa cha madalitso a Dua yomwe ndidapanga mu nthawi ya Madani Qafilah limodzi ndi anthu omukonda mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

Kufuna kuphunzira Sunnah, yendani ndi Madani Qafilah. Kufuna kupeza chifundo, yendani ndi Madani Qafilah. Kufuna kupeza madalitso, yendani ndi Madani Qafilah. Kufuna kupeza bata la mu mtima yendani ndi Madani Qafilah.

Okondedwa abale anga Asilamu, popanda chikaiko kuti Dua ya munthu wa paulendo imalandiridwa, ndipo Dua yopangidwa ndi wapaulendo amene akuyenda munjira ya Allah pamodzi ndi anthu abwenzi a Mtumiki, ndizachidziwikire kuti yayenera kulandiridwa ndi Allah عَزَّوَجَلَّ.

Pakufotokoza pa zifukwa zomwe zingapangitse Dua kulandiridwa ndi Allah, Bambo olemekezeka wa A'la Hadrat Maulana Naqi Ali عَلَيْهِ السَّلَام wayankhula pa tsamba 57 la buku lake lapamwamba lotchedwa Alisan-Ul-Wia 'pa m'kumano wa Auliya Abwenzi a Allah ndi Ophunzira mozama chipembedzo (kutanthauza kuti Dua yopangidwa

m'mikumano kapena moyandikana ndi woyera mtima aliyense wachisilamu kapena ophunzira chipembedzo mozama wa chi Sunni, Dua imeneyo imayankhidwa.

Powonjezera m'munsi mwake mwa mawuwa A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wanena mawu okhuza ophunzira oyera mtima achisilamu motere; Allah عَزَّوَجَلَّ akuyankhula mu Hadith Qudsi kuti' هُمُ الْقَوْمُ لَايَشْقِيْ بِهِمْ جَلِيْسُهُم Awa ndi anthu amene kukhala nawo pamodzi munthu samasemphana ndi chifuniro cha Allah.

بہتر از صد سالہ طاعت بے رِیا          یک زمانہ صُحبتِ با اَولیاء

Nthawi yimene msilamu angakhale pamodzi ndi anthu olemekezeka omwe ndi abwenzi a Allah ndiyabwino poyerekeza ndi zikwizikwi za zaka zomwe munthu angakhale akupembedza mwachilungamo.

Kaya munthu oyera mtima ali moyo kaya akupuma m'manda mwake, kuyandikira kwake ndi njira imodzi yoti Dua ya munthu ilandiridwe mtsogeleri wa abale athu a Chishafi miyanda miyanda, Bwana wathu Imam Shafi wanena kuti; 'pamene ndikufuna china chake, ndinapemphera ma Rakaa awiri, ndikupita ku manda kwa Imam wamkulu Abu Hanifah ndi kukapanga Dua kumeneko. (Pachifukwa cha ichi) Allah عَزَّوَجَلَّ amakwaniritsa zofuna zanga *(Al-Khayrat-ul Hisan, p. 230)*

## Zozizwitsa za A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه

Izi zikusonyeza kuti pa manda a anthu oyera mitima ma Dua amalandiridwa, kuchonderera kumamveredwa ndipo zofuna zimakwaniritsidwa. Mmawu ake A'la Hadrat wafokoza zimene zidamuchitikira iye ali ndi zaka (21) makumi awiri ndi chimodzi. Wafotokoza kuti pa 17 mwezi wa chinayi mmiyezi yachisilamu mchaka cha 1293 pambuyo pa msamuko wa Mtumiki *(17Rabi'-ul-Akhair)*, Pamene ndinali ndi zaka 21 zakubadwa, ndinachitika mwayi kukayendera manda wodalitsika a oyera mtima wopambana Malibub-e-llahi, Nizam-ul-Haq Waddin, Sultan-ul-Auliya (mtendere wa Allah ukhale kwa iye) pa ulendowu ndinali limodzi ndi olemekezeka bambo anga ndi Shaykh Maulana Muhammad Abdul Qadir Badayuni.

Kunja kwa manda kudali zochitika zina zoyipa komanso zosokoneza. Kudali phokoso lolepheretsa munthu kumva zilizonse. Anthu oyera mtima awiriwa ndi mitima yawo ya

mtendere adalowa m'chipinda cha manda komwe mtumbira wa Sultan-ul-Auliya unali ndipo awiriwa anakhala pa malo awo.

Ine ndinasokonezedwa ndi phokoso la zochitika zoipa ndinayima pakhomo lodalitsika la manda amenewa ndipo ndinachita Dua kunena kuti; 'O, mbuye wanga! phokosoli likutsautsa kapolo wanu pa zolinga zomwe wabwerera kuno' kenako ndinalowetsa phazi langa la kumanja m'chipinda, ndipo chisomo cha Mulungu wapamwamba mwamba phokoso lonse linatherathu. Ndinaganiza kuti anthu onse akhala chete, koma nditatembenuka ndinawona m'chitidwe woyipa uja ukupitilirabe. Pamene ndinatulutsa phazi langa m'chipinda cha manda chija, phokoso lija ndinalimvanso.

Kunena mawu a بِسْمِ اللّٰه, ndinalowetsanso phazi langa la manja m'chipinda cha manda chija. Mwachisomo cha Allah عَزَّوَجَلَّ, phokoso lija sindinalimvenso. Apa ndinazindikira kuti izi zinkachitika chifukwa cha mphamvu ya kuyera mtima ya Mulungu yomwe inaperekedwa kwa Sultan-ul- Auliya ndi chifundo komanso chithandizo kwa kapolo wa Allah wapamwambamwamba.

Pofuna kuyamika, ndinalowa m'chipinda chodalitsika chija ndikupeza malo anga. Nthawi zonse ndinali m'menemo sindinamvemo phokoso lililonse. Nditatuluka ndinasokonezedwa ndi phokoso lija ndiponso zinandivuta kuti ndifike pamalo anga wogona amene adali pataliko kuchokera pa manda wodalirikawa. Ndafotokoza izi zomwe zinandichitikira ndi zolinga zolungama. Choyambirira kunali kuyanjidwa kwanga ndi Mulungu ndipo Mulumgu akunena mkuyanja kwake;'

وَ اَمَّا بِنِعْمَةِ رَبِّكَ فَحَدِّثْ ﴿۱۱﴾

**Ndipo lengeza zabwino zimene Bwana wako wakuchitira**

*(Wakukondera part 30, Surah Ad-Dhuha Vesi 11)*

Mowonjezera, izi zikupereka chiyembekezo kwa onse owakonda anthu oyera mtima ndipo zikupereka mavuto kwa onse okanira. O, Allah kupyolera mwa Okondedwa anu, tipatseni Madalitso opanda malire a Okondedwa anu oyera mtima m'dziko lino, mu nthawi yomwe ili kudza, m'manda komanso patsiku la chiwerudzo. *(Alisan-ul-Wi'a, p. 60)*

Okonedwa abale anga Asilamu! Ili ndi fanizo la Dheli, mzinda wa anthu oyera mtima okwana makumi awiri ndi awiri (22). Nkhaniyi ikukhudza zozizwitsa za oyera mtima Khuwajah Mahbub-e-llahi, Nizamuddin Auliya komanso zozizwitsa za A'la Hadrat. Pamene A'la Hadrat adalowa mchipinda cha mtumbira odalitsika, samamvako phokoso la kuyimba kwa ng'oma kapena zida zina zilizonse zoyimbira.

Taphunziranso kuchokera mufanizo limeneli kuti ngakhale anthu ena osaphunzira amachita m'chitidwe oyipa omwe ndiwotsaloredwa pa malamulo a Chisilamu pa manda a anthu oyera mtima ndipo timalephera kuwaletsa anthuwa, komabe tisamalephere ife eni kukayendera manda odalitsikawa. Koma zili zachikakamizo kupewa mchitidwe onyasa omwe umachitika kunja kwa manda ndipo tizidziwona zimenezi kukhala zonyasa m'mitima mwathu. Ndipo wina aliyense ayenera kupewa kuwonelera zinthu zoterezi.

## Bambo Wokalamba Wodabwitsa ndi Ziwanda Zakuda

Nthawi ina yake ku mzikiti wa mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم (Masjid-un-Nabiwi), Bwana wathu Umar Faruq ndi ena olemekezeka omutsatira Mtumiki Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adali akukambirana za kupambana kwa Quran. Mukukambirana kwawo, Bwana wathu Amr mwana wa Ma'dikarib adayankhula modzichepetsa kuti; O, mtsogoleri wa Okhulupirira! Bwanji simukuyankha za kupambana kwa بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم! Ndikulumbira mwa Allah بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndiyopambana.

Atakhala pansi mowongoka Bwana wathu Umar Fraq رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ adayankha motere: O, Abu Saur! (Uwu udali mfunda wa Bwana wathu Amr Bin Ma'dikarib) chonde tiuzeni kupambana kwake kwa بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم. Bwana wathu Amr Bin Ma'dikarib adayankha kuti;" Njala idagwa nthawi ina yake mu nthawi ya umbuli. Ndikufufuza zakudya ndinadutsa pafupi ndi nkhalango. Chapatali ndinawona hema. Pafupi ndi hema imeneyi panali Kavalo ndi ng'ombe. Pamene ndinayandikira ndinawona kuti mkati mwa hema munali mayi wokongola ndi bambo wachikulire amene adakhala pansi atatsamira chinthu china chake.

Momuwopseza bambo okalambayo ndidati;" ndipatse chilichonse chomwe uli nacho!" Iyeyo adayankha kuti; 'O, bambo! ngati mukufuna chabwino chilichonse kuchokera kwa

ife, bwerani. Ngati mukufuna thandizo, ife tikuthandiza.' Ine ndidati; 'Tasiya kupanga chilichonse ndipo undipatse chilichonse uli nacho.' Bambo okalambayu sankakwanitsa kuyima, ndipo akunena بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم anandigwira ine. Mwa kanthawi kochepa anandiponya pansi ndikundikhalira pachifuwa (panganga) ndi kunena kuti; 'tsopano undiuze, ineyo ndikuphe kapena ndikusiye?' Atamva izi anachoka pachifuwa panga.

Ndinadzidzudzula mumtima mwanga ndipo ndinadziyankhulira ndekha; 'O, Amr! Ndiwe munthu wodziwa kuyendetsa kavalo mu Arabia. Kuthawa chifukwa chogonjetsedwa ndi bambo wofooka komanso okalamba ndichisonyezo cha mantha komanso kachitidwe komwe si kamunthu wamamuna; ndibwino kungophedwa kusiyana ndikuti ukhale onyozeka.' Pachifukwa ichi ndinamuwopsezanso kachiwiri bambo uja, 'ndipatse zonse zimene uli nazo!' Atamva izi bambo wodabwitsayu adandigwiranso akunena بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم. Nthawi yomweyo anandiponya pansi ndikudumphira pachifuwa panga ndikuti; 'Tandiuze, ndikuphe kapena ndikusiye wamoyo?' Ndinayankha, 'chonde mundikhululukire, ndipo anandisiya. Koma kenako ndinabwerezanso kumuwopseza ndikumuwuza kuti andipatse zonse zimene anali nazo.

Atanena بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم, anabwerezanso kundigwira ndikuthetsa mphamvu. Kenako ndinamupemphanso; 'chonde ndisiye' koma anayankha;' Akaka ndikachitatu. Sindikusiya momphweka tsopano! Atanena zimenezi, anayitana, 'O, mtsikana bweretsa lupanga lakuthwa!' mtsikana adabweretsa lupanga limene adagwiritsa ntchito kudula tsitsi lapatsogolo pa mutu wanga, kenako anandisiya.

Chinali chikhalidwe cha Aluya (Arabu) kudula tsitsi la kutsogolo kwa mutu kwa munthu ogonjetsedwa, kufuna kuwonetsa kuti munthu wagonjetsedwa, pa kumenyana (ndeu). Ogonjetsedwayo ankachititsidwa manyazi kukumana ndi apabanja ake kufikira tsitsi la patsogolo pa mutu litameranso. Pachifukwa chimenechi ndikakamidzidwa kugwira ntchito kwa bambo wachilendoyu kwa chaka chonse chatunthu. Chaka chitantha bambo wachilendo ameneyu ananditengera kuchigwa kumene adanena Bismillahir Rahmanir Rahim mokweza mau. Mwadzidzi mbalame zonse zinatuluka mzitsa zawo ndi kuwulukira kutali. Atanenatso بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم nyama zonse zinatuluka momwe zinkabisala ndi kuthawira kutali. Atanenatso بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم kachitatu, chidatulukira chiwanda chachitali kufanana ndi mtengo wa tende chitavala

nsalu ya mapeyala. Nditachiwona chiwanda chimenechi thupi langa linagwidwa ndi mantha.

Bambo wachilendo adandiyankhula nati; 'O, Amr limba mtima. Ngati chiwandachi chitandipambane ine, ungonena kuti mzangayu apambana nthawi yina chifukwa cha بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم. Kenako bambo wachilendoyu ndi chiwanda chija anayamba kulimbana. Bambo wachilendo anagonjetsedwa ndi chiwanda. Pakuwona izi ine ndidati; 'Nthawi yina mzanga adzapambana. (Izi zinali zimilungu za mafano kwa anthu osakhulupirira).

Pakumva izi bambo wachilendo uja anandimenya khofi ku nkhope mwa mphamvu kwambiri kufikira kuti sindinazindikire chomwe chinkachitika kwa ka nthawi ndipo zinakhala ngati mutu wanga wachotsedwa ku thupi langa. Mopepesa ndidamulonjeza kuti sindidzabwerezanso zomwe ndidachita. Awiriwa adayambanso kumenyana. Pa nthawi imeneyi, bambo wachilendo uja adagwetsera chiwanda chakuda chija pansi, ndiye ine ndidakuwa kuti; 'mzanga wapambana chifukwa cha madalitso a بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم.'

Nditangoyankhula mawu amenewa, bambo wachilendo komanso okalamba uja adalowetsa chiwanda chija pansi ngati kachidutswa ka nkhuni, ndikudula motumbula mimba ya chiwanda chija, natulutsa chinthu chonga nyali ndipo anati kwa ine; 'O, Amr! ichi ndi chinyengo komanso kusowa chikhulupiriro.' Ndinamufunsa bambo wachilendo okalamba uja; 'pali nkhani yanji pakati pa iwe ndi chiwanda?' Iye adayankha nati; 'chiwanda chomwe si chachisilamu chidali mzanga. Chaka chilichonse chiwanda chochokera ku gulu limeneli chimabwera kudzamenyana nane ndipo Allah عَزَّوَجَلَّ amandidalitsa ndi chipambano chifukwa cha madalitso a بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم.

Kenako tidayenda nkufika pamalo ena pamene bambo wachilendo komanso okalamba uja adagona. Pakutengera mwayi wa kugona kwake ndinalanda lupanga lija ndikumenya miyendo yake kufikira kuti miyendoyo yidachoka ku thupi lake. Adalira kwambiri; 'O, iwe wachinyengo! mwankhanza wandipusitsa ine!' Bamboyu sindinamupatse mwayikuti achirenso ndipo ndinamumenya mosalekeza ndikumudula mtizidutswa. Nditabwerera ku hema mtsikana uja anandifunsa,'O, Amr! zatha bwanji kumenyana ndi chiwanda?' Ndinamuyankha mtsikana motere,'ziwanda zapha bambo wokalamba uja!' Mtsikanayo adayankha,'ndiwe wabodza Amr! munthu osakhulupirika iwe! Ziwanda sizidamuphe bambo wokalamba uja, koma wamupha ndiwe!' Pambuyo ponena mawu amenewa,

mtsikanayo anayamba kulira mosowa chitonthozo, ndipo anawerenga mau asanu a mawu achi Arabu amene atanthauziridwa motere;

1. O, maso anga! gwetsa misonzi ya bambo wa hachi amene adali wolimba mtima.
2. O, Amr! wayenera kukhudzidwa za wako chifukwa mzako wamwalira.
3. Ndipo (Amr! pambuyo pomupha mzako ndi manja ako) udzaima bwanji ndi mphamvu pamaso pa (mtundu wako) Bani Zubaydah ndi ena osakhulupirira?
4. Ndinakulumbirira zaka zanga! (O, Amr) ukanakhala msilikali weniweni (chikhala kuti udamenyana naye mwachamuna popanda chinyengo) zoona zake nzakuti lupanga lake la kuthwa likadakupha iwe.
5. Ngati nkotheka, mfumu yeniyeni (Allah wachikwanekwane) akupatse iwe (Amr) kubwerera kochititsa manyazi komanso konyansa (chifukwa cha nkhanza zimene wapanga) ndipo ukhale moyo wako wochititsa manyazi ndinso onyasa (mofanana mmene wamupangitsira mzako manyazi)

Nditapsa mtima ndinafutuka kuti ndimuphe mtsikanayu, koma modabwitsa mtsikanayu sadawonekenso mmaso mwanga (adasowa) kukhala ngati kuti dziko lamumeza! *(Luat-ul-Marjan, p. 141)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب          صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Okondedwa abale anga Asilamu mwaona kudabwitsa kwa Madalitso بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم? Pofuna kupeza Madalitso, yendeni ndi Dawat-e-Islami Madani Qafilah pamodzi ndi amene ali omukonda Mtumiki صَلَّى اللّٰه عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Mavuto anu adzathetsedwa modabwitsa. Mudzathandizidwa mobisika m'chisomo komanso ubwino wa Allah عَزَّوَجَلَّ.

## Zolinga zabwino zimafikitsa munthu komwe walingalira

Qafilah ya Madani mwa amene amamukonda Mtumiki صَلَّى اللّٰه عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, adali pa ulendo opita ku Kapadvanj (Gujrat, India). Pa ulendo wawo wa mderali oyitanira anthu ku chiongoko adakumana ndi munthu wakumwa mowa. Mkulimbikira kwa aliyense payekhapayekha, odzipereka a Mtumiki صَلَّى اللّٰه عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anamupempha munthu oledzera uja kuti ayende nawo kupita ku Mzikiti. Munthuyu anachititsidwa chidwi ndi kudekha

komanso kudzichepetsa kwa abale a Chisilamu amene panthawiyi adali atavala nduwira zawo zobiriwira ndipo nthawi yomweyo iye adavomera kuyenda nawo abalewa.

Ndi Madalitso amene adali ndi abale odzipereka a Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, munthu oledzerayu adalapa machimo ake, adasunga ndevu, adakongoletsa mutu wake ndi korona wa nduwira yobiriwira ndipo munthuyu adawapanga maganizo ake kusintha ndi kuyamba kuvala zovala za Madani. Adayenda ndi Qafilah ya Madani kwa masiku asanu ndi limodzi nkupanganso chiganizo choyenda kwa masiku makumi asanu, ndi anayi ndi awiri (92). Koma analibe ndalama zoyendera ulendowu.

Tsiku lina adakumana ndi m'bale wake. M'bale wakeyu anadabwa kuti m'bale wake yemwe anali ovuta mdera la kwawo komanso oledzera, adali atasintha adamuuza m'bale wakeyu kuti pamene adayenda ndi Qafilah ya Madani kunapangitsa kusintha kwa moyo wake ndipo adayika chitsimikizo choyenda kwa masiku 92 ndi Madani Qafilah, koma sakadakwanitsa pa nthawiyi chifukwa adalibe ndalama. M'bale wakeyo adayankha kuti;'usadandaule za ndalama.

Ine ndidzakwanitsa kukupatsa ndalama zoyendera ulendowu komanso ndalama zosamalira banja lako kwa masiku 92. Pa chifukwa chachithandizochi, iye adakwanitsa kuyenda masiku 92.

*Chithandizo cha mseri chidzabwera ndipo khomo lidzalemera.*

*Zindikirani pa umunthu wanu, yendani ndi Madani Qafilah.*

*Yang'anirani ubwino wa Mulungu, yendani ndi Madani Qafilah.*

## Ngale zisanu za Madani

Bwana wathu Abdullah mwana wa Amr mwana wa Aas رَضِیَ اللهُ عَنْهُ, adanena kuti; 'ngati munthu angatenge zizolowezi zisanu adzakhala opatsidwa mwayi mmoyo uno komanso moyo umene uli nkudza.

1. Kuwerenga "لَآ اِلٰهَ اِلَّا اللهُ مُحَمَّدٌ رَّسُوْلُ اللهِ" nthawi zambiri.
2. Kuwerenga "اِنَّا لِلّٰهِ وَ اِنَّآ اِلَيْهِ رٰجِعُوْنَ" ndi "لَاحَوْلَ وَلَا قُوَّةَ اِلَّا بِاللهِ الْعَلِيِّ الْعَظِيْمِ" pamavuto (kutanthauza kuti pamatenda, kutaya zinthu zofunika komanso ngati zilizonse zovuta)

3. kuwerenga "اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ" poyamikira kapena kupeza ubwino.
4. kuwerenga "بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ" musanayambe kupanga ntchito iiyonse yovomerezeka.
5. Kuwerenga "اَسْتَغْفِرُ اللّٰهَ الْعَظِيْمَ وَاَتُوْبُ اِلَيْهِ" pamene papangidwa machimo. *(Al- Munabbihat, p. 58)*

## Kuchita zabwino kufanane ndi udindo wa munthu (chopereka chigwirizane ndi opereka)

Mfotokozeri komanso mtanthauziri odziwika bwino pa Mahadith ndi Quran, Mufti Ahmad Yar Khan adanena kuti;'Mu بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ, Allah watchulamo zikhumbo zake ziwiri za رَحْمٰن ndi رَحِيْم Dzina lake (Allah) chifukwa dzina lake (Allah) liri lopatsa chidwi pa mphamvu ndi ulemerero pamene رَحْمٰن ndi رَحِيْم muli chisoni.

Pamene anthu adamva dzina loti Allah ngakhale ochita zabwino pa chipembedzo sadapeze mphamvu kufunsa chilichonse koma pamene adamva maina رَحْمٰن ndi رَحِيْم, ochimwa ndi olakwa nawo analimbikitsidwa kumupempha Allah. Ndizinthu zoona ndithu kuti palibe amene angayankhule ngakhale liwu limodzi pa nthawi ya m'kwiyo wa Allah Azziwajalla koma pa nthawi ya chisoni chake aliyense amatha kusangalala. Mogwirizana ndi zimenezi pali nkhani ina yopatsa chidwi yomwe yatchulidwa mu Tafsir Kabir. Tsiku lina opempha adafika pa chitseko chokongoletsedwa mwa pamwamba cha nyumba ya munthu olemera kwambiri napempha chinachake koma anapatsidwa chinthu chotsika mtengo komanso chosafunikira. Wopempha uja anatenga zopatsidwazo nkupita.

Tsiku lotsatira opempha uja adabweranso ndi chida chokumbira m'manja ndipo anayamba kukumba pansi pa chitseko. Mwininyumba atawona izi adakuwa, 'ukupanga chiyani?' Opempha adayankha 'Uyenera kupereka chopereka mofanana ndi kukongola kwa chitseko chako kapena uchipange chitseko chako mofanana ndi chopereka chimene wapereka.' Zomwe zikutanthauza kuti popeza wakongoletsa chitseko chako kufuna kuwonetsa kuti ndiwe munthu wolemera, ndizofunikanso kwa iwe kuti udzipereka chopereka chambiri poyerekeza ndi anthu ena. Ife wopempha ochimwa nafenso

timapempha Allah, ‘O, Allah, tidalitseni ndi zabwino osati mofanana ndi kufunikira kwathu koma potengera kupereka ndi kukoma mtima kwanu. Popanda chikaiko ife ndife ochimwa koma ndi chikhumbokhumbo chanu cha chikhululuko chili chachikulu kuposa machimo athu.’ *(Tafsir-e-Na’imi, p. 40, part 1)*

*Ngakhale palibe muyezo wa machimo wa kapolo uyu ’O, inu okhululuka kwa okhululuka onse, chikhululuko chanu chilibe muyezo.’*

Okondedwa abale Achisilamu, Ndithudi Allah ndi رَحْـمٰن (wachifundo) komanso رَحِيْم (wachisoni). Amene waika chiyembekezo chake pa chisoni cha Allah nkumayembekeza zabwino kuchoa kwa Allah, nzosatheka kuti iye amanidwe chisoni cha Allah عَزَّوَجَلَّ ndipo adzakhala opambana m’moyo uno komanso moyo ukubwerawo.

## FANIZO LA CHISONI

Zanenedwa pa tsamba 38 mgawo loyamba la Tafsir Na’imi kuti padali abale awiri, mmodzi wa awiriwa adali ochita ntchito zabwino za chipembedzo pamene winayo adali ochita za uchimo. Pamene m’bale ochimwayu adatsala pang’ono kumwalira, m’bale wake ochita zabwino adati kwa iye; ’Tawona, nthawi zonse ndimakulangiza ndi kukudzudzula, koma sudasiye machimo. Ndiuze chomwe chikuchitikire tsopano.’ M’bale ochimwa adayankha nati; ’Ngati Allah adzalore amayi anga patsiku la chiwerudzo kuti adzapange chiganizo cha moyo wanga, amayi angawo angadzanditumize kuti? ku Paradiso kapena ku Gahena?’ M’bale wopanga ntchito zabwino adayankha; ’Nchachidziwikire kuti amayi adzakupititsa ku Paradiso.’ M’bale wochimwa naye adayankhanso’ Mulungu wanga ndiwachisoni choposa cha amayi anga. ’Pambuyo ponena mawuwa iye adamwalira.

M’bale opanga zabwino uja adalota usiku m’chimwene wake omwalira uja ali wamtendere komanso wofewa, ndipo adafunsa chifukwa chachikhululuko chake. M’bale omwalira uja adayankha, ’Mawu omwe aja amene ndidayankhula nthawi yomwe ndinkamwalira ndi amene abweretsa chikhululuko cha machimo anga onse!’

Timupemphe Allah عَزَّوَجَلَّ kuti awachitire chisoni ndikuwakhululukira popanda kusunga mulandu Pa zifukwa zawo.

Kwa ife ochimwa odzichepetsa, kukondera kwanu nkofunika, machimo onse adzatsukidwa, mvula ya Chisoni ndi yomwe tikufuna.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Okondedwa abale anga Asilamu! ndithudi chisoni cha Allah Ndi chachikulu. Ngakhale mawu amodzi woyankhulidwa ndi munthu ndiwokwanira kwa munthu kukhululukidwa kapena kulangidwa. Monga zanenedwa mufanizo limene lapitali, chiganizo chimodzi chidali chokwanira kukhululukidwa munthu wochimwa.

Zili chimodzimodzi ngati munthu angayankhule poyera mawu amene ndiwopanda chikhulupiriro (okanira) ndipo munthuyo ndikumwalira asadalape, adzakhala akulandira chilango cha muyaya ku Gahena.

Njira yopambana kwambiri kuti munthu adziteteze kuchokera ku chilango ndi kupeza chikhululuko ndiyo kuyenda limodzi ndi anthu odzipereka kwa Mtumiki ndi ma Qafilah odzadzidwa ndi Sunnah a Madani, Dawat-e-Islami, gulu lomwe silipanga za ndale koma la chipembedzo potsatira Quran ndi Sunnah. Ngakhale munthu amene wayika chitsimikizo choyenda mu njira ya Allah عَزَّوَجَلَّ koma akulephera pa zifukwa zina, iyeyo adzapezabe madalitso ake mogwirizana ndi chitsimikizo chake. Tamvetserani fanizo lolimbikitsa chikhulupiliro la munthu wamwayi amene adapanga chitsimikizo choyenda ndi Madani Qafilah.

## LENDE M'MUNDA

Chifukwa cha kukhutitsidwa ndikufikiridwa mdera lawo ndi anthu oitanira kuchiongoko makamaka mdera la Hyderabad (Sindh-Pakistan) mnyamata wa nyengo zino adapita ku Mzikiti komwe adakamvetsera ulaliki odzadzidwa ndi Sunnah ndipo mu nthawiyi, onse amene adatenga nawo mbali adalimbikitsidwa kuyenda ndi Madani Qafilah. Mnyamatayu adawonetsa kufunikira koti ayende nawo a Madani Qafilah kotero adalembetsa dzina lake.

Patatsala masiku ochepa kuti anyamuke ndi Madani Qafilah iyeyo adamwalira. Munthu mmodzi ochokera ku banja lakwawo la munthuyu adalotamunthu omwalirayu akusangalala atakwera lende m'munda wa zomera zoboriwira. Munthu olotayu adafunsa, 'kodi zidatheka bwanji kuti iwe ubwere kuno?' iye adayankha,'ndidafika kuno ndi Madani Qafilah ya Dawat-e-Islami! Allah wandidalitsa ine kwambiri. Chonde

mukawauze amayi anga kuti asandidandaule popeza kumene ndili kuno moyo ndiwofewa.'

*Polowa ku Paradiso ndi ulemerero, tidzakhala tikuyimba chiphiphiritso Yaa Rasulallah.*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب    صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Pa malamulo a Chisilamu, loto la munthu amene Sali Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم silimakhala umboni. Choncho tiyenera kukhala ndi chiyembekedzo pa Chisoni cha Allah عَزَّوَجَلَّ komanso tikhale owopa lingaliro la Allah la mseri pa ife. Zonsezi zikudalira chifuniro cha Allah. M'chifuniro chake angathe kulanga munthu ngakale munthuyo atapanaga tchimo limodzi, ndipo mchifuniro chake, angathe kuika Chisomo chake kwa munthu chifukwa cha ntchito imodzi yabwino. Akhoza kumukhululukira munthu pa chifukwa cha Chisoni chake kapenanso Chisomo chake. Allah wachisoni chambiri akunena mu gawo 24, SurahA2-Zumar, vesi ya 53.'

قُلْ يٰعِبَادِيَ الَّذِيْنَ اَسْرَفُوْا عَلٰٓى اَنْفُسِهِمْ

لَا تَقْنَطُوْا مِنْ رَّحْمَةِ اللّٰهِ ؕ اِنَّ اللّٰهَ يَغْفِرُ الذُّنُوْبَ جَمِيْعًا ؕ اِنَّهٗ هُوَ الْغَفُوْرُ الرَّحِيْمُ ﴿۵۳﴾

**Nena, O akapolo anga amene mwadzichitira chinyengo nokha! musataye mtima ndi chifundo cha Mulungu. Ndithu, Mulungu amakhululuka machimo onse. Ndithu iye ngokhululuka kwambiri, wachisoni.'**

*(Kanz-ul-Imani, kumasulira Quran)*

Nkhani ikubwerayi ikukambidwa mu buku la Bukhari, Buku lodalirika kwambiri pa mabuku onse a Mahadith.

## MUNTHU WAKUPHA ANTHU 100 ADAKHULULUKIDWA

Munthu ochokera ku mtundu wa ana a Israel adapha anthu 99. Iye adapita kwa m'busa wachikhristu ndi kumufunsa, 'kodi pali njira ina iliyonse yoti ine ndingalape? Ndine munthu ochimwa kwambiri?' Mayankhidwe a M'busa adamukhumudwitsa ndipo munthuyo adaphanso M'busayo koma adakhumudwa kwambiri nawayendera anthu ena osiyanasiyana kuti apeze njira yakuti alape machimo ake. Pamapeto pake adauzidwa ndi munthu wina kuti apite mu mzinda (kumene akapeze thandizo kwa Wali wa Allah)

choncho adanyamuka pa ulendo wake kupita ku mzinda kuja koma panjira, munthu wakuphayu adadwala. Atatsala pang'ono kumwalira, adalozetsa chidali chake ku mzinda umene ankapitawu kenako adamwalira.

Panthawi yochotsa mzimu wake padabuka kusemphana pakati pa Angelo achisoni ndi Angelo a chilango. Allah adalamula mbali ya dziko (mtunda) wa pakati pa munthu wakufayu ndi mzinda omwe ankapita kuti uchepe mulitali mwake ndicholinga chakuti mzindawu ndi munthu wakufayu ziyandikane. Allah adalamulanso mbali ya dziko ya pakati pamalo omwe wakufayu adachokera ndi malo omwe munthuyu adafera kuti malowa atalike mtunda wake. Ndipo Allah عَزَّوَجَلَّ adalamura kuti mtunda wa malo awiriwa uyezedwe.

Mitundayi itayezedwa, munthu wakufayu adapezeka kuti mitunda iwiriyi idasiyana ndi dzanja limodzi, mtunda wopita ku mzinda kukhala woyandikira ndi munthu wakufa kusonyeza kuti Allah عَزَّوَجَلَّ adamukhululukira munthuyu *(Sahih Bukhani, vol. 2, p. 466, Hadith 3470)*

Allah عَزَّوَجَلَّ amuchtitire chisoni ndikumukhululukira popanda kusiya milandu pachifukwa chake.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Okondedwa abale a Chisilamu momveka bwino kuchokera ku fanizo lomwe lakambidwa ndi chinthu chabwino kwambiri kuwayendera ma Auliya a Allah عَزَّوَجَلَّ ndikupanga mizinda yawo kukhala masomphenya a mitima yathu ndi kulemekeza. Sangalalani ndi chisoni cha Allah عَزَّوَجَلَّ amene adakhululukira munthu wakupha anthu 100 chifukwa cha Chisoni chake. Ngati Allah عَزَّوَجَلَّ akupereka Chisoni chake kwa wachinyamata wamwayi amene adatsimikidza kuyenda ndi Madani Qafilah odzadzidwa ndi Sunnah pamodzi ndi gulu lodzipereka la Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, ndiye kuti izinso zikusonyeza Chisoni chake chachikulu. Ndithu Allah ndi wamphamvu zonse.

Ndi ganizo langa kuti munthu akhale nthawi zonse ochita zinthu ndi Dawat-e-Islami, In Shaa Allah mmoyo uno komanso mmoyo ukubwerawu. Mawu okha sangalongolosole Madalitso a Madani okhudza Dawat-e-Islami! Ndithudi kukhala ndi odzipereka a Mtumiki, kumabereka zipatso. Madalitso samangopereka mmoyo uno okha, komanso pamene munthu wamwalira. Nthawi zina odzipereka kwa Mtumiki amapezedwa ndi imfa mu njira yosilirika. Iyi ndi nkhani yomwe ikufotokoza za kumwalira kosilirika.

## KUMWALIRA KOSILIRIKA

Muhammad Wasim Attari wochokera ku North Karachi, Bab-ul-Madani adali akufika ku Sag-e-Madanali. Iyeyu adavutika ndi matenda a khansa pa mkono wake, mavuto amene adapangitsa kuti iye adulidwe dzanja. M'bale wathu wa Chisilamu ochokera mdera lomweli adalongosola motere, 'M'bale Wasim adali mu ululu waukulu. Ndidapita kukamuwona m'chipatala ndipo ndidamuyankhula momutonthoza motere, O iwe okonda Mtumiki! Usadandaule za kudulidwa dzanja lako lakumazere, popeza dzanja lako la manja liri lotetezeka ndipo mwayi waukulu kwambiri ndiwakuti chikhulupiriro chakonso chili chotetezeka' اِنْ شَآءَاللّٰه. Nditayankhula zimenezi, mzangayo ndinamuona kudekha kwambiri. Anangokhala akumwetulira. Mzangayu anadzuka pabedi lake, kutuluka panja kumandiperekeza.

Pang'onopang'ono, kuwawa kwa mkono wake kunayamba kuchepa koma vuto linali kumuyembekeza. Madzi anadzadza mmapapo ake, zomwe zinamupangitsa iye kukhala ndi ululu waukulu kwambiri. Vuto lakeli lidali likukulabe masiku kamadutsa. Kufikira kuti tsiku lina ululuwu udapambanira, ndipo iye adayamba kupanga Dhikr. Chipinda chomwe adali chidadzadzidwa ndi mawu a Dhikr. Pa nthawiyi umoyo wake udafika povuta kwambiri ndipo adaudzidwa kuti amutengere ku chipatala koma iye adakana. Agogo ake akuchimuna adamukumbatira iye mwachikondi. Iye mwini adanena Kalimah Tayyibah لَآ اِلٰهَ اِلَّا اللهُ مُحَمَّدٌ رَّسُوْلُ اللهِ ndipo mzimu wa Muhammad Wasim Attari, mnyamata wa zaka 22 udatuluka mthupi mwake اِنَّا لِلّٰهِ وَ اِنَّآ اِلَيْهِ رٰجِعُوْنَ

Pamene mtembo wa malemuyu unatengedwa kupita kosambitsidwa, nsalu yomwe inaphimba nkhope yake inatsekuka ndikuwonetsa nkhope yake yowala ngati duwa. Pambuyo pakusambitsidwa mtembo wake, nkhope yake idawala koposa, idawoneka bwino komanso monyezimira. Pambuyo pakuika mmanda mtembo wake, Akukonda a Mtumiki anali akuimba Naat ndipopa nthawiyi kafungo konunkhira kuchokera ku mtumbira wa malemuyu kadakuta aliyense amene adali pa malowa. Mmodzi wa akubanja kwa malemu Muhammad Wasim Attari adalota kuti malemuyu adali mchipinda chomwe chidakongoletsedwa ndi maluwa. Munthu olotayu adafunsa nati, 'kodi iwe Muhammad Wasim ukukhala kuti?' Malemuyu adaloza chipinda kwinaku akuyankha, 'Awa ndi malo anga ndipo ndili osangalala kuno.' Kenako adamuona atatsamira kama (bedi) lokongola.

Bambo ake a Muhammad Wasim nawo adalotanso nawo, kuti adali pafupi ndi mtumbira wa mwana wawo, Muhammad Wasim Attari. Mwadzidzi, mtumbira uja unatsekuka ndipo malemuyu anatuluka mmanda ake atavala nduwira yake yokongola yobiriwira komanso ali mu nsalu yake ya bafuta pathupi lake. Anthuwa adayankhulana nthawi yochepa. Kenako malemuyu analowanso mu dzenje la manda ndi kutsekedwa.

Allah عَزَّوَجَلَّ akhale ndi Chisoni pa iye (Muhammad Wasim Attari) ndipo atikhululukire ife popanda kutisungira mlandu kudzera mwa iye.

O, Allah! Mundikhululukire ine, omwalirayu komanso onse otsatira Mtumiki wathu okondedwa ndi odalitsika Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Mutidalitse ife tonse ndi chikhazikiko ku malo a Madani a Dawat-e-Islami komanso pokhalanso ndi mwayi opanga Dhikr ndi kumanena Salat-Alan-Nabi صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم komanso kumanena Kalimah Tayyibah pa nthawi ya kumwalira kwathu.

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

Pangani mazanamazana a maduwa a chikhululuko changa popeza ndine ochimwa. Werenga (imbani) Naat ya Mtumiki wanga okondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم (Muhammad) pamene mukundigoneka mmanda, O m'bale wanga.

## Malipiro Amakhala Wodziwikiratu Ngakhale Anthu Ena Atasiya Kumvera Malangizo

Ngakhale munthu asamve zomwe tikulalikira kwa iye ife tidzapatsidwabe malipiro athu pa ntchito yathu yolalikira kuti munthuyo akhale olungama. Hujjat-ul-Islami Suyyiduna Imam Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wanena mu buku la Mukashaf-ul-Qulub, Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام nthawi ina adafunsa kwa Allah عَزَّوَجَلَّ modekha, 'Ndi malipiro otani amene angapeze munthu amene wamuitanira m'bale wake ndi kumulamulira kukhala olungama komanso kumuletsa kuchita ntchito za uchimo?' Allah عَزَّوَجَلَّ adayankha kuti, 'Mawu aliwonse amene iye (oyitanira) anganene, ndimamulembera malipiro ofanana ndi kupembedza kwa chaka chimodzi ndipo ndili wamanyazi kumupatsa chilango ku moto munthu olera (oyitanirayo). *(Mukashafa-tul-Qulub, p. 48)*

## Ndizabwino Kuposa Ufumu Wa Dziko Lonse

Munthu wina aliyense atalimbikitsidwa kuti azipemphera komanso ndikutsatira njira ya

Sunnah chifukwa cha kulimbikitsidwa ndi mmodzi wa inu, ndiye kuti inuyo mudzalandiranso malipiro anu pa ntchito yomwe mwagwira. Mtumiki wathu oyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adanena kuti,'Ngati Allah عَزَّوَجَلَّ atadalitsa mmodzi wa inu ndi chiongoko chowonadi pogwiritsa ntchito mmodzi wa inu, izi zili zabwino kuposa ufumu wa dziko lonse la pansi kwa inu.' *(Al-Jami'-us-Saghir, p. 444, Hadith 7219)*

## Chiphe Kusandulika Kukhala (Chosawopsa) Chosapereka Mavuto

Anthu ena opembedza moto adamufunsa Suyyiduna Khalid Bin Walid kuti awawonetse chizindikiro chosonyeza kuti Chisilamu chili choonadi kwa iwo ngati umboni. Khalid Bin Walid adaitanitsa chiphe. Chiphe chitafika iye (Khalid Bin Walid) adanena بِسۡمِ اللّٰهِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِيۡم ndi kumwa chiphecho. Chifukwa cha madalitso a بِسۡمِ اللّٰهِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِيۡم, chiphe chija sichidamuwonetse mavuto aliwonse Sayyiduna Khalid Bin Walid. Opembedza moto aja atawona zimenezi, aliyense payekhapayekha adavomereza kuti Chisilamu ndi chipembedzo chowonadi kwambiri. *(Tafsir Kabir, vol. 1, p. 155)*

صَلُّوۡا عَلَى الۡحَبِيۡب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Okondedwa abale anga Achisilamu! mu fanizo limene lanenedwali zawonetsa kuti kunena بِسۡمِ اللّٰهِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِيۡم usanadye kapena kumwa chili chonse, munthu amatetedzedwa ku zowopseza moyo wake zimene zimapezeka mu chakudya kapena chakumwa powonjezera kukapeza zabwino zazikulu mmoyo umene uli nkudza.

Nkhani iyi yokhudza chiphe kulephera kuwononga moyo wa Sayyiduna Khalid Bin Walid رَضِيَ اللّٰهُ عَنۡهُ ikupezekanso mu mabuku ena mosiyaniranako pang'ono chabe. Ndizothekanso kuti chozizwitsa cha uzimu chimenechi chidachitika kangapo osati kamodzi kokha.

## CHIPHE CHOWOPSA

Pamene Suyyiduna Khalid Bin Walid رَضِيَ اللّٰهُ عَنۡهُ ndi gulu la asilikali ake adali pa malo otchedwa Hira, otsatira ake adati; 'Tili ndi mantha kuti anthu awa amene sia mtundu wa chiArabu (Ajami) akhoza kukupatsa chiphe ndiye chonde ukhale osamala 'Khalid Bin Walid رَضِيَ اللّٰهُ عَنۡهُ adayankha motere; 'Ndione kuti chiphe chimenechi cha anthu amenewa ndi chowopsa bwanji. Ndipatseni chiphecho. Otsatira adachita monga mmene

adawauzira. Atawerenga بِسْمِ اللّٰه, Sayyiduna Khalid Bin Walid adamwa chiphecho koma sadakhudzike ndi kuwopsa kwa chiphecho. Potengera ndi zoyankhula za Kalbi, akunena kuti padali munthu wina amene ndi M'busa, dzina lake Abdul Masih. Munthuyu adali ndi chiphe chowopsa chomwe munthu aliyense akamwa, munyengo yokwana ola limodzi munthu wakumwayo adayenera kufa.

Sayyiduna Khalid Bin Walid رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ atauzidwa za zimenezi adaitanitsa chiphe chimenechi. M'busa uja adabweretsa ndipo Sayyiduna Khalid Bin Walid adamwa pamaso pa M'busa uja kwinaku akuwerenga " بِسْمِ اللّٰهِ وَ بِاللّٰهِ رَبِّ الْاَرْضِ وَالسَّمَاءِ بِسْمِ اللّٰهِ الَّذِیْ لَايَضُرُّ مَعَ اسْمِهِ دَاءٌ". Abdul Masih atawona zimenezi adawayankhula anthu ake amvekere;'O, anthu anga, mukudabwitsika kwanga kwakukulu, Khalid Bin Walid ali wamoyo ngakhale wamwa chiphe chowopsachi. Ndizoyenera kwa ife kuti anthuwa tigwirizane nawo, ndipo ngati sititero ndiye kuti anthuwa atigonjetsa ife.'

Izi zidachitika mu ulamuliro wa Sayyiduna Abub Bakr Siddiq رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ *(Ḥujjatullāĥi-'alal-'Ālamīn, p. 617)*

Allah عَزَّوَجَلَّ awachitire chisoni ndi kutikhululukira ife popanda kutisungira mangawa pachifukwa cha iwo!

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب صَلَّی اللّٰهُ عَلٰی مُحَمَّد

Okondedwa abale anga Achisilamu kodi mwaona ubwino umene Allah عَزَّوَجَلَّ adapereka kwa Sayyiduna Khalid Bin Walid رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ? Izi zidali zozizwitsa zochoka kwa Allah عَزَّوَجَلَّ kumupatsa Sayyiduna Khalid Bin Walid رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ pomwe chiphe sichidakwanitse kuwononga moyo wake. Pali zozizwitsa zosawerengeka zopangidwa ndi anthu oyera mtima zomwe zidali chitetezo chawo ku zinthu zowopsa pa miyoyo yawo. Pakhala pali zitsanzo zingapo zokhudza chiphe ndi zinthu zina zomwe zidakanika kupereka mavuto kwa Auliya a Allah عَزَّوَجَلَّ.

## MOTO KAPENA MUNDA?

Nthawi inayake mfumu yosokonekera idagwira munthu oyera mtima ndi anthu ake omutsatira ndipo mfumuyi idawayankhula anthuwa ndi mawu a chiopsezo ponena kuti; 'Undiwonetse zozizwitsa ndipo ngati sutero iwe ndi okutsatira ako onse ndikuphani.'

Munthu oyera mtimayu adaloza ndowe ya ngamila nayankhula kuti; ’Bweretsani ndipo muwone kuti ndi chiyani.’ Pamene ndoweyo inabweretsedwa idasintha kusanduka kukhala golide weniweni.

Kenako adanyamula kambale kopanda kanthu kalikonse mkati mwake, adakazunguza kambaleko ndi kukalozetsa pansi, kenako adaipatsa mfumu ija kambaleko. Pa nthawiyi kadapezeka kambaleko kali kodzadza ndi madzi ngakhale kuti kadali kozolikitsa pansi, ndipo ngakhale dontho la madzi silidagwe kuchokera mkambaleka. Ngakhale mfumuyi adawona zinthu zozizwitsa ziwirizi, mfumuyi idati; ’zonse zomwe zachitikazi ndi ufiti komanso matsenga!’ kenako mfumuyo idalamura kuti moto ukoledzedwe. Pamene Malawi a moto adakolera m'mwamba, munthu oyera mtima uja ndi anthu ake adadumphira pa motowo, kwinako atatenga mwana wam’muna wachichepere wa mfumuyo. Pamene mfumu idawona mwana wake wagwera pa moto paja, adakhala ndi nkhawa. Patapita kanthawi, mwana wa mfumu uja adabwezeredwa pa miyendo ya mfumu ija mu dzanja limodzi la mwanayo mudali chipatso cha apulo (apple) pomwe mu dzanja linalo mudali chipatso makangaza. Mfumu ija idafunsa; ‘mwana wanga kodi udali kuti?’ Mwana wake wammuna uja adayankha nati; ‘Ndinali m’munda.’ Atawona izi, ogwira ntchito kunyumba ya mfumu osokonekerayu adayankhula nati; ‘izi zonse nzopanda pake komanso ndi zamatsenga.’ Mfumuyo kenako idamuuza munthu oyera mtima uja kuti; ‘Ngati ungamwe chikho cha chiphe ichi, ndidzakukhulupilira.’ Oyera mtima olemekezekayu adamwa chiphechi mosalekeza koma sadawone mavuto ena aliwonse. Chiphechi chidangopangitsa kuti zovala za oyera mtimayu zing’ambike. *(Ḥujjatullāĥi-‘alal-‘Ālamīn, p. 617)*

Allah Azzawajala awachitire chisoni anthu amenewa ndipo atikhulukire ife tonse popanda kutisungira mangawa pachifukwa cha anthuwa. Zingatheke bwanji kuthimitsa nyale yoyatsidwa ndi iye Allah عَزَّوَجَلَّ mwini?

Mphepo imakhalanso chitetedzo cha nyale imeneyi. Okondedwa abale Achisilamu! Mopanda chikaiko, ukulu wa anthu oyera mtima a Chisilamu ndi zozizwitsa zawo sitingakwanitse kuziyankhula mmawu athu. Kuwakonda anthu oyera mtima amenewa ndiye ntchito imodzi yofunika kwambiri ku Dawat-e-Islami limene ndi bungwe losaimira za ndale koma zachipembedzo padziko lonse lapansi potsatira Quran ndi Sunnah. Onse amene ali okhudzana ndi Dawat-e-Islami ali odala ndi chisomo cha Allah عَزَّوَجَلَّ zomwe zimapangitsa ena kukhala odabwitsidwa.

## NGOZI YODABWITSA

Pa 26 Rabi-un-Nur 1420 A.H (11 Julaye chaka cha 1999) Mlaliki wina wa Dawat-e-Islami, Muhammad Munir Husayn Attari رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه (okhala ku Islampur) adagundidwa ndi galimoto napezeka pansi pagalimotoli nthawi yamasana mu msewu wa Lala Musa, mu mzinda wotchuka wa Panjab, Pakistan.

Ngoziyi inali yomvetsa chisoni koopsa kufikira kuti gawo la thupi lake linaduka kukhala chigawo chakumtunda ndi chigawo chakumusi cha thupi la munthu zili zogawikana, komabe munthuyu pa nthawiyi zidali zodabwitsa kuti adali wamoyo komanso ozindikira mokwanira pomwe ankakwanitsa kuwerenga mosalekeza اَلصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلَيْكَ يَا رَسُوْلَ اللّٰه komanso لَآ اِلٰهَ اِلَّا اللّٰهُ مُحَمَّدٌ رَّسُوْلُ اللّٰه ndipo ankawerenga mokweza mawu. Pamene madotolo adakaika za iye kukhala moyo, adatengedwa kupita naye ku chipatala cha Azizi Bhatti mu mzinda wa Gujrat.

M'bale wathu wa Chisilamu amene adamutengera Muhammad Munir Husayn Attari رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ku chipatala adalumbira kuti odwalayu adapitirizabe kuwerenga Salat-Alan-Nabi صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم komanso Kalimah Tayyibah nthawi yonse adali munjira yopita kuchipatala. Pamene madotolo adawona zochitika za Madani zimenezi, nawonso anadabwa powona odwalayu ali ndi moyo komanso ozindikira kuwerenga mosalekeza Kalimah Tayyibah komanso Salat-Alan-Nabi. Iwo adayankhula kunena kuti; 'sitidawonepo munthu olimba mtima komanso odabwitsa ngati ameneyu! 'Patapita nthawi pang'ono, Muhammad Munir Husayn Attari, kakonda wamwayi wa mtumiki, adapempha m'bwalo la mtumiki motere!

*Ya Rasulallah chonde bwerani!*
*Ya Rasulallah chonde ndithandizeni*
*Ya Rasulallah chonde ndikhululukireni*

Pambuyo pa zimenezi, iye adawerenga لَآ اِلٰهَ اِلَّا اللّٰهُ مُحَمَّدٌ رَّسُوْلُ اللّٰه

Ndipo mzimu wake udachoka ndi kumudalitsa iyi kukhala Malitiri. Potengera malamulo Achisilamu, munthu omwalira pangozi amakhala Mmalitiri. Allah عَزَّوَجَلَّ amuchitire chisoni ndi kutikhululukira ife tonse popanda kusiya mangawa pachifukwa cha iye.

## Kuwadzutsa Asilamu Ku Mapemphero A Fajr Ndi Sunnah

Okondedwa abale anga a Chisilamu! Nkhaniyi idasindikizidwa m'manyuzipepala ambiri pa nthawiyo. Mmalitiri wa Dawat-e-Islami, Muhammad Munir Husayn Attari رَحْمَةُ اللّٰه عَلَيْه adali mlaliki osamalitsa ntchito yake mu Dawat-e-Islami ndipo pa nthawiyi adali atangobwelera kuchokera ku Madani Qafilah yodzadza ndi Sunnah yokhudza anthu okonda a Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم yomwe idachitika tsiku limodzi la mmbuyo mwa ngozi yake. Malemuyu adali kuchita Sada-e-Madina tsiku lirilonse. Muchikhalidwe cha Dawat-e-Islami, kuwadzutsa Asilamu ku pemphero la Fajr kumatchedwa kuti Sada-e-Madinah. A chibale osawerengeka Achisilamu omwe ali ndi mwayi amatha kutsatira Sunnah imeneyi. Kuwadzutsa Asilamu ku pemphero la Fajr ndi Sunnah popanda chikaiko kuchokera mmawu awa.

Sayyiduna Abu Bakrah رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ (amene adali otsatira wa mtumiki kuchokera ku mtundu wa Bani Saqif) adanena kuti; 'ndidapita ku pemphero la Fajr pamodzi ndi Mtumiki okondedwa ndi odalitsika. Akamadutsa munthu amene akugona adali kumuitanira ku pemphero kapenanso kumudzutsa ndi phazi lake.' *(Sunan Abi Dawud, vol. 2, p. 33, Hadith 1264)*

## Ndi Ndani Angadzutse Anzake Ndi Phazi

Abale amwayi amene amachita Sada-e- Madina amapeza ubwino wakugwira ntchito ya Sunnah. Kumbukirani! Siyense ali ololedwa kudzutsa munthu ogona ndi phazi. Yekhayo amene ali ogwira ntchito yabwino komanso wachikulire mu msinkhu ndi amene angadzutse munthu ogona ndi phazi popeza ogonayo sanganyasidwe nazo kutero. Komabe, palibe chowopsa kumudzutsa munthu amene wagona pogwira mapazi ake ndi manja pa malamulo Achisalamu, izi sizoloredwa.

Ndithudi, ngati Mtumiki wathu okondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم komanso odalitsika akuwadzutsa omutsatira ake ndi phazi lake lodalitsika, mwayi wakugona kwa munthu ogonayo udzakhala odzutsidwa. Ndipo akaika phazi lake lodalitsika pamutu, maso kapena nganga ya munthu wamwayi, mwa Allah عَزَّوَجَلَّ, adzamudalitsa munthuyo ndi kukhazikika kwa mtima ndi mtendere mmoyo wa dziko lapansi komanso moyo umene uli nkudza.

Mwa kamodzi ndi kamodzi chivomerezi cha Uhud chidatha, ndi mphamvu zazikulu ikani phazi lanu pomwe mungafune. O, inu Mtumiki okondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, Mtima maso ndi mutu wanga zonse zikudikira inu pano.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kupambana Kwa Kuwerenga Kalimah Pa Nthawi Ya Imfa

Zikuonetsa kuti ntchito za Muhammad Munir Husayn ku Dawat-e-Islami zabereka zipatso pamene adapatsidwa mwayi owerenga Kalimah Tayyibah mmasiku omaliza amoyo wake. Ndithudi amene wadalitsika kuwerenga Kalimah pa nthawi ya imfa yake, adzakhulukidwa mmoyo umene uli nkudza. Mtumiki wa Chisoni, nkhalapakati wa Ummah, adanena kuti; 'amene mawu ake omaliza (pakumwalira) adzakhale Kalimah لَآ اِلٰهَ اِلَّا اللّٰهُ adzalowa ku Paradiso. *(Sunan Abi Dawud, vol 3, p. 132, Hadith 3116)*

Panyengo ya imfa, amene angawerenge Kalimah adzalowa ku Paradiso ndi Chisoni cha Allah عَزَّوَجَلَّ.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Satana Wamphamvu Ndi Thanzi

Ma satana awiri adakumana. Winayo adali wa mphamvu ndi thanzi pamene wina adali opanda mphamvu ndi ofooka. Satana wa thanzi adamufunsa ofooka uja nati; 'M'bale wanga! Ndi chifukwa chiyani uli ofooka komanso opanda mphamvu?' iye adayankha nati; 'ndili pansi pa munthu ochita ntchito zabwino yemwe amawerenga بِسْمِ اللّٰه asadalowe mnyumba mwake, asadadye kapena kumwa chilichonse. Ndiye ndimayenera kumutalikira iyeyo, koma okondedwa wangawe uli ndi mphamvu komanso thanzi. Kodi pali chinsinsi chotani pa iwe?

Satana wathanzi adayankha; 'ndinasankhidwa kukhala ndi munthu osamva amene samawerenga بِسْمِ اللّٰه asadalowe mnyumba, asadadye kapena kumwa chilichonse, ndiye ine ndimatenga mbali pa ntchito zake zonse ndipo ndimamukwera iyeyo kunsana mofanana mmene munthu amakwerera nyama (ndipo ichi ndiye chinsinsi cha moyo wanga wabwino). *(Asrar-ul-Fatiha, p. 155)*

## Mayina A satana Asanu Ndi Anayi Komanso Ntchito Zawo

Okondedwa abale anga a Chisilamu! Taphunzira mu nkhani yomwe yapitayi kuti ngati tikulakalaka madalitso mu ntchito zathu komanso kufuna kutetezedwa kuti satana asalowe mu ntchito zathu, nthawi zonse tayenera kuwerenga بِسْمِ اللّٰه tisadayambe ntchito iliyonse yovomerezeka. Ngati osatero ndiye kuti satana otembeleredwa adzatilowelera pa ntchito zathu. Satana ali ndi ana ake ambiri amenenso ali ndi ntchito zawo za usatana.

Allamah Ibn Hajar Asqalani adanena mawu akuti Amir-ul-Muminin, Sayyiduna Umar Faruq Azam رَضِیَ اللّٰہُ عَنْهُ adanena kuti satana ali ndi ana asanu ndi anayi (9) awa;

1. zalitun 2. wasin 3. laqus 4. A'wan 5. Haffaf 6. Murrah 7. Musawwit 8. Dasim 9. Walhan

1. Zalitun ndiwosankhidwa kukhala mmisika mmene amaika mbendera yake.
2. Wasin adasankhidwa kuwapanaga anthu kuti azivutika zinthu zosayembekezera.
3. Laqus adasankhidwa kwa anthu opembedza moto.
4. Awan adasinkha ndikuikidwa kwa anthu olamura.
5. Haffaf ali ndi udindo kwa anthu omwa mowa
6. Murrah adasankhidwa kwa anthu oyimba nyimbo ndi zida zoyimbira (zing'wenyeng'enye).
7. Musawwit adasankhidwa kufalitsa mbiri. Izi zimapangitsa anthu kuti akhulupirire nkhani zabodza ndikuwalepheretsa kudziwa zoona.
8. Dasim adasankhidwa kunyumba. Ngati munthu sawerenga بِسْمِ اللّٰه polowa mnyumba mwake, kapena osapanga Salaam akalowa, satana ameneyu amabweretsa chisokonezo mnyumba kufikira kuti anthu amasiya banja kusiyana banja kuchokera ku chigamulo cha bwalo lovomerezeka kuti banja lithe kapena kumenyana kumene.

9. Walhan adasankhidwa pofuna kupereka chinyengo cha usatana mu mtima wa munthu pamene akupanga Wudhu, pa Swalah komanso pa ntchito zina zopembedza Allah. *(Al-Munabbihat, p. 91)*

## Kuthetsa Chisokonezo Cha Banja

Odziwika kwambiri pa kafotokozedwe ka Quran, Hakim-ul-Ummat, Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adanena kuti; 'munthu akamalowa mnyumba mwake ayenera kunena "بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم" ndikuyamba kulowa ndi mwendo wamanja, kenako anene Salam kwa anthu a banja lake. Ngati mnyumbamo mulibe munthu wina aliyense, olowayo anene kuti "اَلسَّلَامُ عَلَيْكَ اَ يُّهَا النَّبِيُّ وَرَحْمَةُ اللّٰهِ وَبَرَكَاتُهٗ" Ena mwa oyera mtima akhala akuwonedwa akuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndi Surah Al-Ikhlas pa nthawi yolowa mnyumba zawo pamene tsiku likuyamba. Izi zimabweletsa mgwirizano kwa okhala mnyumbamo ndipo zimapewetsa kukangana ndi kuwonjezera madalitso pa zofunika (zakudya) za mnyumbamo *(Mirat-ul-Manajih, vol. 6, p. 9)*

O, Allah wamphamvu zonse titetezeni kuchokera kwa satana. Tisungireni malo ku Paradiso ndi kutipewetsa ku chilango.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب        صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Werengani بِسْمِ اللّٰه Musanayambe Kudya

Ndi Sunnah kuwerenga بِسْمِ اللّٰه musanayambe kudya kapena kumwa (chilichonse chololedwa kutero). Sayyiduna Huzayfah رَضِىَ اللّٰهُ عَنْهُ adanena kuti; Mtumiki olemekezeka adayankhula kuti; 'chakudya chimene بِسْمِ اللّٰه sadanenedwe chimakhala chovomerezeka kwa satana (m'mawu ena zikutanthauza kuti satana amakhala nawo mugulu lakudya chakudyachi chisadayambe kudyedwa ngati بِسْمِ اللّٰه sadanenedwe)' *(Saluh Muslim, vol. 2, p. 172, Hadith 2017)*

## Chipulumutseni Chakudya Kuchokera Kwa Satana

Chakudya chisanayambe kudyedwa koma بِسْمِ اللّٰه sadanenedwe, chakudya chotere

sichikhala ndi madalitso. Sayyiduna Abu Ayyub Ansari رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ adafotokoza motere; 'tidali limodzi ndi Mtumiki odalitsika komanso okondedwa, mkhalapakati wa Ummah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم pa nthawi yomwe chakudya chidaperekedwa. Koyambirira kwa chakudyacho tidawona madalitso amene sitidawawonepo, koma cha kumapeto kwa chakudyachi tidawona kuti kudalibe madalitso. Tidafunsa Mtumiki kuti alongosole zimene zidachitikazi kodi inu mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi chifukwa chiyani zakhala choncho? Ndipo iye poyankha adati; 'tonse tanena بِسْمِ اللّٰه tisadayambe kudya, ndiye munthu wina amene sadanene بِسْمِ اللّٰه adakhala nkuyamba kudya ndipo satana anadya naye munthuyu. *(Sharh-us-Sunna, vol. 6, p. 62 Hadith 2818)*

## Ngati Munthu waiwala Kunena بِسْمِ اللّٰه

Umm-ul-Muminin, Sayyidatuna Aisha Siddiqah رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهَا adafotokoza kuti mtumiki adanena kuti; 'pamene munthu akudya chakudya atchule dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ (kutanthauza kuti anene بِسْمِ اللّٰه). Ngati munthuyo angayiwale kunena بِسْمِ اللّٰه poyambirira pa chakudya, ndiye kuti mkati mwa chakudya anene kuti "بِسْمِ اللّٰهِ اَوَّلَه وَاٰخِرَه" *(Sunan Abi Dawud, vol. 3, p. 356, Hadith 3767)*

## Satana Adasanza

Sayyiduna Umayyah Bin Makhshi رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ adafotokoza kuti; 'munthu wina adali kudya chakudya koma sadanene بِسْمِ اللّٰه pa nthawiyo mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adali pompo. Pamene munthuyo ankafuna kudya nthongo yomaliza, adakumbukira kuti sadanene بِسْمِ اللّٰه ndipo nthawi yomweyo iye adanena بِسْمِ اللّٰهِ اَوَّلَهٗ وَاٰخِرَهٗ. Powona izi Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adayankhula kwinaku akumwetulira,' satana amadya naye munthuyu. 'Pamene adatchula dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ, satana wasanza zimene zidali mmimba mwake' *(Sunan Abi Dawud, vol. 3, p. 35, Hadith 3767)*

## Palibe Chobisika Kuchokera Ku Maso Odalitsika A Mustafa (Mtumiki ﷺ)

Okondedwa abale anga Achisilamu! Munthu (msilamu) ayenera kunena بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم pamene akufuna kudya chakudya. Ngati munthu akudya chakudya popanda kunena

بِسْمِ اللّٰه, satana yemwe dzina lake ndi Qarin amakhala akudya naye munthuyu. Ndizodziwika kuchokera ku Hadith yofotokozedwa ndi Sayyiduna Umayyah Bin Makhsh رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ kuti diso lodalitsika la mtumiki wa anthu onse. Mtendere wa mtima ndi maganizo athu, opereka ndi kukoma mtima kuposa aliyense, adawona chilichonse ndipo ndi chifukwa chake adamwetulira atawona kukhumudwa kwa satana.

Odziwika bwino pa kafotokozedwe ka Quran yoyera, Hakim-ul-Ummat, Mufti Yar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza kuti; 'mtumiki wathu oyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ali wakutha mokwanira kuwona zolengedwa zobisika. Hadith ikulongosola poyera tanthauzo lake ndipo siifunanso kulongosola kwina kapena kumasulira kwina kodutsa pamenepo. Pamene sitimadya chakudya chomwe mwagwera ntchetche (pomwe ntchetcheyo isanachotsedwe) zili chimodzimodzi kuti chakudya chomwe patchulidwa dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ pakudya, satana sangadye kapena kugaya mmimba mwako chakudyacho. Ngakhale chakudya chosanzidwa ndi satana chili chosafunikira kwa ife, komabe satana apezeka kuti ndi odwala akhala ali ndi njala, ndipo madalitso achakudya chathu chotaikacho akhalabe ali chimodzimodzi ngakhale chakudya chatayika. Kutanthauza kuti ife tili ndi ubwino umodzi pamene satana ali ndi kuipa kuwiri.

Ndizotheka kuti satana sadzafunanso kudya nafe mtsogolo powopa kuti tidzanenanso بِسْمِ اللّٰه pa nthawi ya chakudya ndipo zidzamutengera satanayo kusanzanso chakudya chomwe wadya. Munthu mmodzi watchulidwa mu Hadith kuti amadya yekha. Zikadakhala kuti munthuyu amadya pamodzi ndi mtumiki wathu okondeka ndi odalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, munthuyu sakadaiwala kunena Bismillah chifukwa anthu opezeka ndi Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankanena بِسْمِ اللّٰه mokweza ndipo ankalangizana wina ndi mzake kupanga chimodzimodzi (kunena بِسْمِ اللّٰه) *(Mirat-Sharh-e-Mishkat, vol. 6, p. 30)*

Mu ma Qafilah a Madani ya Dawat-e-Islami, ma Dua onenedwa ndi بِسْمِ اللّٰه nthawi zambiri amakahala onenedwa mokweza mawu poyamba kapena pomaliza chakudya. Munthu amene akuyenda ndi ma Qafilah a Madani nthawi zambiri amakhala ndi mwayi ophunzira ma Dua ndi Sunnah. Mwayenera mwachizolowezi kuyenda ndi ma Qafilah a Madani mwa okonda Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Mvetserani mu chimodzi mwa zochitika ndikukhala osangalara.

## SIDDIQ AKBAR رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ ADACHITA OPERESHONI WA MADANI

Chidule cha nkhani yoperekedwa ndi munthu okonda Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم . Madani

Qafilah yodzadzidwa ndi Sunnah adali pa ulendo opita ku Naka Khari (Baluchistan, Pakistan). Mmodzi mwa atengambali pa Qafilah imeneyi adali ndi vuto la kupweteka kwa mutu chifukwa cha zotupa zinayi zazing'ono zomwe zidali pamutu pake. Pa nthawi yakumva kuwawa kwa zotupazi iye ankasautsika kwambiri ndi kusowa mtendere, zomwe zimachititsa malo a zotupazo ku nkhope kwake kukhala mtundu wakuda. Usiku umodzi adasautsika ndi ululu, ndipo tidamupatsa iye mankhwala oletsa kuwawa kotero adagona. Atadzuka mmawa, adali okondwa kwambiri. Iye adatifotokozera ife motere; Mwachisomo cha Allah ndinadalitsika ndi maloto a Mtumiki wathu olemekezeka ndi omutsatira ake apafupi anayi. Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adali akundiloza ine, ndikumuuza Abu Bakar Siddiq رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ kuti chotsa mavuto akupweteka kwanga kwa mutu.

Pa nthawiyi, mzake wa Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم mu phanga komanso ku manda, Sayyiduna Abu Bakar Siddiq رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ adapanga opereshoni wa Madani potsekula mutu wanga ndikuchotsa zotupa zakuda zinayi kuchoka mu ubongo wanga ndipo kenako iye (Abu Bakr) adati; mwanawe, tsopano palibe chomwe chingachitike kwa iwe.

M'bale ndithu adachilitsidwa. Pakubwelera kuchokera ku Madani Qalifah adapita ku chipatala kukawunika vuto lake la mmutu ndipo kumeneko dotolo adakuwa modabwa, 'Achimwene! Izi nzodabwitsa! Zotupa zonse zinayi zachoka mu ubongo mwanu! Pa izi iye (amene ankadwala) adalongosola misonzi ikutsika za maloto komanso madalitso omwe adakumana nawo poyenda ndi Madani Qafilah. Anakhutitsidwa pakumva zimenezi, ogwira ntchito m'chipatala okwana khumi ndi awiri (12) komanso ma dotolo ena adaganiza zoyenda ndi Madani Qafilah kwa masiku khumi ndi awiri (12). Madotolo adapanga chiganizo chokongoletsa khope zawo ndi chizindikiro chomukonda Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم pokhala ndi Sunnah yosunga ndevu.

Kufuna kuphunzira Sunnah ndi kupeza madalitso, yendani ndi Qafilah. Kufuna kudalitsika ndi chifundo cha Mtumiki, yendani ndi Qafilah.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِیْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Okondedwa abale anga Achisilamu! Zomwe zidachitika za munthu uyu adachizidwa mmaloto sizatsopano ayi. Chifukwa cha Mdalitso wa Allah عَزَّوَجَلَّ, Mtumiki wa chifundo, Mkhalapakati wa Ummah, صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amachilitsa matenda. Konzani chikhulupiriro chanu pomvetsera nkhani zisanu zokhudza anthu ochizidwa kudutsira mmaloto, nkhani

zofotokozedwa ndi Sayyiduna Imam Yusuf Bin Ismail Nabhani قُدِّسَ سِرُّهُ الرَّبَّانِي mu gawo la chiwiri la Buku lake lotchuka lotchedwa حُجَّةُ اللهِ عَلَى الْعٰلَمِيْنَ فِيْ مُعْجِزَاتِ سَيِّدِ الْمُرسَلِيْن.

## 1. Mtumiki Adabweretsa Kuwona (Maso)

Sayyiduna Muhammad Bin Mubarak Harbi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza kuti; 'Ali Abul Kabir adali osawona. Nthawi ina adalota atamuwona Mtumiki okondedwa ndi odalitsa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Mtumiki oyera adamuchiza poika dzanja lake pamwamba pa maso a Ali Abul Kabir. Abul Kabir atadzuka mmawa, adayamba kuwona. *(Hujjatullah alal-Alamin, vol.2, p. 526)*

Ndidalitseni ndi kuzindikira kuti ndikhale ndi masomphenya okuwonani. Madalitso miyandamiyanda akhale kwa inu.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب     صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 2. Mtumiki Adachiza Chotupa Chowundana

Sayyiduna Taquyyuddin Abu Muhammad Abdus Salam رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza kuti; 'M'chimwene wanga Ibrahim adali ndi zotupa pakhosi pake ndipo adali ululu owopsa. Nthawi ina adalota atamouna Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم M'maloto. Ibrahim adapempha, O Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم okondedwa ine ndavutika ndi ululu opweteka chifukwa cha matendawa. Mtumiki wa Chisoni, mkhalapakati wa Ummah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adayankha motere; 'pempho lako lamveka. Kuchokera ku madalitso a Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, mchimwene wanga adachitira. *(Hujjatullah-alal-Alamin, vol.2 p.526)*

Wabwera kwa kakonda wake amene akumwalira kuwonetsa kukhudzika kwake kwa Chisoni.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب     صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 3. Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Adachitiza Chifuwa Cha Mphuno

Oyera mtima Olemekezeka adafotokoza motere; 'ndidadwala kwambiri ndi kugonekedwa pa kama (bedi) mnyumba mwanga. Bambo anga okalamba nawonso ankavutika ndi nthenda ya asima adagonekedwa pa bedi mu chipinda cha pamwamba

cha nyumba yathu. Ine sindidakwanitse kuwayendera mu chipinda cha pamwambapo komanso iwo (bambo anga) adalephera kundiyendera ine kubwera kuchipinda cha m'munsi.

Mu usiku umodzi ndinadalitsika ndi maloto kumuwona Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Ndinatenga mtsamiro (pilo) kumupatsa Mtumiki olemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo ndipemphe machiritso amatenda amene ndinali kudwala komanso machiritso amatenda amene bambo anga anali kudwala (mphumu). Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم atamva pempho langa adakwera muchipinda cha mu mtunda (kumene bambo anga adagonenekedwa).

Panthawi ya pemphero la Fajr ndidamva mawu a munthu akubuula ndi ululu. Zoona zake ndizakuti adali bambo anga olemekezeka amene amabuula akutsika kuchokera mchipinda cha m'mwamba kuyenda m'masitepe. Abambowa adabwera kwa ine ndi kuyankhula kuti; 'mwana wanga, usiku walero ndadalitsika ndi Dalitso la Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم okondedwa ndi odalitsika. Ine ndidawayankha bambo ponena kuti; 'O, bambo anga okondedwa! Mtumiki olemekekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم wamudalitsa kale munthu ochimwa (ine) asadakwere kubwera kuchipinda chanu kumwambako kudzakupatsani Madalitso. Tonse awirife tapeza moyo wa thanzi kudutsira m'madalitso a Mtumiki wathu okondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. *(Hujjatullah-alal-Alaminn, vol. 2. Pp 527)*

*Umachiza matenda a mdziko mu nthawi yochepa, iwe Mtumiki (Ya Rasulallah)*
*Chonde ndichotsereni madandaulo ndi zovuta zanga mwa chifuniro cha Allah.*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 4. Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Adachiza Khate

Sayyiduna Shaykh Abu Ishaq رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza kuti; 'ndidali ndi khate pa phewa panga. M'maloto ndinadalitsika kumuwona Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Mtumikiyu ndinamuuza za matenda anga ndipo Mtumiki wachisoni, Mkhalapakati wa Ummat صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adaika dzanja lake pa phewa langa. Mmawa nditadzuka ndinachiritsidwa ku khate *(Hujjatullah-alal-Alamin, vol. 2, p. 531)*

Matenda a uchimo andiyandikitsa ine ku imfa. Moyo wanga suli bwino, chonde ndipatseni machiritso.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Adachiritsa Matuza A Mmanja

Munthu wina wangwiro adafotokoza kuti Shaykh Hammad رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه adali ndi matudza m'manja mwake. Matudza a ululu amenewa adaphulika. Madotolo onse adagwirizana kuti dzanjalo angolidula. Sayyiduna Hammad رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه adafotokoza kuti; 'usiku onse ndidali ndikumva ululu waukulu komanso ndi nkhawa nthawi yonseyi ndinali pamwamba pa denga la nyumba yanga ndinamupempha Allah عَزَّوَجَلَّ kuti andipatse machiritso.'

Nditagona mwayi wa kugona kwanga udadzuka pondidalitsa ndi maloto a Mtumiki oyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Mmaloto ndinamupempha Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuti; 'iwe Mtumiki (Ya Rasulallah) ndichiritse ine ku mavuto a matuza mudzanja langa!' Mkuyankha kwake Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adati; 'tambasula dzanja lako! Ndinachita monga mwa langizo la Mtumiki okondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adaika dzanja lake la Madalitso pa mwamba pa dzanja langa nkundiuza kuti; 'Dzuka!' pamene ndidaima matuza mudzanja langa adali atachiritsidwa kuchokera mmadalitso a Mtumiki okondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.

Odwalayu akumwalira ndipo machiritso ali mudzanja lako, O! iwe ochiritsa. Bwerani msanga, O, inu mwini Madinah, Bwerani msanga!

صَلُّوۡا عَلَى الۡحَبِيۡب      صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## CHINYENGO CHA SATANA

Ndi Allah عَزَّوَجَلَّ yekha ndi amene amapereka machiritso. Pakumvetsera mafanizo amene anenedwawa munthu akuvutitsidwa mmaganizo ndi chinyengo cha satana poganiza kuti; kodi aliponso opereka machiritso pambali pa Allah عَزَّوَجَلَّ?

## MACHIRITSO A CHINYENGO CHA SATANA

Popanda chikaiko mwa iye yekha ndi Allah عَزَّوَجَلَّ yekha amene ali ochiritsa (kutanthauza kuti ochiritsa weniweni ndi Allah) koma mmadalitso a Allah عَزَّوَجَلَّ ndi mphamvu zake, akapolo ake a Allah عَزَّوَجَلَّ akhoza kuchiritsanso. Koma ngati munthu wina angakhale ndi chikhulupiliro kuganiza kuti (munthu) wakuti ndi wakuti akhoza kuchiritsa munthu popanda mphamvu yochokera kwa Allah عَزَّوَجَلَّ (mphamvu ya Allah) ndiye kuti munthu

ameneyo ali opanda chikhulupiriro (Sali Msilamu) (Kafir) kaya ndi machiritso, kayanso ndi mankhwala, palibe amene angapereke ngakhale kochepetsetsa kwa ena popanda mphamvu yoperekedwa ndi Allah عَزَّوَجَلَّ.

Msilamu aliyense ali ndi chikhulupiriro kuti zonse zimene Atumiki ndi anthu oyera mtima amapereka (kwa ena) iwowo amapereka pokhapokha mu mphamvu zomwe iwowo apatsidwa ndi Allah عَزَّوَجَلَّ. Allah عَزَّوَجَلَّ atitalikitse, ngati pali munthu wina okhala ndi chikhulupiriro kuti Allah عَزَّوَجَلَّ sadapereke mphamvu kwa Mtumiki aliyense kapena kwa oyera mtima wina aliyense wa Chisilamu ndicholinga chochiritsa kapena kupereka china chake, ndiye kuti munthu wachikhulupiriro chotere akutsutsa chilamulo cha Quran yoyera.

Werengani vesi 49 ya Surah Al-e-Imran mu gawo lachitatu poyang'anira tanthauzo lake, chinyengo cha satana chidzachotsedwa ndipo satana sadzapindura ndipo adzakhala wokhumudwa. Quran yoyera ikunena zoyankhula zamadalitso za Sayyiduna Yesu (Isa) عَلَيْهِ السَّلَام motere;

وَ اُبْرِئُ الْاَكْمَهَ وَ الْاَبْرَصَ وَ اُحْيِ الْمَوْتٰى بِاِذْنِ اللّٰهِ ۚ

**'Ndipo ndichiritsa osapenya chibadwire ndi wakhate, ndi kuukitsa wa kufa mwa chilolezo cha Allah.**

*(Kanz-ul-Iman, part 3, Surah Al-e-Imran vesi 49)*

Mwaona? Sayyiduna Isa (Yesu) عَلَيْهِ السَّلَام mwapoyera komanso momveka bwino akulengeza kuti akupereka kuwona kwa anthu osapenya, akuchiza akhate komanso kudzutsa anthu akufa potengera mphamvu za Allah عَزَّوَجَلَّ zomwe zaperekedwa kwa iye. Mphamvu ndi ulamuliro osiyanasiyana zidaperekedwa kwa Atumiki ndi Allah عَزَّوَجَلَّ. Kuwonjezera apo, ndi madalitso a Atumiki, mphamvu zimaperekedwanso kwa ma Auliya ndipo iwowa amathanso kupereka machiritso ndi zinthu zina zambiri.

Pamene Sayyiduna Isa ali ndi ulemelero waukulu ndi wapamwamba choncho (potengerea ndi zimene zanenedwa mu Quran) tangoganizani kuti ndizodabwitsa bwanji ulemelero wa Mtumiki wathu okondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم komanso odalitsika Mustafa, amene ali ndi ulamuliro wa Atumiki onse kuwonjezerapo Sayyiduna Isa عَلَيْهِ السَّلَام!

Kumbukirani kuti Mtumiki olemekezeka صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم ali ndi ubwino wa Atumiki onse komanso ubwino wa zolengedwa zonse. Zoona zake ndizakuti aliyense amene ali ndi zabwino kapena kukonderedwa ndi Allah عَزَّوَجَلَّ ndichifukwa cha zabwino za Mtumiki Muhammad صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم.

Apapa taphunzira kunena kuti ngati Sayyiduna Isa angathe kuchiritsa odwala, kupereka machiritso amaso kwa osawona ndi kudzutsa anthu akufa, Mtumiki oyera Muhammad صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم ali nkuthekera kopereka zabwino (kwa Akakonda ake) mokulirapo poyerekeza ndi mmene Isa anaperekera.

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Zabwino Zokwana Zikwi Makumi Asanu Ndi Awiri Mphambu Zisanu Ndi Imodzi (76,000)

Zanenedwa ndi Sayyiduna Ibn Masud رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ kuti Mtumiki wa anthu onse, Ufulu wa mmitima ndi maganizo athu, opereka ndi okoma mtima oposa onse صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم adanena kuti; ‘ munthu amene anganene بِسْمِ اللّٰہِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْم, Allah عَزَّوَجَلَّ adzamulembera iye zabwino zokwana (4000) zikwi zinayi m'buku lake la zabwino pa lemba lirilonse la بِسْمِ اللّٰہِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْم, adzamukhululukira machismo okwana zikwi zinayi(4000) mmachimo ake, ndi kumukweza ulemerero wake pa nyota zokwana zikwi zinayi (40000).’ *(Firdaus-ul-Akhbar, vol. 4, p. 26, Hadith 5573)*

Abale anga okondedwa Asilamu! Kondwerani! Chisoni chachikulu cha Allah nchodutsa malire! Tiyeni tiwerenge; بِسْمِ اللّٰہِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْم ali ndi malembo okwana 19. Choncho tikawerenga بِسْمِ اللّٰہِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْم kamodzi owerengayo adzalandira zabwino zokwana zikwi 76, machismo okwana zikwi 76 adzakhululukidwa ndi zikwi 76 kuchuluka kwake. Allah ali ndi ubwino waukulu kwambiri.

## Nzeru (Zokhudza) Kusawerenga الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْم Pozinga Nyama

Potchula chisoni cha Allah عَزَّوَجَلَّ chopanda malire, Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ adanena kuti Ganizani pa nkhani yakuti بِسْمِ اللّٰہِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْم sanalembedwe mu Surah At-

Taubah. Mofanana, pamene tikuzinga بِسۡمِ اللّٰہ samatchulidwa yense, koma mmalo mwake بِسۡمِ اللّٰہِ اَللّٰہُ اَکۡبَر ndi amene amanenedwa. Kodi mudaganizapo kuti nchifukwa ninji timatero nanga pali nzeru zotani pamenepa kuti tizitero? Nzeru zake pamenepa ndizakuti Surah At-Taubah yonse ikukamba za Jihad (nkhondo) komanso kupha, chimene chili chilango kwa anthu okanira (Makafira). Zili chimodzimodzi kuti pamene tikuzinga, moyo wa chinyama chozingidwacho umakhala kuti ukuchotsedwa; nthawi yozinga imakhala ngati ya mkwiyo ndi chikakamizo. Pachifukwa ichi munthu ozingayo ali oletsedwa (otetezedwa) kunena zachisoni pa nthawiyi.

Pa chifukwa ichi, aliyense (amene ali ndi chizolowezi chowerengera بِسۡمِ اللّٰہ yonse بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِیۡم) adzatetezedwa ku mkwiyo wa Allah. *(Tafsir-e-Na'imi, vol. 1, p. 43)*

صَلُّوۡا عَلَی الۡحَبِیۡب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Nzeru (Kukhudzana) Ndi Malembo 19 A بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِیۡم

Kupambana kwina ndi kwakuti usiku ndi usana uli ndi maola 24, mwa maola amenewa 5 amakhala amapemphero asanu patsiku lirilonse. Pamene maola otsala 19, malembo 19 a بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِیۡم adavomerezeka.

Izi zikutanthauza pa ola lina lirilonse lomwe munthu adzakhala akunena بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِیۡم, lidzaganiziridwa (lidzatengedwa) kuti munthuyo wakhala akupembedza ola lirilonselo ndipo machimo ake a ola lirilonse adzakhululukidwa. *(Tafsir Kabir, vol. 1, p. 156)*

## Kufewetsedwa (Kuchepetsedwa) Kwa Chilango Cha Mmanda

Nthawi ina yake Sayyiduna Isa عَلَیۡہِ السَّلَام adadutsa pa manda nazindikira kuti munthu amene adaikidwa mmandamo adali kulangidwa. Patapita nthawi adadutsanso pa manda paja adawona kuti manda aja adali owala mkati mwake ndipo chisoni cha Mulungu chidaikidwa pa manda amenewa.

Mukudabwitsidwa, Sayyiduna Isa adapempha Allah عَزَّوَجَلَّ kuti amuuze chinsinsi cha zomwe adawonazi. Allah عَزَّوَجَلَّ adati; 'O, Isa! عَلَیۡہِ السَّلَام munthuyu adali kulangidwa chifukwa adali wochimwa kwambiri. Pamene adamwalira munthu ameneyu adasiya

mkazi wake ali woyembekezera ndipo adabereka mwana wa m'muna. Lero lino mwana wakeyu anatumizidwa ku Madarassah kumene mphunzitsi adamupangitsa mwanayu kuwerenga بِسۡمِ اللّٰه. Ndidachita manyazi kumulanga mamunayu pansi pa nthaka pamene mwana wake amatchula dzina langa pa mwamba pa nthaka. *(Tafir Kabir, vol. 1, p. 155)*

Allah Azzajalla amuchitire chisoni mamunayu ndipo atikhululikire ife popanda kutisungira mangawa mu chifuniro chake!

*Chisoni chanu chilibe malire, O mbuye wa Mustafa.'*
*Ndikhululukireni pa pa chifukwa cha Shah-e-Jilan.*

Tonse tiwaphunzitse ana athu kutchula dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ kuyambira pamene ali pa msinkhu wachichepere mmalo mowaphunzitsa ana mawu akuti 'Tata' kapenanso 'papa' Makolo omwalira sadzalandira madalitso azokhazo okha, koma ophunzira ndi ophunzitsa onse adzapeza malipiro ochuluka Choncho pamene mukucheza ndi ana anu, tchulani 'Allah عَزَّوَجَلَّ' kawirikawiri kwa iwo ndi cholinga chowaphunzitsa anawo, mu chifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ. Akafika pa msinkhu odziwa kuyankhula, anawa adzakhala akutchula dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ asanayambe kutchula mawu ena aliwonse.

## Kaleredwa Ka Ana Ku Madani

Sayyiduna Sahl Bin Abdullah Tustari رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza kuti; 'ndili ndi zaka zitatu ndidali ndikudzuka usiku ndi kukawawona malume anga akuchikazi, Sayyiduna Muhammad Bin Sawar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه akupemphera. Tsiku lina, malemuwa adandifunsa ine kuti; 'kodi sukumukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ amene adakulenga iwe?' Ine ndidawafunsa atsibweni angawo kuti; 'ndingamukumbukire bwanji Allah عَزَّوَجَلَّ?' Atsibweni angawo adandiyankha ponena kuti; 'usiku usadagone, uzikhala ndi chithunzithunzi chokhala ngati ukunena chiganizo ichi katatu mu mtima mwako popanda kuyendetsa lirime lako.

اَللّٰهُ مَعِیَ ، اَللّٰهُ نَاظِرٌ اِلَیَّ ، اَللّٰهُ شَاهِدِی

**'Allah ali ndi ine, Allah akundiwona ine, Allah ndiye mboni yanga.'**

Sayyiduna Sahl رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه akupitiriza kunena kuti; ''ndidanena ziganizo (mawu amenewa) kwa usiku owerengeka, kenako ndinawauza amalume anga za zomwe ndinkapangazo. Amalume adandifunsa kuti ndibwereze kunena zimenezi kokwana kasanu ndi kawiri

(7). Ndidapanaga motsatira malangizo a amalume anga ndipo ndinawafotokozeranso patapita usiku owerengeka. Kenako malumewo adandilangiza kuti ndibwereze kunena mawuwa kokwana khumi ndi kamodzi (11), ndipo ndidakwanitsa kutero mwa malangizo a amalume, ndipo pa nthawiyi ndinasangalatsidwa ndi mawu amenewa mumtima mwanga. Chaka chitatha, amalume anga adandilangiza; 'upitirire kunena zomwe ndakuphunzitsazi kufikira nthawi yako yolowa mmanda mwa chifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ. Izi zodzakuthandiza iwe mmoyo wadziko la pansi komanso mmoyo umene uli kubwera pambuyo pa moyo uno.'

Sayyiduna Sahl Bin Abdullah Tustari رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adapitirira kunena kuti; 'kupanga Dhikr pandekha, ndinapitirira kunena mawu amenewa kwa zaka zambiri kufikira kuti ndinamva kukula kwa uzimu ndi chisangalalo mu mtima mwanga. Tsiku lina amalume anga adandifunsa, 'O, Sahl! Kodi nkutheka munthu kunyozera Allah عَزَّوَجَلَّ kumachita kuti Allah عَزَّوَجَلَّ ali ndi munthuyo, akumuwona ndipo Allah عَزَّوَجَلَّ nkukhalanso mboni ya munthuyo pazochita zake? Ayi ndizachiwikire kuti ndi zosatheka munthu kunyozera Allah عَزَّوَجَلَّ. Choncho iweyo uwatalikire machimo.' Kenako, malume anga olemekeza adandiyambitsa Madrassah. Ndinawapempha aphunzitsi anga kuti azindilora kubwelera kunyumba ndikaphunzira kwa ola limodzi popeza sindimafuna kuti mchitidwe wanga wopanga Dhikr kuti usokonezedwe. Nditakwana zaka zokwana zisanu ndi chimodzi kapena zisanu ndi ziwiri (6/7) ndinakwanitsa kuloweza pa mtima Quran yonse. Ndinakwanitsa kusala kudya tsiku lirilonse ndikudya buledi nthawi ya dakwi.

Ndinapitiriza kupanga zimenezi mpaka ndidakwana zaka khumi ndi ziwiri (12). Nditakwanitsa zaka khumi ndi zitatu (13) ndinakumana ndi nkhani ya chipembedzo. Pofunafuna yankho la nkhani imeneyi, ndinapempha chilolezo kwa makolo anga ndipo ndinayenda ulendo  opita ku Basra (Iraq). Ndili kumeneko ndinawafunsa akatakwe ophunzira bwino za chipembedzo zokhudzana ndi nkhani yomwe idandipangitsa kufika kudera limeneri, koma palibe aliyense wa iwo amene adandipatsa yankho kuti ndikhutitsidwe, choncho ndinapita ku malo ena otchedwa Abbadan. Ndinafotokoza za nkhani yachipembedzo, munthu odziwika bwino ku Abbadan, Sayyiduna Abu Habib Hamzah Bin Abi Abdullah Abbadani amene adandipatsa ine yakho lomveka komanso logwira mtima.

Ndidakhala naye katakweyu kwa nthawi yaitali, kuwonjezera maphunziro anga, kupeza kuwala pa uzimu ndi kuphunzira makhalidwe abwino. Kenako ndidapita ku Tustar

pofuna kukwaniritsa zofuna zanga. Ndinkafuna kukwaniritsa zofuna zamoyo wanga, ndinkagula ufa wa tirigu wokwana 'Dirham' imodzi ndicholinga chopanga mkate (buledi) kuti ndidye. Usiku uliwonse ikakwana nthawi ya dakwi, ndinkadya chidutswa chimodzi cha mkate wa tirigu okwana kulemera ma giramu makumi asanu ndi awiri (70 grams) koma mkate opanda mchere ndiponso opanda ndiwo.

Dirhamu imodzi ya tirigu idali yokwana kwa ine chaka chonse chatunthu. Kenako ndidaganiza kuti ndizidya chakudya kamodzi kwa masiku atatu. Kenako ndinayamba kukhala ndi njala kwa masiku asanu, kenako kwa masiku asanu ndi awiri, kenako masiku okhala ndi njala ankafika makumi awiri ndi asanu (25) zomwe zikutanthauza kuti ndinkadya chakudya kamodzi pakapita masiku makumi awiri ndi asanu (25). Izi ndidakhala ndikupanga nditazolowera kwa zaka makumi awiri (20). Kenako ndidayendayenda ndi kuzungulira kwa zaka zambiri. Pambuyo pa zonsenzi ndidaganiza zobwereranso ndi chifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ.

Sayyiduna Imam Ahmad رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza kuti; 'sindidamuonepo Sayyiduna Sahl Bin Abdullah Tustari رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه akudya zakudya za mchere moyo wake onse. *(Ihya-ul-Uluni, vol. 3, p. 91)*

Allah عَزَّوَجَلَّ awachitire chisoni ndikutikhululukira ife tonse popanda kutisungira mangawa mu chifuniro chake.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Okondedwa abale anga Achisilamu! Mwayi ndi nzeru zakudya zili kwa makolo amene amakhudzika kwambiri ndi zabwino za ana awo zokhudza moyo wa mtsogolo poyerekeza ndi moyo umene tilinawo pano pa dziko la pansi. Tifotokoza nkhani ya kulimbikitsa chikhulupiriro yomwe ikukhudza mayi wa nzeru zakuya amene adachilimika mwa iye yekha pofuna kusintha moyo ndi khalidwe la mwana wake wa mwamuna. Werengani nkhaniyi ndi kukhala onyadira!

## Kupambana Kwa Phunziro La Maleredwe Ku Dawat-E-Islami

Kakonda wa mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ochokera ku Jhang (Pakistan) adafotokoza izi; 'mayi anga adali odwala kwa nthawi yaitali. Mayi angawa nthawi zonse ankafunisitsa kuti ine ndisiye machimo ndi kukhala munthu osinthika mmoyo mwanga. Chifukwa cha

kukonda kwawo Dawat-e-Islami, mayi anga ankandipatsa zofunika ndipo nthawi zonse adali akulimbikira kunditumiza kupita ku faizani-e-Madanah, likulu la Dawat-e-Islami dziko lonse la pansi, malo amene akupezeka ku Bab-ul-Madinah, Karachi. Amayi anga adandilangizanso kuti ku Faizan-e-Madinah ndikaphunzire maphunziro a maleredwa a ana (Tarbiyyat) pamodzi ndi Kakonda a mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم muchikhalidwe chodzadza ndi moyo wa chisoni ku Faizan-e-Madinah, ndipo anandiuzanso kufunika kowapangira Dua amayi anga, powafunira machiritso.

Ndidafika ku Bab-ul-Madinah, Karachi, kumene ndinayamba nawo course ya mareredwe (Tarbiyyat) ndipo ndinakhala ndikuyenda ndi ma Qalifah a Madani. Ndinapanganso maduwa kuwafunira machiritso amayi anga. Nditabwerera kunyumba pambuyo pomaliza maphunziro a mareredwe, ndinasangalatsidwa powona kuti amayi anga adali kupeza bwino ndi madalitso a Dua yomwe ndinapanga ndili ku Faizani-e-Madinah pamene ndimapanga maphunziro a Mareredwe.

Ndinayamika Allah عَزَّوَجَلَّ kuti ndi madalitso a phunziro la maleredwe, ndinali munthu ochirimika pa mapemphero ndipo ndinakhala nawo mugulu la makhalidwe a Madani Dawat-e-Islami. Ndidadzipanga kukhala okonda ntchito za Sunnah komanso kuyenda ndi ma Qafilah a Madani. Ndi chilakolako chokhazika mumtima mwanga kuti wachibale aliyense m'banja mwathu atenge moyo ndi makhalidwe a Madani, Dawat-e-Islami ndipo kuno mavuto athu atherethu.

*Amayi achiritsidwa ndipo ine ndakhala kakonda wa Sunnah.*
*Ndichisomo cha Allah, komanso ndi madalitso okhala nawo ku Faizan-e- Madinah.*

Amene amawapanga ana awo kukhala okonda dziko lapansi ndikuwapewetsa anawo kukhala ndi anzawo (magulu) abwino, oterewo amawaika anawo pa chiopsezo cha moyo umene uli kudza (pambuyo pamoyo uno)

## Kulepheretsa Anthu Ena Kukhala Nawo Pa Qalifah Ya Madani Kumabweretsa Zovuta

Mukulimbikira kwa iye yekha, Kakonda wa Mtumiki ochokera ku Madina-tul-Auliya Ahmedabad, India, adakwanitsa kumunyengerera mnyamata kuti akhale nawo pa ulendo wa Madani Qalifah koma abambo ake a mnyamatayu adamulepheretsa pa

ulendo wa maphunziro a chipembedzo pakuwona kuti mnyamatayu adzataya nthawi ya maphunziro ake a dziko lapansi. Mwatsoka, mnyamatayu adamuphera ufulu wokhala nawo mgulu la Akakonda a Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.

Mmalo mwake, mnyamatayu adalowa nawo mgulu la mnzake ochita zonyasa pakusanduka kukhala okonda kuledzera. Bambo tsopano adawona ndi kuzindikira za kulakwitsa kwawo kwakukulu ndipo adapita kukapempha kakonda wa mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم uja kuti akamutenge mwana wawo kukhala nawo ku Madani Qalifah ndicholinga chakuti mnyamatayu asiye moyo wakumwa mowa. Kakonda wa mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adayesetsanso, koma mnyamatayu adali atadzadzidwa kale ndi moyo wa uchidakwa. Komanso kukhala ndi anzake amakhalidwe onyasa kwambiri, zimene zidapangitsa kuti mnyamatayu asakhale okonzeka pa ulendo wa Madani Qalifah. Makolo ayenera kupereka mpata wa Madani, ochita zabwino kwa ana awo kuyambira pomwe anawo ali achichepere. Ngati osatero ndipo ana ndikuwonongeka chifukwa cha anzawo oyipa omwe amakhala ndi kuyenda nawo, makolowo mapeto ake adzanong'oneza bondo.

Tsiku lina, mlembi wa bukuli, Amir-e-Ahl-eSunnat (DBA) adandiuza kuti mchemwali wina wachisilamu adamupempha mchemwali wanga wamkuluyu kuti apange Dua yofuna kusintha makhalidwe oipa a mwana wake wa mmuna, pa nthawiyi mchemwali wachisilamuyu adali kugwetsa misonzi. Poyankha mchemwali wangayu adati; 'kalanga ine! Ine ndemwe ndinamuwononga mwana wanga wa mmuna ndidamuyambitsa maphunziro oloweza Quran (Hifz) pa Madrasa-tul-Madinah. Akabwerera kunyumba pambuyo pophunzira Sunnah ndi makhalidwe oyenera adali ndi chizolowezi chomatiuza zomwe waphunzira, koma ife tidali kumuseka. Chifukwa chowawidwa mtima, mwana wangayu adasiya kupita ku Madrasa-tul-Madinah. Pakadali pano wangosanduka mwana ongoyendayenda chifukwa cha anzake a makhalidwe onyansa. Mu nthawi iyi ndidalowa nawo muzochita za Madani ya Dawat-e-Islami. Pakadali pano ndikunong'onedza bondo pazachipongwe zomwe ndidamuchitira mwana wanga. Kalanga ine! Sindikudziwa chomwe chidzandichitikire ine!

صُحبتِ صالِح تُرا صالِح کُنَد        صُحبتِ طالِح تُرا طالِح کُنَد

Kukhala limodzi ndi anthu opanga ntchito zabwino za Allah zimakupangitsa iwe kukhalanso wopanga zabwino, pamene gulu la opanga zoipa lidzakupanganso iwe

kukhala oipa.

## Nyumba Ya Nyama Zambiri

Okondedwa abale anga Asilamu! Sayyiduna Sahl Bin Abdullah Tustani رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه adali Siddia (munthu oyera mtima okhala mgulu la anthu a ulemelero wapamwamba). Iyeyo ankapewa (zokoma) zolawa ndi zachisangalalo. Samagwiritsa ntchito mchere mu chakudya chake chifukwa kugwiritsa ntchito mchere, kumapangitsa chakudya kukoma.

Ngakhale chakudya chitaikidwa zokometsera za mitundu yonse, koma ngati mulibe mchere ndithu chakudayacho sichikoma.

Ndizofunikanso kudziwa kuti kuchuluka koyenelera kwa mchere, kuli kofunikira mthupi la munthu, kotero kuti ichi chidali chozizwitsa china cha Sayyiduna Sahl Bin Abdullah Tustari رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه, iyeyo adakhala ndi moyo popanda kudya chakudya chothira mchere kwa nthawi yaitali. nyumba yake yodalitsika yomwe idali ku Tustar inkatchedwa kuti Bayt-us-Siba' (nyumba ya nyama zambiri) chifukwa chakuti nyama zambiri monga mikango, akambuku ndi nyama zina zidali kubwera pa nyumba pake pomwe iye ankazidyetsa nyamazo.

Kumapeto kwa moyo wake, Sayyiduna Sahl Bin Abdulla Tustari adapuwala, koma nthawi ya mapemphero, kupuwala kwake kunali kusowa kufikira kuti ankakwanitsa kupanga mapemphero ake bwinobwino. Iye akangomaliza kupemphera, kupuwala kuja kumabwereranso mwa iye ngati kale.

Allah عَزَّوَجَلَّ amuchitire chisoni iye komanso atikhululukire ife popanda kutisungira mangawa nchifuniro chake.

صَلُّوۡا عَلَى الۡحَبِيۡب    صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Machiritso A Kutentha Kwa Thupi

Zikufotokozedwa kuti munthu adadwala kutentha thupi. M'phunzitsi wake olemekezeka wa munthu odwalayu Shaykh Faqih Wali Umar Bin Sa'id رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه adamuyendera odwalayu. Atamupatsa ta'wiz (mankhwala auzimu ochita kulemba) Shaykh adamulangiza ophunzira wakeyu kuti asatambasule ndikuwona zomwe zidali

mmankhwalamo. Shaykh atachoka odwalayu adavala mankhwalawa ndipo nthawi yomweyo adachira ku matenda a kutentha thupi.

Ndikudabwitsidwa pamene adachira adafunabe kudziwa zomwe zidali mmankhwalawo. Atatambasula mankhwalawo adapeza kuti palembedwa بِسۡمِ اللّٰهِ الرَّحۡـمٰنِ الرَّحِيۡمِ. Chinyengo cha satana chidamufikira odwalayu poganiza munthu wina aliyense akadakwanitsa kulemba zimenezi! Pamene (chilemekezo) ulemu wake wopereka kwa Shaykh akewa udamuthera, nthawi yomweyo matenda aja adayambiranso.

Ali odandaula odwalayu adapita kwa Shaykh ndikupepesa zomwe adalakwa. Shaykh adakonzaso mankhwala aja (Ta'wiz) ndikumangirira ku dzanja la odwala pamodzi ndi dzanja lake (la iye Shaykh) ndi kuchiritsa matendawo nthawi yomweyo. Pa nthawiyi Shaykh sadamuletse odwalayu kuwona zomwe zidali mmankhwalamu, komabe pa iye yekha, odwalayu sadatsekule mankhwalawa powopa zomwe zidamuchitikira poyamba zija. Kumapeto kwake, chaka chitatha, adamasuka nkupeza kuti padalembedwa بِسۡمِ اللّٰهِ الرَّحۡـمٰنِ الرَّحِيۡمِ.

Allah عَزَّوَجَلَّ amumvere iye chisoni komanso atikhululukire ife popanda mangawa pachifukwa cha iye.

Okondedwa abale anaga Asilamu! بِسۡمِ اللّٰهِ الرَّحۡـمٰنِ الرَّحِيۡمِ ali ndi Madalitso ochuluka (osawerengeka). Alinso ndi machiritso pa matenda. Fanizo lomwe tawerengali likupereka phunziro lonena kuti ngati Msilamu woyera mtima akumuletsa munthu wina ngakhale zinthuzo zikhale zovomerezeka pachisilamu, munthu oletsedwayo ayenera kumvetsera ndikuzipewa zimene waletsedwazo, ngakhale kuti oletsedwayo sakudziwa zifukwa zomuletserazo. Phunziro lina ndilakuti munthu sayenera kutambasula Ta'wiz chifukwa kulemekezeka kwa munthu wina kukhoza kukhudzidwa ngati angatero. Kuwonjezera apo, Ta'wiz imapindiwa mnjira yakeyake ndipo nthawi zina madua apaderadera amanenedwa pa nthawi yopindayo. Choncho kutambasula kapena kuwona Ta'wiz kukhoza kuchotsa phindu lopezeka (zabwino) mu Ta'wiz.

## 5 Machiritso A Kuphwanya Kwa Mthupi Opezeka Ku Madani

لَا يَرَوۡنَ فِيۡهَا شَمۡسًا وَّلَا زَمۡهَرِيۡرًا ﴿۱۳﴾

**Sadzamva m'menemo kutentha kwa dzuwa kapena kuzizira!**

*(Kanz-ul-Iman, part 29 Surah Ad-Dahr vesi 13)*

1. Werengani vesi limeneli kokwana kasanu ndi kawiri (7) powonjezerapo Salat-Alan Nabi صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kamodzi pambuyo komanso mukamaliza kuwerenga vesi limeneli, kenako muuzire (mpweya) pa munthu odwalayo, 'm'bukuli mawu oti 'Dam' agwiritsidwa ntchito ngati machiritso a auzimu ndipo katchulidwe ka mawu amenewa ngati ***d^m***. asatchulidwe kuti '***daem*****!**'dziwani kuti mawuwa ayikidwa mu Italic m'buku lonseli poika 'D' chilembo chachikulu.'m'chifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ kuphwanya kwa mthupi kudzachepetsedwa ndipo odwala adzamva bata la mthupi. (Dziwani kuti sizili zofunikira kuwerenga tanthauzo la vesi)

2. Sayyiduna Iman Ja'far Sadia رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ adanena kuti; 'werengani Surah Al-faatihah kokwana makumi anayi (40) (powonjezerapo Salat-Alan-Nabi صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kamodzi poyamba komanso ku mapeto kowerenga Faatihah) kenako mupange Dam (kuwuzira mpweya mmadzi kenako madziwo awazidwe kumaso kwa munthu odwalayo, mukatero kuphwanya kwa thupi kudzachiritsidwa m'chifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ.

3. Pamene Mtumiki okondedwa ndi odalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adadwala kuphwanya thupi, Sayyiduna Jibrail عَلَيْهِ السَّلَام adawerenga Dua yotsatirayi kenako adapanaga Dam:

بِسْمِ اللّٰهِ اَرْقِيْكَ مِنْ كُلِّ دَاءٍ يُّؤْذِيْكَ
وَمِنْ شَرِّ كُلِّ نَفْسٍ اَوْ عَيْنِ حَاسِدٍ ط اَللّٰهُ يَشْفِيْكَ بِسْمِ اللّٰهِ اَرْقِيْكَ

**Tanthauzo: ndikukuchiza mu dzina la Allah ku nthenda iliyonse ingakusautse, komanso ku zoipa zonse ndi diso la nsanje, Allah akupatse machilitso, mu dzina la Allah ndikukuchiza.**

*(Sahih Muslim, p. 1202, Hadith 2186)*

Nenani Dua imeneyi mu chiyankhulo cha ChiArabu basi (pamodzi ndi Salat-Alan-Nabi, kamodzi koyambirira komanso kumapeto kwa Dua imeneyi) kenako mupanga Dam (muuzire mpweya pa wodwalayo)

4. Munthu odwala kuphwanya kwa thupi nthawi zonse aziwerenga mawu akuti بِسْمِ اللّٰهِ الْكَبِيْرِ.

5. Zanenedwa mu Hadith Yodalitsika motere; ngati m'modzi wa inu adwala kuphwanya kwa thupi, muwazeni madzi odwalayo mmawa kwa masiku atatu. *(Al- Mustadrak, vol. 4, p. 223, Hadith 7438)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب　　صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Tikuyamika Allah عَزَّوَجَلَّ kuti Abale ndi Alongo a chisilamu amene ali pamodzi ndi Dawat-e-Islami, bungwe ladziko lonse la pansi lomwe silipanga za ndale koma za chipembedzo pogwiritsa ntchito Quran ndi Sunnah, onsewa ali onyadira pokhala iwowo Akakonda a Mtumiki okondedwa ndi Wodalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Nthawi zina, chifukwa cha madalitso a Dua yopangidwa nthawi ya Madani Qalifah yodzadzidwa ndi Sunnah ku Dawat-e-Islami pamodzi ndi Akakonda a Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, odwala ena amakhala akuvutika ku matenda osachiritsika ndi madotolo, anthuwa amachira ndikupezanso chisangalalo chawo mmoyo.

## Osawona Amabwezeretsedwa Kuwona

Nthawi ina yake Mlaliki wa Dawat-e-Islami wochokera ku Liaqat Colony, Hyderabad (Bb-ul-Islami Sindh, Pakistani) adamuitanira mnyamata ku ulendo wa Madani Qalifah ya Dawat-e- Islami mnyamata woitanidwayu adanyansidwa ndi kukhumudwa, kotero iye adayankha; 'opereshoni wa maso a amayi anga wakanika, pachifukwa ichi amayi anga akhala osawona. Tiri mu mavuto aakulu, iwe ukundifunsa ine kukhala pa ulendo ndi Madani Qafilah!'

Mowugwira mtima ndi kulimbikira kwake, Mlalikiyu adamuyankha mnyamatayu mokhudzika popanga Dua ya amayi ake motere; 'Allah awadalitse amayi ako ndi machiritso! Madotolo akutinji pa matenda a amayi ako?' mnyamatayu adayankha; 'madotolo akunena kuti amayi anga sangachiritsidwe ngakhale atatengedwa kupita ku America kuti akachiritsidwe. Akumusisita ku msana mokhudzika, Mlalikiyu adayankhula ndi mawu a chipepeso kwa mnyamatayu, 'mchimwene wanga! Ngati madotolo akukhumudwitsa iwe, ndichifukwa chiyani ukutaya chiyembekezo? Madotolo sangachiritse wina aliyense. Ndi Allah عَزَّوَجَلَّ yekha amene ali m'chiritsi wa aliyense. Dua

ya munthu wa paulendo imayankhidwa ndi Allah عَزَّوَجَلَّ. Ukayenda ndi Madani Qalifah pamodzi ndi Akakonda a Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم komanso ndikuwapangira Dua amayi ako pa ulendo umenewu, udzapeza madalitso ake.'

Atalimbikitsidwa komanso kukhutitsidwa ndi kudzipereka kotherathu komwe kudali ndi Mlaliki ameneyu, mnyamata odandawulayu adanyamuka pa ulendo wa Madani Qafilah umene pa nthawiyi adapanga Dua modzichepetsa kuwapangaira amayi ake. Atabwerera kunyumba pambuyo pa Madani Qafilah, adakondweretsedwa pakuwona amayi ake kuti akukwanitsanso kuwona (kuwona kwawo kwabwezeretsedwa)

Kufuna kukolola Chisoni cha Allah, yendani ndi Qafilah, kufuna kuphunzira Sunnah, yendani ndi Qafilah.

Kufuna kuwonanso komanso kukhala ndi mtendere mmoyo mwanu, kufuna kupeza mtima wokhazikika, yendani pamodzi ndi Qafilah.

Okondedwa Abale anga Achisilamu! Mtumiki oyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adanena kuti; 'mitundu itatu ya Dua imalandiridwa ndi Allah. Palibe chikaiko chilichonse mkulandiridwa kumeneku.

1. Dua yopanga munthu amene akuponderezedwa.
2. Dua yopanga munthu amene ali pa ulendo.
3. Dua yopanga bambo kumupangira mwana wake. *(Jami' Tirmidhi, vol 5, p. 280, Hadith 3459)*

Ngati munthu akuyenda ndi Madani Qafilah pamodzi ndi Akakonda a mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, Dua yake ndiyoyenera kutheka kulandiridwa. Fanizo limeneli likuwonetsanso kuti kulolera ndikofunika pamene munthu akulimbikira ntchito ya chipembedzo. Ngakhale mutanyozedwa ndi kumenyedwa, muyenerabe kukhala olimbikira pa inu nokha popanda kuwonetsa kukhumudwa. Ngati mungawonetse mkwiyo kapena kusadekha, mudzapangitsa zina kutayika pa chipembedzo. Musasiye kuwalangiza anthu ena, chifukwa kulangizaku nchachidziwikire kudzabereka zipatso. Allah عَزَّوَجَلَّ wanena momveka mu vesi 55 ya Surah Ad-Dhariat gawo 27;

وَ ذَكِّرْ فَاِنَّ الذِّكْرٰى تَنْفَعُ الْمُؤْمِنِيْنَ ﴿۵۵﴾

**'Kumbutsa (langiza), ndithu, kukumbutsa (kulangiza) kumawathandiza okhulupirira.'**

## Machiritso A Mutu

Kayesar wa ku Roma adatumiza kalata kwa Amir –ul-Mminim Sayyiduna 'Umar Faraq Azam رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ Mu kalata yake adatchulamo nkhani yake yakuti; 'ndili ndi matenda a mutu a mgonagono, ngati uli ndi mankhwala ena aliwonse a matendawa, chonde unditumizireko'

Amir-ul-Muminum Sayyiduna Umar Faruq A'zam رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ adamutumiza chikofiya (chisoti) cha nsalu kwa mfumu Kayesar. Nthawi iliyonse mfumu Kayesar akavala Chikofiya chimenechi amamva bwino ku vuto lake la mutu, ndipo akakhala kuti wavula chikofiyacho, vuto lake la mutu limamuyambiranso. Podabwitsidwa ndi zimenezi, mkati mwake mwa chikofiya adapezamo pepala lolembedwa بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم. *(Asrar-ul-Fatihah, p. 163; Tafsir Kabir vol. 1, p. 155)*

## Njira Za Kachiritsidwe Ndi بِسْمِ اللّٰه

Okondedwa Abale anga Achisilamu! Taphunzira kuchokera ku fanizo lomwe lapitali kuti ngati munthu wina angakhale ndi vuto la kupweteka kwa mutu, ayenera kulemba بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم pa pepala, kapena kulembedwa ndi kumangilira mmutu ngati Ta'wiz. Lembani pogwiritsa ntchito ink (monga cholembera, kapena pentopeni (marker) ndikusiya zunguliza wa 'ہ' ndi malembo onse atatu a م a بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم otsekula.

Mfundo za kalembedwe ka Ta'wiz ndikoti ngati munthu akulemba Ayah (vesi) ya Quran kapena mawu ena apaderadera, zunguliza aliyense wa zunguliza okhala ndi chilembo akhalae otsekula, mwachitsanzo;

Sizofunika kuyika zizindikiro zosiyanitsa

Mukalemba zimenezi, mukutire mu pepala lomwe silingasungunuke m'madzi kapena kukulunga m'pepala la pulasitiki, kenako muike mu chikopa kapenanso mkachidutswa ka nsalu ndikumangilira mmutu. Amene amavala nduwira mmitu yawo akhoza kungosokera Ta'wiz ku nduwira zawo mkati mwake. Chimodzimodzi alongo athu a Chisilamu akhoza kusokera limodzi ndi mipango yawo kapena ku zitchingo (velo) za

mmutu mwawo. Kuchita zimenezi ndi chikhulupiriro kuwawa kwa mutu kudzatha mchifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ.

Sizikuloledwa kwa anthu amuna kuvala Ta'wiz woikidwa mchinthu chomwe ndi cha golide kapenanso siliva mwinanso choika chilichonse cha chitsulo. Zili chimodzimodzi kusaloledwa komanso tchimo kwa amuna kuvala tcheni chopangidwa ndi chitsulo ngakhale tchenicho kutaikidwa Ta'wiz ndizoletsedwa.

Kuwonjezera apo, ndizoletsedwa kwa munthu wa mamuna kuvala zokongoletsa za zithunzi, zibangiri kapena Zavala mmanja ndi pakhosi zokhala ndi golide, siliva, kapena zachitsulo zilizonse, kaya pali zolembedwa pa chitsulopo kapenanso ngati palibe, komanso ngakhale zitakhala kuti pa chitsulopo pali dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ mwinanso Kalimahh Twayyibah ndi zina zilizonse za nchipembedzo Msilamu Sali ololedwa kuvala zimenezi pa thupi lake, mmanja, pkhosi kapena mchiuno. Koma amayi anthu aakazi ali ololedwa kuvala Ta'wiz oyikidwa mu golide, kapenanso mu bokosi la siliva.

## Machiritso A Kupweteka Kwa Mbali Ina (Theka) Ya Mutu

1. Ngati munthu akumva kupweteka (kuwawa) kwa mbali ina yamutu wake, werengani Surah Ikhlas kamodzi pamodzi ndi Salat-Alan-Nabi صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم kamodzinso poyamba ndi pamapeto pa Surah Ikhlas ndi kumuwuzira munthu odwalayo (Dam). Ngati kuli kofunika kuwuzilako kukhoza kuchitika motere; katatu, kasanu ndi kawiri (7), khumi ndi kamodzi (11) mu chifuniro cha Allah kupwetekako kudzatha musanakwanitse kuwuzira kakhumi ndi kamodzi (11)

2. Nyikani jinja owuma mmadzi, ndipo mbali ya jinja yomwe yanyikidwa mmadziyo mupake pa mphumi (mutu). Kuwawa kwa mbali yamutu kudzatha mukatero muchifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ.

3. Nyikani masamba owuma a minti pamodzi ndi mphesa mmadzi kwa maola angapo, kenako mumwe madziwo. Izi zidzakhala zothandiza mu chifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ. Madzi amene ayenera kugwiritsidwa ntchito ndi omwe ali ochokera m'mbiya (mtsuko) ya dothi.

4. Kumwa ghee wosakaniza ndi mkaka otentha, zimakhalanso zothandiza.

5. Kumwa madzi a kokonati zimathandiza kuthetsa kupweteka kwa mutu wonse.

6. Kusungunula mchere m'madzi wofunda mchiwiya chomwe chili chachikulu ndi kuika mapazi mchiwiyacho kwa mphindi zokwana khumi ndi ziwiri (12). Izi zidzathandiza kuletsa kuwawa kwa mutu mchifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ. Kutalika kwa nyengo ya machiritso awa kudzatengera kukula kwa matenda amene akufuna kuchiritsa.

## Machiritso Asanu Ndi Awiri (7) Okhudza Mutu

لَا يُصَدَّعُوْنَ عَنْهَا وَلَا يُنْزِفُوْنَ ﴿۱۹﴾

***(Zakumwa zake) zosapweteketsa mutu ndiponso zosaledzeretsa.***

*(part 27, Surah Al- Waqiah, vesi 19)*

Werengani vesi imeneyi kokwanira katatu, pamodzi ndi Salaat-Alan-Nabi kamodzi musadanene vesi komanso mukamaliza kuwerenga vesi imeneyi, pambuyo pa zonsezi muwuzire (Dam) munthu amene akudwala mutuyo. Munthuyo adzapeza bwino.

7. Werengani Surah An-Nas kokwanira kasanu ndi kawiri (7), powonjezerapo Salaat-Alan-Nabi kamodzi musadasome Surah An-Nas komanso mukamalidza kusoma Surah An- Nas, ndipo kenako awuzire mmutu mwa munthu odwalayo kenako mumufunse odwalayo ngati akumvabe mutu amuuzirenso. Ngati odwalayo akumvabe kuwawa kwa mutu, mubwereze kuwuzira kachitatu. Ngakhale mutuwo kaya mbali yamutu ikupweteka cha mtundu bwanji, kupweteka kwa mutuwo kudzatha kuwuzira kwa chitatu kusanachitike.

8. Kupweteka kwa mutu wonse kapenanso kupweteka kwa theka la mutu, werengani Surah At-Takasur kamodzi pambuyo pa Salat-ul-Asr, pamodzi ndi Salat- Alan- Nabi kamodzi musawerenge Surah At-Takasur komanso kamodzi pambuyo pakuti mwawerenga Surah At-Takasur kenako muwuzire (Dam) kupweteka kwa mutu kudzachepetsedwa mukatero mchifuniro cha Allah.

9. Ikani mchere pa lilime kwa mphindi khumi ndi ziwiri (12) kenako imwani kapu ya madzi mutu ungawawe bwanji, pamapeto popanga zimenezi kuwawako kudzachepetsedwa mchifuniro cha Allah. (Zindikirani kuti kugwiritsa ntchito

mchere kwa munthu amene akudwala nthenda ya kuthamanga kwa magazi sikuli kwabwino)

10. Ikani sipuni imodzi yakale mkapu ya madzi, mukatero muwiritse madziwo. Madzi akawira, mumwe kapena mununkhize nthunzi ya madziwo, kuwawa kwa mutu kudzatha mu chifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ. (Mudzigwiritsa ntchito khale pophika ndiwo kapena zakudya zina) Munthu amene amakwanitsa kudya khale okwana galamu imodzi (1 gram) tsiku lirilonse, munthuyo adzakhala wotetedzedwa ku matenda akhansa.
11. Idyani Jalaybi wotentha komanso wophikidwa kumene dzuwa lisanatuluke zomwe zakazingidwa mmafuta a ghee. Kuwawa kwa mutu kudzatha mchifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ. (Jalaybi ndi zakudya zozuna zaku Asia)
12. Ngati munthu amamva kuwawa kwa mutu apo ndi apo, sungunulani mankhwala awiri oletsa kupweteka mthupi, mukatero mumwe pambuyo pa chakudya. Kuwawa kwa mutu kudzathetsedwa mchifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ. (Ngati munthu angafune kumwa mankhwala oletsa kupweteka mthupi, ayenera kumwa pambuyo pa chakudya chifukwa kumwa mankhwalawa munthu asadadye kumabweretsa mavuto)

Maganizo operekedwa kuchokera ku Madani ndi akuti; Ngati munthu amene akudwala kuwawa kwa mutu sakupezabe bwino pambuyo pakumwa mankhwala akuchipatala ayenera munthuyo kukayezetsa maso ake.

Ngati kuwona maso ake kuli kufooka, munthuyo azivala magalasi. Izi zidzachepetsa vuto la kupweteka kwa mutu mwa chifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ. Ngati sakuchilabe vuto la kuwawa kwa mutu, munthu odwalayo ayenera kukakumana ndi dotolo oyang'nira za ubongo. Ngati osasamala zimenezi, zikhoza kubweretsa chiwonongeko pa moyo wa munthu odwalayo.

## Machiritso A Mtsamphuno (Kamfuno)

Ngati munthu wapezeka ndi vuto la mtsamphuno (magazi wotuluka mphuno), iyeyo ayenera kulemba pogwiritsa ntchito chala cha mkomba phala mawu akuti; بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم,

kuyambira pa mphumi pake kulekezera pamapeto pa mphuno yake. Magazi wofulukawo adzasiya muchifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ.

## Faniziro Lokhudza Mankhwala

Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza kuti; 'ngati odwala atanena بِسْمِ اللّٰه asadamwe mankhwala, mankhwala amenewo adzagwira ntchito.'

Nthawi ina yake Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام adamva kupweteka mmimba kwambiri. Modzichepetsa iye adamupempha Allah عَزَّوَجَلَّ kuti amuchotsere mavuto akewo ndipo Allah Awwajalla adamulamula Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام kuti adye zitsamba zakuti zakuti kuchokera kutchire. Choncho Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام adadya zitsamba zimenezi ndipo nthawi yomweyo adachira ku mavuto ake a mmimba aja.

Patapita masiku, mavuto a mmimba aja adamuyambiranso, ndipo iye adadyanso zitsamba zomwe zija. Mosemphana ndi zomwe amayembekezera, mavuto a mmimba adakulanso kwambiri. Modzichepetsa adamupempha Allah عَزَّوَجَلَّ wamphamvu zonse kuti; 'O, Allah pali chinsinsi chanji pa izi? Mankhwala amodzi ali ndi zotsatira ziwiri zosiyana! Nditamwa poyamba paja, mankhwala adandichiritsa, koma pamene ndamwa kachiwiri mavuto anga akupweteka kwa mmimba awonjezereka.' Allah adati; 'O, iwe Musa! Poyamba paja udagwiritsa ntchito zitsamba ndi lamulo langa, koma pa nthawi ino wagwiritsa ntchito mogwirizana ndi iwe mwini mmene ukudziwira. O, Musa, machiritso ali mdzina langa. Popanda Dzina langa chilichonse cha mdziko la pansi ndi chakupha ndipo dzina langa ndilimene liri machiritso a chiphe.' *(Tafsir-e-Naini, vol. 1, p. 42)*

Allah عَزَّوَجَلَّ amuchitire chisoni ndi kutikhululukira ife pachifukwa cha iye!

## Khulupirirani Allah Osati Mankhwala

Fanizo lomwe talongosola m'mwambamo likuwonetsa kuti munthu ayenera kukhulupirira Allah عَزَّوَجَلَّ osati mankhwala. Ngati Allah عَزَّوَجَلَّ atafunandiye kuti mankhwala achiritsa matenda. Ngati Allah عَزَّوَجَلَّ sakufuna, ndiye kuti mankhwala omwewo akhoza kupangitsa kuti matenda akule kwambiri.

Zimaonetsa kuti mtundu wina wamankhwala umachiritsa munthu odwala, komanso mtundu omwewonso wa mankhwala akamwa munthu wina, umaika moyo wa odwalayo

pa chiswe kupangitsa odwalayo kudwala matenda ena owopsa kapena kupuwala kumene mwinansoo kufikira kumwalira. Pamene wina aliyense akumwa mankhwala, ayenera kuwerenga (kunena) بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم kapena بِسْمِ اللّٰهِ الشَّافِيْ بِسْمِ اللّٰهِ الْكَافِيْ.

## Kukhutitsidwa Kwa Mtima

Allah عَزَّوَجَلَّ adatumiza vumbulutso kwa Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام, 'mtima uliwonse umakhala ndi ludzu ukamachoka pa dziko lapansi kupatula yekhayo wawerenga (wanena) بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم *(Asrar-ul-Fatihah, p. 162)*

## Ubwino Pakuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم Mopambana Kwambiri

Sayyiduna Ali Murtadhwa رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ adafotokoza kuti; 'munthu wina adawerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndipo munthuyo adakhululukidwa machimo ake. *(Shu'ab-ul-Iman, vol. 2, p. 546, Hadith 2667)*

## Kukoma Kwa Dzina La Kumwamba Kumabweretsa Chikhululuko

Munthu wina wamamuna kutulo kwake adawona munthu ochimwa ndipo adamufunsa, 'kodi Allah عَزَّوَجَلَّ wakupangira iwe zotani?' ochimwa uja adayankha kuti; 'nthawi ina yake ndikuyenda kudutsa pamalo pomwe padali Madrassah, ndinamva بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ikuwerengedwa ndi munthu wina wake. Kukoma kwa Dzina lokoma la Allah عَزَّوَجَلَّ zidabweretsa kukhudzika kwina kwake pa ine mu mtima mwanga. Pa nthawi yomwe yonso ndinamva mawu ochokera mseri (Ghayb), onena kuti, 'sitidzasonkhanitsa zinthu ziwiri pamodzi (1) kukoma Dzina La Allah عَزَّوَجَلَّ (2) mazunzo (zowawa) imfa *(Anis-ul-Wa'iszin, p. 4)*

Chisoni cha Allah عَزَّوَجَلَّ chikhale pa iye komanso chikhululuko cha Allah عَزَّوَجَلَّ chikhale pa ife popanda mlandu pachifukwa cha iye.

Okondedwa Abale anga Asilamu! Zomwe zafotokozedwa posachedwapa zawonetsa kuti munthu amene angakhale ndi chisangalalo chifukwa cha Dzina loyera la Allah عَزَّوَجَلَّ, munthuyo amachoka mdziko lino la pansi pa mthunzi wa chisoni, ndipo imfa imamubweretsera iye uthenga wa chikhululuko ndi kukhululukidwa. Chisoni cha Allah

عَزَّوَجَلَّ ndi chachikulu ndi chopanda malire. Ngakhale ochimwisitsa akhoza kukhululukidwa chifukwa cha zochita zabwino zimene zimawoneka zazing'ono.

Chisoni cha Allah عَزَّوَجَلَّ chilibe mtengo (sichigulitsidwa) Chisoni Cha Allah عَزَّوَجَلَّ chimangofuna munthu kupepesa (kulapa)

## Umboni Wa Tsiku La Chiweruzo

Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza kuti; pofuna kutambasula kupambana kwa بِسْمِ اللّٰه komanso ubwino wake; Amene adalemba Tafsir Azizi adanena kuti padali

Wali wa Allah عَزَّوَجَلَّ amene adapanga chikonzero chake cholemba بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ iyeyo asadamwalire. Chikonzekerochi chidalembedwa pa pepala limene lidaikidwa pansi pa chofunda chake. Atafunsidwa za zimene adapanga, mkuyankha kwake Wali adati, Patsiku la chiweruzo izi zidzakhala umboni wanga olembedwa umene udzandithandize popempha chisoni cha Allah عَزَّوَجَلَّ. *(Tafsir-e-Na'imi, vol.1, p. 42)*

Chisoni cha Allah عَزَّوَجَلَّ chikhale pa iye komanso chikhululuko cha Allah عَزَّوَجَلَّ pa ife popanda mlandu uliwonse pachifukwa cha iye.

*Chuma cha dziko lapansi komanso moyo wina pambuyo pa moyo uno chidzapita kwa inu. Werengani بِسْمِ اللّٰه*
*Allah akafuna, malo anu ofikira adzakhala Paradiso- werengani بِسْمِ اللّٰه*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Chitetezo Kuchokera Kuchilango

Zanenedwa mu Durr-e-Mukhtar, buku lodziwika bwino pa Fiqh ya Hanafi kuti munthu wina adaika chikonzero chakuti pamtima ndi pamphumi pake padzalembedwe بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم pambuyo pakumwalira kwake. Munthuyu atamwalira chikonzero ndi malingaliro ake zinakwaniritsidwa.

Masiku ochepa munthuyu atamwalira, munthu wina wake adamulota iye (wakufayo) kutulo ndipo adamufunsa kuti afotokoze mmene ankamusungira. Iye wakufayo adayankha; 'Nditayikidwa mmanda, Angelo azilango adabwera koma ataona بِسْمِ اللّٰه

atalembedwa pa mphumi panga.' Angelowo adayankhula kuti, 'wapulumutsidwa kuchokera ku chilango' *(Durr-e-Mukhtar, vol. 3 p. 156)*

Chisoni Cha Allah عَزَّوَجَلَّ chikhale pa iye komanso Allah عَزَّوَجَلَّ atikhululukire machimo athu popanda kutiwerengera pachifukwa cha iye.

## Kodi بِسْمِ اللّٰه Angalembedwe Bwanji Pa Sanda

Okondedwa Abale anga Achisilamu! Msilamu akamwalira, muzilemba بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndi mawu ena oyera pa mphumi pake ndi mbali zina. Kukhala tcheru pazimenezi kungathe kubweretsa makhululuko kwa munthu amene wamwalira. Kuwonjezera pamenepo, ntchito yabwino yakukhudzidwa kwanu ndi munthu omwalirayo, zikhozanso kubweretsa makhululuko kwa inu anthu amoyo.

Allamah Shami' رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza kuti; Ndizothekanso kuti بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndi لَآ اِلٰهَ اِلَّا اللّٰهُ مُحَمَّدٌ رَّسُوْلُ اللّٰه zilembedwe pa mphumi komanso pa mtima pa munthu omwalirayo mwandondomeko imeneyi (بِسْمِ اللّٰه pa mphumi pomwe Kalimah ilembedwe pa mtima.) Allamah Shami (adanena kuti; 'ndizothekanso kuti بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndi Laa ilaaha illallahu Muhammadur Rasullallah kuti zilembedwe pa nkhope (chipumi) komanso pa mtima pa munthu omwalra mwandondomeko yomwe yatchulidwa (بِسْمِ اللّٰه pa chipumi koma Laa illaaha pa mtima).

Allamah Shami (adanena kuti; 'ndizothekanso بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndi Laa ilaaha illallah Muhammadur Rasulullah kuti zilembedwe pa nkhope(chipumi) komanso pa mtima pa munthu omwalira mwandondomeko yomwe yatchulidwa (بِسْمِ اللّٰه pa chipumi koma Laa ilaaha pa mtima). Lembani zimenezi ndi chala cha mkombaphala osati inki, pambuyo poti omwalirayo wasambitsidwa koma asanavekedwe sanda. *(Rad-ul-Muhtar, vol. 3, p. 157)*

Sizofunikira kuika zizindikiro za mkalembedwe. Ndizovomerezeka kuika Shajarah ndi Ahd Namah mdzenje (mmanda). Zili zofunikira kuika mpata ku khoma la kutsogolo koika nkhope ya munthu womwalira poyang'ana ku Qiblah kenako ndikuika Shajarah ndi Ahd Namah mdzenjemo.

Zikunenedwa mu Durr-e-Makhtar kuti sichidangokhala chilolezo chokha kuika cholemba Ahd Namah pa sanda, komanso pali chiyembekezo cha chikhululuko kwa munthu womwalira potengera ubwino wa zolembazi. *(Bahar-e-Shariat, vol.4, p.108)*

## Kuperekedwa Kwa Chikhululuko

Pa tsiku la chiweruzo, Angelo a chilango adzamugwira munthu. Angelowa adzalamulidwa kuwunguza thupi la munthuyu kuti apezemo ntchito zabwino. Choncho, Angelowa adzafufuza thupi lake lonse koma osapeza ntchito iliyonse yabwino kenako adzamufunsa munthuyo kuti awonetse lirime lake ndicholinga chofuna kupezamo ntchito zabwino. Pamene munthu adzawonetse lirime lake, Angelo adzawona بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم litalembedwa mmalemba oyera pa lirime lake. Nthawi yomweyo, zidzalengezedwa kwa iye ponena kuti; 'Pita! Lero takukhululukira machimo ako.' *(Nuzha-tul-Majalis, vol.1, p.25)*

Allah عَزَّوَجَلَّ amuchitire iye Chisoni ndi kutikhululukira ife tonse popanda kutiwerengera zochimwa zathu.

O, inu ochimwa! Musadandaule! Musadandaule! Lowani ku Janna ya Paradiso poika maso anu pa Chisoni cha Allah.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Okondedwa Abale anga Achisilamu! Ndichisomo cha Allah عَزَّوَجَلَّ kuti Amamukhululukira amene wamufuna. Popanda chikaiko kuti munthu okhululukidwayo ayenera kuti adawerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم. kuchokera pansi pa mtima, zimene pambuyo pake zamuthandiza iye mwini, pokhala kuti ntchito yomwe imawoneka ngati yaing'ono ikagwiridwa kuchoka pansi pa mtima imasanduka kukhala ntchito yaikulu.

Mtumiki wa Chisoni, mkhalapakati wa Ummah, صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adanena kuti; " اَخْلِصْ دِيْنَكَ يَكْفِكَ الْعَمَلُ الْقَلِيْلُ" 'khalani odzipereka mu chipembedzo chanu, ngakhale ntchito yaing'ono idzakhala yokwanira kwa inu!! *(Al-Mustadrak, vol. 5, p. 435, Hadith 7914)*

Hujjat-ul-Islam, Imam Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adabwereza mawu oyankhulidwa ndi munthu oyera mtima ponena kuti; 'kudzipereka ngakhale kwa nthawi yochepa kumakhala maziko akukhulukidwa machimo ndi Allah عَزَّوَجَلَّ, koma kudzipereka kuchoka pansi pa mtima kumakhala kosowa kwa anthu.' *(Ihya-ul-Ulum, vol. 4, p. 399)*

## Zizindikiro Za Ntchito Yodzipereka Kuchoka Pansi Pa Mtima

Ophunzira a Sayyiduna Isa عَلَيْهِ السَّلَام adamufunsa iye (Yesu) kuti; 'kodi ndi ntchito iti yomwe ili yodzipereka kuchokera pansi pa mtima?' Sayyiduna Isa (Yesu) عَلَيْهِ السَّلَام adawayankha ophunzira ake ponena kuti; 'ntchito yodzipereka ndi yomwe munthu amagwira pofuna kumusangalatsa Allah عَزَّوَجَلَّ ndipo munthuyo amadana nazo kuti anthu adzimuyamikira chifukwa cha ntchitoyo.' *(Ihya-ul-Ulum, vol. 4, p. 403)*

Allah عَزَّوَجَلَّ akhale ndi Chisoni pa iye komanso atikhululukire ife tonse popanda kuwerengedwa pa chifukwa cha iye.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب　　صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

O, Allah عَزَّوَجَلَّ, pa chifukwa cha Mtumiki wanu odzipereka, Sayyiduna Isa (AS) Allah عَزَّوَجَلَّ, mutikhululukire popanda zifukwa zathu koma chifukwa cha chisoni chanu Amin!

Kalanga ine! Zomvetsa chisoni! Mwachangu tikugwa mu dzenje la chiwonongeko chifukwa cha zolakalaka za mtima ndi satana! Kalanga ine! Mitima yathu siimakhala yokhutitsidwa pokhapokha ntchito zathu ndi zachipembedzo zitakhala zoyamikidwa ndi anthu ngati njira imodzi yotilimbikitsa.

*Ntchito yanga iliyonse ikhale yofuna kukusangalatsani O, inu a mphamvu zonse.*

*Ndidalitseni ndi chuma chodzipereka.*

## Ma Dua Osavuta Pofuna Kuchotsa Zovuta

Sayyiduna Ali رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ adafotokoza kuti Mtumiki oyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adanena kuti; 'O, Ali! رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ kodindisakuuze mawu amene uyenera kunena pa nthawi ya zovuta?' Sayyiduna Ali رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ adamuyankha mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم,' Eya, ndiuze Mtumiki! chonde. Ndikupempha moyo wanga utaperekedwa nsembe chifukwa cha iwe!

Ndaphunzira zambiri zabwino kuchokera kwa iwe! kenako Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adamuuza Ali motere; 'nthawi zonse ukakumana ndi zovuta, uzinena izi;

بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْمِ وَلَاحَوْلَ وَلَا قُوَّةَ اِلَّا بِاللّٰهِ الْعَلِيِّ الْعَظِيْم

## Kuchotsa Zovuta

Okondedwa Abale Achisilamu! pamene mukukumana ndi zovuta monga matenda, ngongole milandu ku khoti, kuvutitsidwa ndi m'dani kusowa ntchito, zovuta zongobwera mosayembekezera, kutaika (kusowa) kwa chinthu, kaya mwakhumudwa kapena mwamemyedwa ndi munthu wina wake, kapena mwapunthwa pachina chake, kapena mwakwama mumdipiti wa magalimoto, kapena mwataya chuma komanso sizidayende pa malonda, kaya mwaberedwa mwina galimoto kumene yawonongeka, mwachidule, ngati muli ndi vuto lalikulu kapena laling'ono, khalani ndi chizolowezi chonena بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْمِ وَلَاحَوْلَ وَلَا قُوَّةَ اِلَّا بِاللّٰهِ الْعَلِيِّ الْعَظِيْم. Malingaliro abwino amafikitsa komwe munthu walinga kutanthauza kuti, ngati mawuwa atanenedwa ndi chikhulupiliro chozama, zidzakuthandizani inu mu chifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ.

Ntchito ina yomwe mungapange pofuna kuthetsa mavuto ndiye kusamba musadapite ku pemphero la Ijumah, kuvala zovala zoyera bwino (zopanda utchisi) kenako munene يَـا اَللّٰهُ kokwana zikwi ziwiri (200) pomwe muli panokha (powonjezera ndi Salat Alan-Nabi katatu pachiyambi ndi pamapeto pa ya Allah) Ngakhale vuto lanu litakhala lalikulu bwanji, vutolo lidzatha ndithu, ndipo pazofunika zomwe munthu angafune, zidzakwanilitsidwa, mwa chifuniro cha Allah عَزَّوَجَلَّ.

Ndi madalitso opanga Dua pamodzi ndi Akakomnda a Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم mu nyengo ya Madani Qafilah odzadzidwa ndi Sunnah ku Dawat-e-Islami, mavuto osawerengeka a Abale athu achisilamu adathetsedwa.

## Moyo Watsopano

Ogwira ntchito wina adalowetsedwa m'chipatala kuti akachiritsidwe ku vuto la impso. M'phwake oipa makhalidwe adafika kudzamuwona kuchipatala odwalayu. Atawaona atsibweni ake ali mu nyengo yoopsa ya matenda awo, mnyamatayu adathedwa nzeru ndipo adayamba kutulutsa misonzi mmaso mwake. Iye adamvapo kuti ma Dua

apangidwa moni komano ya Madani Qafilah yozadzidwa ndi Sunnah ku Dawat-e-Islami, amalandiridwa. Choncho naye adayenda ndi Madani Qafilah kumene adapanga Dua ya misonzi pofuna machiritso a atsibweni ake.

Pamene adabwelera kunyumba kwawo adali odabwitsidwa kuwawona atsibweni ake amene pa nthawiyi adali atachira ndipo atatuluka kuchipatala kuja, ndipo adali akuyenda kupita ku mzikiti kuti akapemphere! powona zochitika zachisonizi, mnyamata uja adalapa machimo natenga moyo okongola wa Madani ku Dawat-e-Islami!

Matenda adzachiritsidwa, yendani ndi Madani Qafilah. Mavuto adzathetsedwa, yendani pamodzi ndi Madani Qalifah.

Mitambo ya zodandaula idzachotsedwa, yendani pamodzi ndi Madani Qalifah.

Mvula ya chimwemwe idzagwetsedwa pa inu, yendani pamodzi ndi Madani Qafilah. Dua yonenedwa kuchokera pansi pa mtima siingakanidwe ndi Allah عَزَّوَجَلَّ. Dua iliyonse yopangidwa kwa Allah عَزَّوَجَلَّ, ndiyosakaikitsa kulandiridwa. Allah عَزَّوَجَلَّ wachisoni adatsimikiza.

وَقَالَ رَبُّكُمُ ادْعُوْنِیْۤ اَسْتَجِبْ لَكُمْ ؕ

**Ndipo mbuye wanu walengeza 'Pemphani (pempherani) kwa ine, ndipo ndidzayankha mapempho anu!**

*(Surah A-Mumin, vesi 60)*

## Chinyengo Cha Satana

Mopanda chikaiko, Allah عَزَّوَجَلَّ walengeza Mu Quran yoyera ponena kuti; 'pemphani kwa ine, ndipo ndidzayankha mapemphero anu! Komatu nthawi zambiri mapemphero athu amaoneka kuti sayankhidwa. Mwachitsanzo munthu akupempha kuti apeze ntchito pa kampani kapena bungwe koma zolakalaka zake osakwaniritsidwa (pachifukwa chimenechi zimaganiziridwa kuti pemphero lake silinayankhidwe)

## Machiritso A Chinyengo Satana

Kusamvetsa zokhudza tanthauzo la kukwaniritsidwa kwa pemphero zimamutengera

munthu ku chinyengo cha satana. Palibe chikaiko pa nkhani ya kukwaniritsidwa kwa pemphero. komabe pemphero likhoza kukwaniritsidwa mu njira zosiyanasiyana zitatu mwa izo zatchulidwa mmunsimu.

1. (Nthawi zina) zomwe opempherayo akufunsa sizimaperekedwa kwa iye pachifukwa choti zopemphazo sizabwino kwa iyeyo (opempherayo), kuchita kuti Allah عَزَّوَجَلَّ wachisoni amafunira akapolo Ake zabwino zokha zokha.

وَعَسٰۤى اَنْ تَكْرَهُوْا شَیْــٴًـا وَّ هُوَ خَیْرٌ لَّكُمْۚ

وَعَسٰۤى اَنْ تُحِبُّوْا شَیْــٴًـا وَّ هُوَ شَرٌّ لَّكُمْؕ وَ اللّٰهُ یَعْلَمُ وَ اَنْتُمْ لَا تَعْلَمُوْنَ (۲۱۶)

**'Ndipo mwina mungachide chinthu pomwe icho chili chabwino kwa inu. Ndiponso mwina mungakonde chinthu pomwe icho chili choipa kwa inu, ndipo Allah عَزَّوَجَلَّ akudziwa pomwe inu simudziwa'**

*(Surah Baqarah vesi 216)*

2. (Nthawi zina) Mavuto aakulu atha kumuwonekera munthu opemphera koma munthuyo ali otetezedwa ndi Allah عَزَّوَجَلَّ wapamwambamwamba chifukwa cha ubwino wa pemphero lake limene kungowona chabe zimakhala ngati zosakwaniritsidwa kwa iye. Mwachitsanzo, munthu akadavulalala phazi pa ngozi ya njinga ya moto pambuyo pa pemphero la Maghrib pa tsiku la Sabata. Pambuyo pa pemphero la Asr tsiku la sabata, munthuyo adapanga Dua. 'Yaa Allah wakuti wakuti ali ndi ngongole yanga ya ndalama yokwana 1000 Rupi. Chonde abweze ndalama yanga! 'Pambuyo popemphera pemphero la Maghrib, munthuyu afika kunyumba ya munthu wa ngongoleyu osachita ngozi koma wangongoleyu sadakwanitse kumubwezera ndalama yake ija (1000 Rupi). Mmaganizo ake mwini ndalamayo adaganiza kuti pemphero lake silidayankhidwe, koma zoona zake nzakuti munthuyu sakuzindikira kuti chifukwa cha madalitso a pemphero lake, limene likuwoneka ngati silinalandiridwe kwa iye, munthuyu watetezedwa ndi pemphero lomwelo kuchokera ku mavuto omwe akadachitika ovulala phazi lake pa ngozi ya njinga yamoto pamene adali pa ulendo opita ku nyumba ya munthu wa ngongole.

3. (Nthawi zina) Zimene opempherayu akupempha siziperekedwa kwa iye koma mphoto yochuluka idzaperekedwa kwa iye mmoyo winawo uno ukadzatha. Zatchulidwa mu Hadith ya Madalitso kuti; 'Mmoyo umene ukubwerawo, pamene munthu adzawone

mphoto za mapemphero ake amene sanayankhidwe pa dziko la pansi, adzalakalaka munthuyo, zikadakhala bwino (kuti mapemphero anga onse asayankhidwe pa dziko lapansi ndipo mphoto zonse zikadangosungidwa konkuno kukonzekera moyo uno pambuyo pa moyo opita (wadziko lapansi) *(Alisan-ul-Wia, p. 37)*

Zatchulidwanso mu Hadith ya Madalitso kuti, 'Makomo a ku Paradiso adzatsekulidwa kwa munthu amene wadalitsika kupanga mapemphero.' *(Alisani-ul-Wi'a, p. 141)*

## Kakonda Wa بِسْمِ اللّٰه

Mlaliki nthawi ina yake amalongosola za kupambana kwa بِسْمِ اللّٰه pakati pa anthu otsatira. Pa malopa padalinso mtsikana amene Saadali Msilamu. Atasangalatsidwa ndi zabwino za بِسْمِ اللّٰه, mtsikana yemwe saadali Msilamuyu adalowa Chisilamu nayamba moyo wa chizolowezi chomanena بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم akamagona, kuyenda, kukhala, kugwira ntchito za mnyumba mwawo. Mwachidule, mtsikanayu adayamba kumawerenge بِسْمِ اللّٰه nthawi zonse.

Makolo amtsikanayu omwe pa nthawiyi Saadali Asilamu, sadasangalatsidwe naye mtsikanayu. Chifukwa cha udani wawo ndi Chisilamu, makolowa adayamba kumunzunza mtsikanayu ndikumamukonzera chiwembu chofuna kumupha pomunamizira zinthu zina. Tsiku lina, bambo a mtsikanayu amene ankagwira ntchito ku nyumba ya chifumu adamupatsa mtsikanayu mphete kuti akasunge pa malo otetezeka.

Mtsikanayu atawerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم adatenga mpheteyo ndikuyika mthumba mwake akuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم. Usiku utafika mtsikanayu ndikupita kokagona, bambo a mtsikanayu adaitenga mphete ija mwachinsinsi kuchokera mthumba muja ndi kukaitaya mpheteyo mu mtsinjemo, mpheteyo idamezedwa ndi nsomba.

Mmawa otsatira wa tsikuli, msodzi adaponya ukonde wake ophera nsomba mumtsinjemo ndipo zidangopezana kuti msodziyo adagwira nsomba yomwe idameza mphete ija. Msodzi uja adapereka mphatso ya nsomba ija kwa munthu uja ogwira ntchito kwa mfumu (Bambo wake wa mtsikana uja). Bamboyo adapereka nsomba kwa

mwana wake (yemwe uja) wamkazi kuti aphike nsomabyo. Mtsikana adatenga nsomba ija akuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم. Mtsikana uja adadula pamimba pa nsombayo uku akuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم, ndipo adapezamo mphete ija mmimbamo. Mtsikanayu akuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم adaikanso mphete ija mthumba lake nagawira bambo ake nsomba ija. Atamaliza chakudya idali nthawi yoti bambo ake a mtsikana uja apite ku bwalo la mfumu ndipo adamufunsa mwana wawo uja kuti apereke mphete ija. Mtsikanayo akuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم adatulutsa mphete mthumba lake ndikuwapatsa bambo ake. Atawona izi, bambo a mtsikanayu anadabwa kwambiri. Mu njira imeneyi, Allah عَزَّوَجَلَّ adamupulumutsa mtsikana yemwe adali kakonda wa بِسْـمِ الـلّٰـه kuti asaphedwe. *(Lam'an-e-Sufiya)*

Allah عَزَّوَجَلَّ apangire iye chisoni ndi kutikhululukira ifenso popanda kuwerengeredwa chifukwa cha iye!

## Kupambana Kolemba بِسْـمِ الـلّٰـه

Sayyiduna Anas رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ akufotokoza kuti Mtumiki Wa Mtendere, Mkhalapakuti wa Ummah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adanena kuti, 'amene walemba بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم mokongoletsa pofuna kulemekeza Allah عَزَّوَجَلَّ, munthu ameneyo adzakhululukidwa ndi Allah عَزَّوَجَلَّ.' *(Ad-Dur-rul-Mansur, vol. 1, p. 27)*

Olemekezeka bambo a Ala Hadrat, Shaykh Sayyiduna Naqi Ali Khan Qadiri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adamwalira pa tsiku lachinayi pa nthawi ya pemphero la Dhuhr mmwezi olemekezeka wa Dhul-Qa'ada-til- Haram mchaka cha 1297 A.H. chomaliza kulemba mmoyo mwake chidali بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْـمٰنِ الرَّحِيْم.

Pakulongosola nthawi zokhudzika mtima za kumwalira kwa bambo awo, A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه akunena motere, 'pa tsiku la kumwalira kwawo, bambo adapemphera pemphero la Fijr. Pemphero la Dhuhr lisadakwane, bambo adali atamwalira. Pamene mzimu wawo umachoka mthupi lawo, anthu onse amene adalipo pa nthawi yakumwalira kwawo adaona kuti bambo mopitilira adali akupereka salaam pomwe maso awo adali atatseka (izi zikusonyeza kuti mizimu yodalitsika ya Auliya idali kusonkhana kuwalandira bambo) mu kupuma kwawo komaliza, adayendetsa manja awo pa thupi lawo lokhala ndi Wudhu kungokhala ngati kuti adali kupanga Wudhu.

Panthawiyi adatsukanso mphuno yawo kuchokera mkati mwake. Iwowo zopanga zawo amakhala ngati akupemphera pemphero la Dhuhr koma atakomoka.

Pamene mzimu wawo odalitsika umachoka mthupi mwawo, Faqir uyu (ine) ndidali pafupi ndi mutu wawo. Ndikulumbira mwa Allah عَزَّوَجَلَّ! Kuwala kokongola kudawonekekera kwa aliyense. Kuwalaku kudayambira pa mtima (pachidali) pawo ndikuwala pa nkhope ngati kuwala kwa chiphaliwali, ngati mawunikidwe akuwala kwa chiphaliwali, ngati mawunikidwe akuwala pa kalilole. Izi zidachitika ka nthawi kochepa kenako zidasowa, ndipo mzimu wawo udachoka mthupi lawo pa nthawi yomweyo. Mawu awo omaliza kuyankhula adali ‘Allah ndipo mawu awo womaliza kulemba adali بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْم, masiku awiri asadamwalire.

Patapita nthawi, ine (A’la Hadrat) رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ndidali ndi maloto amene ndinaona Muurshid wanga olemekezeka رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, ndiye ndidafunsa, ‘olemekezeka! Muli pano?’ Iwo (Murshid) adayankha, ‘kuyambira lero (nthawi ino), ndidzakhala ndikupezeka pano’. *(Hayat-e-A’la Hadrat, vol. 1, p. 50)*

Allah عَزَّوَجَلَّ awachitire iwowo komanso atikhululukire ife popanda kutiwerengera zochimwa zathu pa chifukwa cha iwowo.

Okondedwa Abale Achisilamu! Kufuna kupeza dipo lalikulu polemba بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْم ngati kuli kotheka, munthu akakhala ndi Wudhu olembayo alembe pa pepala mokoletsa bwino malembedwe. Osalemba pamalo pamene pali podetsedwa.

Zili chimodzimodzi kuti osalemba mavesi ndi mawu mzipupa chifukwa paint ndi kulembera mawu oyera amatha kusuluka kapena kusendeka pachipupa ndi kugwa pansi (izi zikhale chimodzimodzinso mmizikiti) kulemba بِسْمِ اللّٰه kapena mawu ena oyera pa dothi kapena pansi ndi zinthu zoletsedwa popeza utumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adakaniza kutero.

## Kulemba Pansi

Mtumiki wa anthu onse, Mtendere wa mumtima ndi mmaganizo mwathu, opereka kwa opereka onse, okoma mtima صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, nthawi ina anadutsa pamalo pamene china chake chinalembedwa pansi. Mtumiki olemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم atawona zimenezi adamufunsa mnyamata amene adakhala pafupi ndi pomwe padalembedwapo, ‘kodi

ndichiyani chomwe chalembedwa apo?' Mnyamata adayankha, 'بِسْمِ اللّٰه' Mtumiki odala صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adati, 'matemberero apite kwa munthu amene wachita zimenezi. Lembani بِسْمِ اللّٰه pamalo ake oyenera (kutanthauza kuti بِسْمِ اللّٰه ikhale yolemekezeka) *(Ad Dur-rul-Mansur, p. 29)*

Tifunefune kuthekera kolemekeza zinthu zoyera chifukwa amene salemekeza zimenezi amakhala onyezeka komnso omanidwa zabwino za Mulungu.

## Lemekezani Malembo A Ziyankhulo Zonse

Okondedwa Abale Achisilamu! Malembo a chiyankhulo chilichonse asalemebedwe pansi. Anthu ena amaganiza kuti palibe chifukwa chopatsira ulemu chiyankhulo cha chizungu, uku ndikusamvetsa kwakukulu kwa anthu amene amaganiza motero. Tangoganizani ngati dzina la ALLAH عَزَّوَجَلَّ litalembedwa M'chizungu, kodi simulimekeza dzinalo? Ndithudi, dzinalo mudzalilemekeza kuchokera pansi pa mtima wanu. Ngati munthu wina wake ataponda pa dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ lomwe lalembedwa mchingerezi (Allah ateteze zimenezi) pa pepala kapena pena paliponse mwinaso munthuyo wangoganiza kuti ataye chinthu chomwe chalembedwa dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ ndicholinga chofuna kunyozetsa dzinalo, munthuyo ngati anali Msilamu ndiye kuti pazimene wachitazi apezeka kuti watuluka Chisilamu. Pachifukwa chimenechi, munthu ayenera kulemekeza malembo aziyankhulo zonse kuwonjezerapo chingerezi.

Zatchulidwa pa tsamba 396 mu (voluyomu yoyamba) m'buku loyamba la Tafsir Kabir kuti ziyankhulo zonse za dziko lapansi zili Ilhami (zovumbulitsidwa kuchoka kwa Allah عَزَّوَجَلَّ). Ndizodziwikiratu kuti kulemba pansi mawu a chiyankhulo chilichonse ndikunyozetsa chiyankhulocho. Masiku ano mawu ena amapentedwa pa mseu ndi anthu a nthambi yoona zapa nseu ndi cholinga chowawongolera oyendetsa galimoto zoyenera kuchita pa nsewu, izizi ndizolakwika. Zikadakhala bwino akadangogwiritsa ntchito zizindikiro (zikwangwani) pogwiritsa ntchito mitundu yosiyasiyana (kupatula mtundu wobiriwira). Chimodzimodzi zopondera zapakhomo zomwe zimalembedwa mawu akuti MWALANDIRIDWA, zisamayikidwe pafupi ndi pakhomo.

Chokhumudwitsa ndi chakuti masiku ano zili zotheka (zopweka) kwambiri kusalemekeza ziyankhulo. Nthawi zambiri, dzina la kampane kapena fakitale yopanga

zinthu zimalembedwa pa sanza za nsalu, nsalu zoyala pansi, pa matiresi, zokutira zovunda, nsalu zofunda, zoyala pa bedi, ndi zina.

Mayina olembedwa amalembedwanso pa zimbudzi, pa mapatapata, pa nsapato komanso pa zopondera za nsapato. Dzina la kampane limalembedwanso mmbalimbali mwa nsalu. Nthawi zina, mabuluku, zovala pogona zimasokedwa mu njira yonena kuti dzina la kampane lomwe lalembedwa mmbali mwa nsalu, limakhala kumbuyo kwa chovalacho, komwe kuli kupitiriza kusalemekeza malembo. Chinthu chodandaulitsa kwambiri zolembazi zimawonekanso pansi pa matailosi omwe ayikidwa pansi pa nyumba. (Pofuna kupewa kusalemekeza) zolembedwa pa matailosi omwe ali pansi zikhoza kuchotsedwa pogwiritsa ntchito 'Angle Grinder'. Amene amagula katunduyu wambiri akhoza kugula katunduyu popanda zolemba makamaka poyankhula ndi opanga katunduyu kuti asalembedwe koma zimatengera ndani pomapanaga maganizo ngati awa a Madani! Potengera kuthekera kochokera kwa Allah عَزَّوَجَلَّ, chilichonse ndi chotheka.

Nthawi ina yake ku Bab-ul-Madinah Karachi, Sag-e-Madinah adapwetekedwa mtima kwambiri atawona njerwa yofiira patalembedwa dzina la 'Umar' Njerwa zofiirazi zimagwiritsidwa ntchito pomanga mipanda, pansi malo osambira ndi zimbudzi. Polemba mawuwa, pali zina zoswetsa mtima zomwe ndakumbukira zidachitika mmbuyomu. Ndiloleni ndigawane nanu nkhaniyi.

## Kukumbukira Zoswetsa Mtima Za Ku Madina

Cha kummawa kwa mzikiti oyera wa Masjid-un-Nabawi, kutsogolo kwa Bab-Jibrail, kunali Njira yakale kwambiri imene imakafikira ku Jannat-ul-Baqi. Akakonda ankaitcha njira imeneyi kuti 'Njira ya Paradiso'. Malo osiyanasiyana a chikumbutso adali akupezeka kumeneko kuwonjezerapo nyumba zoyera za odalitsika akubanja kwa Mtumiki oyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Pakadali pano, njira yokoma ndi yokongola ya Madaniyi idaphwasulidwa.

Madzulo a chisangalalo m'chaka 1400A.H, Ine (olemba bukuli) ndinali kuyenda mu msewu uwu otchedwa 'msewu wa Paradiso' pamene ndinawona mawu a chi Arabu altalembedwa pa chotsekera cha dzenje. Nditayang'anira pafupi ndidaona mawu olembedwa kuti مَجَارِى الْمَدِيْنَة atalembedwa pa chotsekera cha dzenjecho. Ndinawapsopsona ndili okhudzika molemekeza mawuwa ndipo ndinamva udani

osaneneka kwa anthu opanda mwayi amene adalemba dzina la mzinda wanga wokoma ndi okondedwa Madina pa chotsekera cha dzenje. Pa nthawiyi, munthu wachikulire (wokalamba) wochokera ku Yemeni amene adandiwona ndikupsopsona mawuwa adabwera ndi kundiuza kuti ndichoke pamalopa. Ndinagwetsa nkhope yanga ndikuyenda kumapita mwa msanga. Ndidangoyenda mtunda pang'ono pomwe ndidamva munthu wina akundipatsa salaam. Nditatembenuka kuti ndiwone yemwe amandipatsa salaam, ndidadzazindikira kuti adali munthu wochokeraku ku Pakistan. Adandipeza modekha. Chodabwitsa pa nthawiyi chidali chakuti munthuyu adayamaba ndi kupepesa kwa ine ponena kuti,'chonde musaziike ku mtima kwanu zimene munthu wachikulire wa ku Yemeni wayankhula kwa inu!!'

Adapitiriza munthuyu ndi kunena kuti, 'ndapatsidwa chidwi kwambiri ndi machitidwe anu opereka ulemu ndi kulemekeza pa mzikiti uwu wolemekezeka ndi Woyeraa wa Masjid-un-Nabawi. Ndakhala nthawi zonse ndikukutsatirani komanso kuwona mayendedwe ndi machitidwe anu onse. Chonde bwerani mukhale nane pa nyumba panga.' Ine ndinayankha kuti, 'ndikuyamika Mulungu (Allah) kuti ine ndili ndi malo anga okhalako!' kenako munthuyo adati,'chonde bwerani ndi ine tidye chakudya' ine ndinamuyankha munthuyo kuti, 'pakadali pano sindikufuna kaye chakudya,' kenako munthuyo adakakamirabe ponena kuti, 'chonde landirani ndalama ngati mphatso yochoka kwa ine,' Momuyamika munthuyo ndidafotokoza kutii, 'Ine sindine munthubwosaukitsitsa, ndili nazo zofunikira zokwanira, ndiyamika Allah. Mwanjira iliyonse munthuyu adali ndi zikhulupiriro zolondola (zokhoza) ndipo adali wondikonda ine. Adali munthu wachilendo kwa ine, ndipo kuchokera pa tsiku ili pomwe tidangokumana mosayembekezera, munthuyu sindidakwanitse kukumana nayenso Allah عَزَّوَجَلَّ Amudalitse munthuyu ndi mphatso zazikulu ndi kuteteza Msilamu aliyense ku mchitidwe wonyozetsa zachipembedzo komanso atiteteze ku ntchito zonyansa za anthu onyozetsa zinthu zachipembedzo.

اٰمِيۡن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّی اللّٰہُ عَلَيۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم

Nditetezeni nthawi zonse kwa anthu onyoza za chipembedzo O, inu Amphamvu zonse! Chonde ndisadzapangeko mchitidwe wonyoza za chipembedzo.

## Mtsutso Wa Munthu Wanzeru

M'chiyankhulo chachi Arabu, liwu lakuti Madinah limatanthauza 'mzinda' choncho

palibe cholakwika chilichonse kulemba liwu la Madinah pa chotsekera cha dzenje.

## Yankho La Kakonda

M'chiyankhulo chachi Arabu, liwu lakuti (بَلَد) limatanthauza kuti 'mzinda'. Ngakhale khonsolo ya mzinda wa Madinah imatchedwa kuti Baladiyyah, ndiye chidawachititsa ndichiyani anthuwa kuti alembe dzina lokongola la Madinah pa chotsekera cha dzenje? Kupatula chiyankhulo chachi Arabu, mawu akuti 'Madinah akagwiritsidwa ntchito mchiyankhulo china chilichonse kuwonjezerapo chiyankhulo chachi Urdu, dzina lakuti Madinah lidzatanthauza Mzinda Woyera wa Madinah womwe ndi Mzinda wa Mtumiki Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

Kuwonjezera apo, akuluakulu pa maphunziro a Chisilamu anaika dzina limodzi lomwe ndi Madinah kambirimbiri kutanthauza Madina-tul-Munawwarah. Kupitirira apo, pa mabuku olembedwa okhudza mbiri ya Madina-tul-Munawwarah, akutsimikiza kuti mawu akuti Madinah amayimira mzinda odalitsika wa Mtumiki oyera Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Mwachitsanzo pa tsamba 22, Gawo loyamba la Buku lake lotchedwa Wafa-ul-wafa, Allamah Nuruddin Ali Bin Ahmad Assamhudi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza maina a madalitso a Madina-tul-Munawwarah, ndipo limodzi mwa mainawa ndi mawu amodzi oti Madinah.

Izi zili apo, mitima ya anthu okonda Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم siingavomere kulembedwa kwa liwu lakuti Madinah kapena Al-Madinah pa chotsekera cha dzenje. Kodi Al-Madinah ndi chiyani? Mitima yokhayo ya okonda Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndiyomwe ingamvetse za ulemerero wa Al-Madinah. Mtsogoleri wa okondawa, Imam wa Ahl-e-Sunnat, Mtsitsimutsi wa Chipembedzo, Maulana Shah Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza za kufunika kwa 'Madinah' m'maphatikizo amawu awa:

*Kutchulidwa kwa Madinah kwachititsa kuti mphepo ya Kuparadiso iwombe*

*Ndipo zachititsa chisoni cha m'mitima mwathu kukhala chachikulu*

Mchimwene wawo wa A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه Maulana Hasan Raza Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, wawonetsa chikondi chake cha Madinah m'mawu ake awa:

*Masomphenya anga oyera akhalabe mumtima mwanga,*

*Maganizo anga okhudza Madinah amagwira mtima wanga*

*(Zauq-e-Na'at)*

## Chinyengo Cha Satana

Ndizachidziwikire kuti ndizonyasa kupsopsona chotsekera cha pa dzenje.

## Machiritso Pa Chinyengo Cha Satana

Chotsekera chili pakamwa pa dzenje koma zonyasa zili mkati. Choncho palibe chitsimikiziro choneneratu kuti chotsekera cha pa dzenje chomwe chili chouma chili chodetsedwa chomwe chilibe chionetsero pa chilichonse chokhuza kudetsedwa kwake. Palibe Mufti aliyense wachisilamu yemwe angalengeze kuti kuchipsopsona chotsekera chimenechi mwachikondi komanso mosonyeza kudzipereka kuli koletsedwa chifukwa cha mawu akuti Al-Madina amene ali okhudzana ndi mzinda oyera wa Madina-tul-Munawwarah, ngakhale zitakhala mawuwa alembedwa kapena kuikidwa pa chotsekera cha dzenje. Ndithudi, ndi m'chitidwe wa akakonda a 'Madina' okha omwe mwachangu komanso mwachisangalaro amapsopsona mawu akuti 'Al-MAdina' omwe ali olembedwa kapena kuikidwa pa chotsekera choikidwa mu Mzinda odalitsika oyera wamtumiki olemekezeka Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. E; Akakonda a Mzinda okondedwa Madinah ndi Mtumiki wa Mzinda صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Nenani ndi chisangalaro:

*Tili ndi chikondi cha MAdinah, ndithudi In Shaa Allah tidzakhala opambana.*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Wakumwa Mowa Wakhulukidwa

Padali anthu apaubale awiri. Mmodzi wa iwo adali oyera mtima, pamene winayo adali okonda kumwa mowa. Oyera mtima nthawi ina adayitana m'bale wake okonda kumwa mowa uja ndikumulanga chifukwa cha mchitidwe wake okonda kumwa mowa. Akubwera kuchokera kwa m'baleyu, iye adagwa padziwe la madzi ndikumira, pamapeto pake iye adalowetsedwa mmanda. M'bale wake oyera mtima uja adalota usiku pomwe adawona m'bale wake omwalira uja akuyenda ku Paradiso. Modabwitsidwa, m'baleyu adamufunsa m'bale wake motere; "iwe udali chidakwa ndipo udamwalira utaledzera, zatheka bwanji kuti walowa ku Paradiso?" M'bale omwalirayu adamuyankha ponena kuti "pamene ndinkabwera utandimenya, mu njira ndidapeza kachidutswa ka pepela

komwe kadalembedwa بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم. Ndinatola ndikumeza ka pepela kameneka. Kenaka ndipamene ndinagwa pa dziwe la madzi ndikumira.

Pambuyo poikidwa mmanda Munkaar ndi Nakir adabwera mmanda mwanga ndikundifunsa mafunso. Mwaulemu ndinati "Mukundifunsa ine pamene Dzina Loyera la Mulungu wanga Okondedwa liri m'mimba mwanga!" Pamene ndinanena mawu amenewa, mawu ochokera ku malo Amseli (osaoneka) adamveka "صَدَقَ عَبْدِىْ قَدْ غَفَرْتُ لَهٗ" "Kapolo wanga wayankhula zoona. Popanda chikaiko, iyeyo ndamukhululukira." *(Nuzha-tul-Majalis, vol. 1, p. 27)*

Allah عَزَّوَجَلَّ amuchitire chisoni iye komanso atikhululukire ife popanda kutiwerengera zochita zathu pachifuwa cha iye!

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب          صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Msilamu aliyense zikanakhala zabwino kukhala mugulu la Sunnah kuphunzira ndi kuphunzitsa anthu okonda Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم pokhala limodzi ndi Dawat-e-Islami, Bungwe la dziko lonse la pansi lomwe si landale koma lopanga zachipembedzo potsatira Quran ndi Sunnah. Ndipo tonse tikadapeza mwayi okhala nawo pa maphunziro ndi misonkhano yonse yozadzidwa ndi Sunna komanso podzipereka ndi mtima onse kulimbikira pochita ntchito zolungama.

## Dipo La Chikhululuko

M'bale wa chisilamu ananena kuti "msonkhano wa Ijtima ozadzidwa ndi Sunnah wamasiku atatu wa Dawat-e-Islami, Bungwe la dziko lonse la pansi lomwe si landale koma lochita zachipembedzo potsatira Quran ndi Sunnah, unkayembekezeka kuchitika ku Bab-ul-Madinah Karachi. Zokonzekera zazikulu za Ijitma imeneyi zidali mkati kukonzedwa ndipo Sitima zapa mtunda zapadera zochokera mmizinda yosiyanasiyana zidakonzeketseredwa ndi cholinga chakuti Akakonda a Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم akakhale nawo pa Ijitma imeneyi yomwe adali kuchokera mmadera onse dziko la Pakistan.

Mmasiku amenewo, m'bale wanga adamwalira mmasiku ochepa akumwalira kwake, munthu wina ochokera m'banja lake adamuona omwalirayu m'maloto. Atamufunsa za mmene iye adaliri panthawiyi, wakufayu adayankha ponena kuti, "Ndinasungitsa malo

(mpando) apaulendo pa imodzi mwa sitima za padera dera zapamtunda ndi cholinga chakuti ndikakhale nawo pa Ijitma yozadzidwa ndi Sunna ya Dawat-e-Islami yomwe idayenera kuchitikira ku Karaachi, Allah عَزَّوَجَلَّ wandikhululukira machimo anga, chifukwa cha chitsimikizo changa chomwe chinali choonadi."

*Chisoni cha Allah عَزَّوَجَلَّ chilibe kulipira mtengo. Chisoni cha Allah عَزَّوَجَلَّ chimasakasaka chipepeso (pepani) cha munthu.*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Madalitso Pa Zolinga Zabwino

Kumbukirani kuti cholinga (Niyyah) chabwino zikutanthauza cholinga (Niyyah) chochoka mu mtima (kutanthauza kulera kwa mtima mukupanga chinthu). Ngati munthu (mwachionekele) avomera kupanga ntchito yolungama koma munthuyo alibe cholinga mumtima mwake, munthuyo sapeza dipo la cholinga. Mwachitsanzo, munthu atauzidwa kupita malo ena ake mawa ndipo munthuyo nkuyankha ponena kuti, "Inde" koma mumtima nkukhala ndi cholinga choti sapita kumeneko. Ili lidzangokhala lonjezo labodza chabe, ndipo kupanga lonjezo la bodza ndi ntchito ya Haram yomwe imamutengera ku Gahena.

Pamene Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adanyamuka kupita ku nkhondo ya Tabuk, iye Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adati, "ku Madina Tayyibah kuli anthu ena amene ali nafe nthawi zonse tikamawoloka chigwa ndikulowa mmalo ena, pofuna kukwiyitsa anthu osakhulupilira, kuwonjezera apo timagwiritsa ntchito ndalama ngati tili ndi njala, nawonso amakhala kuti alinafe pa zonsezi ngakhale kuti pa nthawiyi iwowo ali ku Madina-tul-Munawwarah". Ophunzira odalitsika رَضِىَ اللّٰهُ عَنْهُ adafunsa "Inu Mtumiki wa Mulungu صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم zimatheka bwanji zimenezi? Anthuwa salinafe limodzi!" Mtumiki okondedwa ndi odalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adati, "Anthuwa alephera kukhala nafe chifukwa cha zokakamiza zina za moyo wawo (kutanthauza kuti anthuwa akuyenera kupeza dipo lawo chifukwa adali ndi cholinga chilimba kuti atenge nawo mbali koma sadatero chifukwa ali ndi zikakamizo zina zomwe ndi zoyenera iwo kusabwera kukhala nafe). *(Sunan Kubra, vol. 9, p. 24)*

Munthu amene akugwiritsa ntchito zonunkhira pofuna kumusangalatsa Allah عَزَّوَجَلَّ, munthuyo adzafika patsiku la chiweruzo mokwanira kuti zonunkhira zakezo zidzakhala

zonunkhira koposa musk ndipo ogwiritsa ntchito zonunkhira ndi cholinga chosangalatsa ena koma osati Allah عَزَّوَجَلَّ, munthuyu adzafika pa tsiku la chiweruzo kufikira kuti fungo lake lidzakhala lonunkha kufanana ndi kununkha kwa nyama yakufa yowola *(Musannaf Abdur Razzaq, vol. 4, p. 319, Hadith 7932) (Ihya-ul-Uhim, vol. 4, p. 813)*.

Pogwira mawu a Hadith yodalitsika, m'buku lake lodziwika bwino Kimiya-e-Sa'adat, Hujja-tul-Islam, Imam Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه akunena kuti, "munthu amene akubwereka ndalama kapena china chilichonse popanda obwerekayo kukhala ndi cholinga chobweza zomwe wabwerekazo, iyeyo ndiwakuba" *(Attarghib Wattarhib, vol. 2, p. 602)*

## Malingaliro A Mulungu Obisika

Ndithudi chisoni cha Mulungu chili cha kuya komanso chopanda malire .iye(Mulumgu) ndiwodziimira payekha ndipo palibe amene akudziwa za mapulani obisika a Mulungu pa iye (mulumgu) pamene chisoni cha Mulungu chikulamulira ,Iye (Mulungu) amamudalitsa munthu ndi zabwino zodabwitsa za paradiso mogwilizana ndi kukoma kwa ntchito yomwe imaoneka ngati yaing'ono poichita, koma akufuna kumulanga munthu, Mulungu amamulanga munthu ngakhale ndi tchimo laling'ono choncho,munthu asasiye kupanga ntchito iliyonse yabwino ndipo nthawi zonse azidzitalikitsa ku machimo amtundu ulionse munthu aliyense wayenera kukhala owopa mkwiyo wa Mulumgu.

## Fanizo (Lodzutsa Tsitsi) Lodabwitsa

Allamah Abdur Rahaman Ibn Jauza رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza kuti sayyidina Hassan Basri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه nthawi ina yake adakhala pamalo ena ake pamodzi ndi anzake panthawi yomweyo gulu lina la anthu adali kukoka mtembo wa munthu amene adaphedwa malingana ndi lamulo, pamene Sayyidina Basri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adayang'ana mwachidule nkhope ya munthu ophedwayu, nthawi yomweyo adagwa pansi mkukomoka. Atatsitsimuka, munthu wina adamufunsa sayyiduna Hasan Basri za nkhaniyi, ndipo iye adayankha nati," munthu ophedwa uja nthawi ina yake adali opembedza"

Moonjeza chidwi, anthu adamupempha Sayyiina Hasan Basri ponena kuti "ya Sayyidina, (eee inu powona anthu) chonde tiuzeni ife tsatanetsatane wa nkhaniyi." olemekezeka oyerayu adafotokoza," tsiku lina munthu opembedzayu adachoka panyumba pake

kupita kukapemphera. Ali munjira munthuyo adaona mtsikana amene sadali msilamu, ndipo nthawi yomweyo adagwa m'chikondi ndi mtsikanayu. Polephera kudziletsa mamunayu adamupempha mtsikanayu kuti akwatiwe naye. Mtsikanayu adamuuza mamuna opempherayu kuti alowe chipembedzo chake (cha mtsikana). Poyambirira mamuna opempherayu adadziletsa kulowa chipembedzo cha mtsikanayu, koma pa mapeto pake iye mamuna adagonja chifukwa pofuna kutsata zosilira zake nalowa chipembedzo cha mkaziyo kusiya chisilamu.

Pamene mamunayu adamufotokozera mtsikana ofunidwayo kuti iye wavomera chipembedzo cha mtsikanayo, mtsikanayu adakwiya kwambiri ndipo adayankhula momulangiza iye mamuna ponena kuti" O, munthu watsoka, ulibe chabwino. Suli munthu okhulupilika ngakhale kuchipembedzo chako, zingatheke bwanj kukhala munthu okhulupilika kwa wina aliyense! O, munthu wa tsoka loipa iwe waika pachiopsezo kupembedza kwa moyo wako onse. Kupembedzera kwako ngakhaleso chipembedzo chako poziika mkati mwa zilakolako zako! imva izi , iweyo watuluka chisilamu pochikana  chisilamu koma ine ndavomera chisilamu posiya chipembedzo chabodza, ndikuyamika Mulungu.

Atanena izi mtsikanayo adawelenga surat Al_Ikhlas. Munthu wina adamufunsa mtsikanayu modabwa," udakwanitsa bwanj iwe kuloweza surat imeneyi pamtima?" iye adayankha," Mmaloto ndidalota nditatsala pang'ono kuponyedwa kumoto pamene bambo wina olemekezeka anabwera ndikundikhazikitsa mtima mmalo ponena kuti "usaope. Bambo uyo waikidwa kukhala chotetedzera chako (kuti usaponyedwe kumoto), mmalo mwake bamboyu adzalowa kumoto mmalo mwako!! kenako ndidaona wachikondi watsokayu akubweretsedwa kuti atengedwe ku moto mmalo mwanga. Kenako, bambo olemekezeka adatengera ine ku paradiso kumene ndidaona mawu otsatilawa atalembedwa:

يَمۡحُوا اللّٰهُ مَا يَشَآءُ وَ يُثۡبِتُ ۚۖ وَ عِنۡدَهٗۤ اُمُّ الۡكِتٰبِ ﴿۳۹﴾

**"Allah amafananiza zimene wazifuna kukhazikitsa zomwe wazifuna ndipo kwa iye (Allah) ndi komwe kuli gwero la zolembedwa zonse (malamulo)**

*(Kanz_ul-iman_Gawo13 surah Ar-Ra'd, verse 39)*

kenako bambo olemekezeka uja adandiphunzitsa ine surat ikhlas ndipo nditadzuka ndinali nditaloweza surah imeneyi pa mtima

Sayyidina Hassan Basri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه kenako adati: mtsikana wamwayiyu adakhala msilamu, koma opemphera watsoka adasanduka kukhala munthu otuluka chisilamu chifukwa chotsata zilakolako zake, ndipo lero lino waphedwa. نَسْأَلُ اللّٰهَ الْعَافِيَة Tikumupempha Allah عَزَّوَجَلَّ chitetezo chake *(Bahr_ud-Dumu, p.76)*

Okondedwa abale Achisilamu! Aliyense akhale owopa kusakhudzika kwake Allah عَزَّوَجَلَّ komanso mapulani ake obisika. Palibe wina aliyense wa ife amene akudziwa kuti mwina tidzamwalira tiri achikhulupiliro kapena ayi

Kalanga! mwa Allah! chifukwa chobadwira mdziko timakumana ndi mayesero komanso mavuto osiyanasiyana. Pa nkhani imeneyi, nyama ngakhaleso tizilombo ting'onoting'ono zili zabwino popeza izo zilibe mantha kapena nkhawa yotaya chikhulupiliro (Iman) ndikumva zowawa za imfa ndipo zilibenso nkhawa ndi mantha kuti mwina zidzakumana ndi zoopsa za mmanda, zowopsa za tsiku la chiweruzo kapena mazunzo aku moto.

**Zikanakhala kuti sindinabadwile mudziko lino. Madandaulo a mmanda ndi kudzuka kwa mmanda, zikanakhala zitatha. Kalanga ine! Mantha otaya chikhulupiriro zikundidya pang'onopang'ono ine. Zikanakhala kuti amai anga sanandibeleke ine. kalanga ine! Kuchuluka kwa machimoku komanso mantha owopa moto. zikanakhala kuti sindinali munthu mdziko muno.**

Mulungu alibe chodandaula. Nthawi zonse tizimuopa iye. Tisakhale anthu osalabadira poteteza chikhulupiliro chathu. Gulu la anthu oipa ndi gulu lowononga kwambiri pomwe gulu la anthu ochita zopembedza ndikudzipeleka komanso kulumikizana ndi anthu opembedza ndizofunika kwambir. Izi ndi zomutengera munthu ku chitetezo (mmoyo wa dziko lino komanso moyo umene ukubwera.

Aliyense amene angalowe nawo muzochita za Dawat_e_islam, bungwe la dziko lonse lomwe silipanga za ndale, koma ntchito za chipembedzo potsatira Quran ndi sunna, munthuyo nakhala olumikizana ndi bungweli mmoyo wake onse, iye adzadzadzidwa ndi chisoni kufikira kuti anthu ena adzakhala odabwa!

## Wapaulendo Wa Kumadinah

Ichi ndi chidule cha nkhani yomwe mlaliki wa Dawat-e-islam ochokela ku dera la Nayaadad (Bab-ul-madina, Karadi) adapeleka. Iye akufotokoza kuti: Bambo anga olemekezeka a zaka makumi asanu ndi awiri (70), Haji Abdur Rahim Ahari (patni) anali kumayambiliro amoyo wawo akusangalala ndi zokongola za mdziko koma kenako adadalitsidwa ndi zochitika za madani, Dawat-e-islami zimene zidasintha moyo wawo kukhala wa m'chitidwe wa ku madani.

Atatsala pang'ono kupanga mapemphero awo a Hajji achiwiri, m'chaka cha 1995, adali munthu osangalala kwambiri komanso okondwa. Nthawi ya ulendo wawo ikuyandikira chisangalalo chawo chidali chikuonjezeker. Adali otangwanika usiku wonse akukonzekera kunyamuka. Pamapeto pake, nthawi yakuti anyamuke idakwana zomwe zidaonjezera chimwemwe chiwo. Tidanyamuka ulendo opita kukakwera ndege nthawi ili 4 koloko mmamawa.

Nthawi ili cha m'ma 3 koloko mmamawa, bambo anga adaika nsalu yawo ya Ihram pambali pawo nagona m'chipinda mwawo kuti apume. Nanenso ndidalowa mchipinda mwanga kuti ndipumulenso. Sipadadutse ngakhale mphindi khumi ndi zisanu pomwe ndidamva kugogoda pa chitseko cha chipinda chomwe ndidagona. nditatsekukula chitseko, ndinawona amai anga olemekezeka ataimilira koma akuoneka ali ndi nkhope nkhawa komanso yodandaula. Mayi anga adandifotokozera kuti bambo anga adali kumva ululu waukulu mthupi mwawo. Nthawi yomweyo ndidapita kuchipinda chawo chogona ndikuwapeza bambo anga kuti adali akusisita pamtima pawo koma akumva ululu, ndidawafulumizitsa ulendo wakuchipatala kumene madotolo adatifotokonzera kuti bambo adali atadwala matenda amtima. Nkhawa zidadzadza mnyumba mwathu. Aliyense adakhudzika nkudandaula chifukwa kudwala kwawo kudafika pomwe ulendo wawo opita ku madina utakonzedwa.

Kalanga ine! ndege yopita ku madinah idanyamuka koma bambo anga sadakwanitse kupita nawo. Bambo anga adakhala mchipatala masiku okwana asanu (5) pamene abambo anga adali muchipatala adavutika matenda a mtima kokwana kanayi. Pamene bambo anga anali kuzindikira zomwe zinkachitika, sadasiye mapemphero awo chifukwa cha madalitso a madani mmachitidwe a Dawat-e-islami. Amati akangowuzidwa kuti nthawi ya mapemphero yakwana, nthawi yomweyo bambo amatsekula maso awo. Amapanga tayammum pothandizidwa ndi munthu wina napanga mapemphero awo

pogwilitsa ntchito zizindikiro za manja awo, izi amachita malingana ndi kufooka kwa thupi lawo. kenako adavutikanso matenda a mtima kufikira kuti samadziwa zomwe zimachitika.

Atamva azan kuitana kwa pemphero la Isha, adaphethira diso pang'ono, panthawi imeneyi ndidawafunsa bambo." Bambo, kodi ndikuthandizeni kupanga tayammum kuti mupemphere?" iwo adavomera ndi mutu kuyamika Mulungu. Ndidawathandiza kupanga tayammum, kenako adapinda manja awo kwinaku akupanga Takbeera (Allahu Akbar) kenako adakomokanso. Ndi nkhawa ndidatuluka panja ndikukaitana dotolo. Mosachedwa, bambo anga adasamutsidwa kupita ku chipinda cha anthu odwalika kwambiri (ICU). Patapita phindi pang'ono, dotolo adabwera ndikundiuza kuti bambo anga adali munthu wamwayi chifukwa adawerenga kalimah لَآ اِلٰهَ اِلَّا اللّٰهُ مُحَمَّدٌ رَّسُوْلُ اللّٰهِ mokweza mawu kenako adatisiya (adatsilizika) nkumwalira. (Ndithudi ife ndi a Mulungu ndipo kwa iye (Mulungu) (tonse) tidzabwelera. *(Gawo 2, surat Baqarah, vesi 156)*

Sayyid (obadwa kuchokera m'banja la Mtumiki Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi amene adasambitsa mtembo wa bambo anga olemekezeka. Bambo anga adali ndi chizolowezi chomawerenga (kukhala ndi chiwerengero cha ma Dua (kupembedzera) (Wazaif) pogwilitsa ntchito zala zawo. Atamwalira, zala zawo zidali ngati akugwilitsa ntchito kupanga ma Dua pamene adali moyo, kangapo konse tidayesetsa kuti tiwongole zala zawo, koma zidakanika popeza zala zawo zidali zikubwelera kukhala ngati akupanga ma Dua powelenga zala, chiyamiko chonse ndi cha Allah عَزَّوَجَلَّ. Abale a chisilamu ambiri adakhala nawo pa mwambo oika bambo mmanda.

Mchaka chomwecho mchimwene wanga adakonza ulendo opita kumapemphero aHajj. Iye adadalitsika ndi mwayi okapanga mapemphero a Hajj, Iye (mchimwene) adanena kuti," ku madina–tul-munawwarah, ndinapanga ma Dua okhetsa misozi kumene Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adaikidwa (m'bwalo la Mtumiki SAW) ndicholinga choti ndidziwe mmene malemu bambo anga adaliri panthawiyi. pamene usiku ndidapita kukagona, ndidalota bamboo anga olemekezeka atavala nsalu ya Ihram ndipo anabwera ndikunena kuti "ndabwera kuno ku Madinah ndi chitsimikizo chodzapanga mapemphero a umrah. Udandikumbukira ndipo ndabwera kwa iwe chiyamiko chonse ndi cha Allah عَزَّوَجَلَّ. Ndine wachimwemwe kwambiri."

Chaka chotsatira m'phwanga adaona agogo ake olemekezeka (kutanthuza malemu a bambo anga Hajj Abdur Rahim Attari) akupanga mapemphero motsagana ndi iye pambali pake mu Masjid-al-Haram kutsogolo kwa Kaabah. Atamaliza pemphero, mphwangayu adawafufuza agogo akewa koma sadawapeze.

Allah عَزَّوَجَلَّ amuchitire chisoni iye ndi kutikhululukira ife popanda kutiwerengera zochimwa zathu pa chifukwa cha iye!

**Opembedza opita ku Madinah kuchokera ku Sindh wafika ku Madinah popanda kugwiritsa ntchito njira iliyonse ya mayendedwe.**

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Allah عَزَّوَجَلَّ ndiosangalala ndi anthu amene amalemekeza Dzina Lake. Iye (Allah) amapereka chisoni chake ndi zabwino kwa anthu olemekeza Dzina Lake, komanso mapulani Ake obisika kuti akhoza kukhala osangalala ngakhale ndi ntchito yomwe ikuoneka yaying'ono yome yapangidwa ndi munthu wamachimo kwambiri komanso chidakwa. Ndipo akhoza kumudalitsa iye ndikuthekera kolapa machimo ake ndikumpanga iye kukhala oyera mtima (wali).

## Omwa Mowa Asintha Kukhala Waliy

Asadalape machimo ake, Sayiduna Bishr Hafi adali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه munthu okonda kumwa mowa. Tsiku lina adali pa ulendo opita ku malo oipa omwera mowa. Paulendo wakewo adawona chidutswa cha pepala chitalembedwa بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم. Iye adatola kachidutswaka mwa ulemu. Kenako, iye adagula zonunkhira zomwe adazipaka pa chidutswa chake cha pepala lija nayika pepala lija pamwamba mwa ulemu.

Usiku utafika munthu wina oyera mtima adalota munthu wina akumuuza kuti "pita ukamuuze Bishr kuti walipanga Dzina langa kuti linunkhire, walilemekeza ndi kuliika malo apamwamba. Pachifukwachi Ife tidzamuyeretsa iye (Hafi). Munthu oyera mtimayu atadzuka, adaganiza mwa iye yekha kuti," Bishir ndi chidakwa cha mowa; mwina ineyo sindikutha kumvetsa tanthauzo la maloto amenewa." Kenako adapanga wudhu ndikupanga pemphero la Nafl, adapita kokagonanso koma ali mtulo maloto aja

adamubweleranso, kenako adabweranso kachitatu ndi malangizo omwewo "uthenga wathu ndiwokhuza Bishr! Pita ndipo ukamuuze Bishr za uthengawu!"

Choncho munthu oyera mtimayu adatuluka mnyumba mwake akumufunafuna Sayyiduna Bishr رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ndipo iye adauzidwa kuti Bishr adali pakati pa zidakwa. Atafika pa mkumano wa zidakwa, munthu oyera mtimayu adayitana 'Bishr' koma adauzidwa ndi anthu kuti Bishr adali pa malo oyipa omwera mowa. Munthu oyera mtimayu adawauza anthu kuti," pitani ndipo mwanjira ina mukamuuze kuti munthu wina wabwera ali ndi uthenga wake ndipo wayima kunja."

Munthu wina adapita kukamuuza Bishr zimenezi. Sayyiduna Bishr Hafi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adati," mukamufunse amene wabweretsa uthengawo kuti wachokera kwa ndani?" Atafunsidwa, munthu oyera mtimayu adayankha ponena kuti, "Ndabweretsa uthenga wa Allah". Atawuzidwa zimenezi, Sayyiduna Bishr رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adachiona chinthu chachikulu kwambiri ndipo nthawi yomweyo iye adatuluka asadavale nsapato. Pakumva uthenga wa Allah iye adalapa machimo ake kuchoka pansi pa mtima wake ndipo adapezeka udindo wake pa uzimu uli pamwamba kotero adayamba kukhala osavala nsapato chifukwa chakupambana kwa mphamvu ya Mulungu yomwe idamuonekera mmoyo mwake. Ichi ndichifukwa chake Sayyiduna Bishr HAfi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adatchuka ndi dzina lakuti Hafi (kutanthauza kuti munthu oyenda osavala nsapato) *(Tazkira-tul-Auliya, p. 68)*

Allah عَزَّوَجَلَّ awachitire iwo chisoni ndikutikhululukira ife popanda kutiwerengera zochimwa zathu pachifukwa cha iwo!

## Zabwino Chifukwa Cha Kuonetsa Ulemu

Okondedwa Abale Achisilamu! Munthu wamachimo komanso chidakwa cha mowa adasandulika kukhala wali wa Allah عَزَّوَجَلَّ chifukwa cholemekezeka ndi kupereka ulemu ku chidutswa cha pepala pamene padalembedwa Dzina Lodalitsika la Allah عَزَّوَجَلَّ. Ndiye ife ochimwafe zingakanike bwanji kuti nafenso tidalitsike ndi chisomo komanso ubwino wa Allah, ngati nafenso titalemekea anthu amene m'mitima mwawo munalembedwa Dzina la Allah nakhala mmoyo wawo ali otangwanika pomukumbukira Allah nthawi zonse. Kuonjezera apo, zidzakhala zokondedwa bwanji ka Allah عَزَّوَجَلَّ ngati tikumulemekeza Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم popeza Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndiye mtsogoleri wa atumiki komanso oyera mtima onse!

Ndithudi kulemekeza dzina al munthu oyera (pa Uzimu) zimabweretsa madalitso. Sayyiduna Bishr Hafi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adapeza udindo wapamwamba wa Uzimu polemekeza dzina la Allah. Ngati ifeyo tingalemekeze dzina la Mtumiki wathu okondedwa Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم zingalephere bwanji kuti tipeze kulemekezeka? Tikamva dzina lodalitsika, ife tikapsopsona zala zathu zikuluzikulu zakumanja ndikugwira m'maso mwathu chifukwa cha kulemekeza dzinalo, kodi zingakanike bwanji kuti ife tipeze madalitso? Sayyiduna Bishr Hafi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adapaka zonunkhira pa pepala pamene padalembedwa Dzina la Allah, ndipo adayeretsedwa. Kodi titawauza (kuthira) madzi amaluwa paliponse pamene (Zikr) kukumbukiriwa kwa Mtumiki wathu okondedwa Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kukuchitika, zingalephere bwanji kuti tiyeretsedwe?

## Nyama Nazonso Zimapereka Ulemu Kwa Waliy

Sayyiduna Bishr Hafi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه nthawi zonse amayenda osavala nsapato. Pamene adali ndi moyo ku Baghdad, palibe nyama iliyonse imawonongera mmisewu ya mzindawu pofuna kulemekeza ndi kupereka ulemu ndi cholinga chakuti Sayyiduna Bishr Hafi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه asavutitsidwe pamene amayenda osavala nsapato.

Tsiku lina nyama idawonongera mu msewu; mwini wake wa nyamayi adali odandaula poganiza kuti Sayyiduna Bishr Hafi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه mwina mwake wamwalira chifukwa sizikadatheka nyamayi kuwonongera mu msewu, patapita nthawi yochepa mwini nyamayu adamva kuti oyera mtima wamkuluyi (Sayyiduna Bishr Hafi) adamwalira. *(Ahsan-ul-Wi'a, p. 137)*

Allah عَزَّوَجَلَّ amuchitire iye chisoni ndikutikhululukira ife popanda kutiwerengera zofooka zathu pa chifukwa cha iye!

## Chikhululuko Kwa Anthu A Ulemu

Atamwalira Sayyiduna Bishr Hafi, رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, Qasim Bin Munabbeh adamuwona (Sayyiduna Bishr Hafi) mmaloto ndipo adamufunsa, مَا فَعَلَ اللّٰهُ بِكَ؟ "Kodi Allah عَزَّوَجَلَّ wakuchitira zotani iwe?" Iye (Bishr Hafi) adayankha, "Allah عَزَّوَجَلَّ wandikhululukira ine ndikundiuza ine kuti,'O Bishr! Ndakukhululukira iwe ndi kuwakhululukira anthu onse amene adatenga nawo mbali pa pemphero la maliro ako.' Kenako ndinapempha kuti,' O Mbuye wanga, mukhululukirenso anthu amene amandikonda ine.' Allah عَزَّوَجَلَّ adati,'

Ndawakhululukira onse amene amakukonda iwe kufikira tsiku la Chiweruzo." *(Sharh-us-Sudar, p. 289)*

*Timamukondadi Bishr Hafi*
*In shaa Allah tidzapambana*

*Timawakondadi Auliya onse*
*In shaa Allah tidzapambana*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kupambana Kotola Mapepala Opatulika

Sayyiduna Ali Murtadhwa رَضِیَ اللّٰہ عَنْہ adafotokoza kuti Mtumiki opatulika ndi odalitsika صَلَّى اللّٰه عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adanena kuti, "Amene angatole pepala (kuchoka pomwe lagwa pansi) pomwe palembedwa dzina mwa maina a Allah, Allah adzakweza dzina la munthu ameneyo mu Iliyyin (malo aakulu kokhalako mizimu ya anthu) ndipo ndidzachepetsa chilango cha makolo ake ngakhale makolowo atakhala osakhulupirira." *(Majma'-uz-Zawaid, vol. 4, p. 300)*

## Mufti A'zam Hind Amalemekeza Mapepala Ndi Malembo

Mwana okondedwa wa Aila Hadhwrat ophunzira wachisilamu, wali wa Allah, odzipereka Mtumiki wa Al-Haj Muhamad Raza Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه otchuka ndi dzina lakuti Mufti. Azam Hind, amalemekeza mapepala ngankhale osalembedwa chilichonse komanso zilembo zonse popeza zilembozi zimagwira ntchito polemba Quran, Mahadith komanso malamulo achisilamu.

M'chaka cha 1391, AH, Iye adabwera ku Dar-ul-Ulum Rabbaniyyah Banda (India) kuti akakhale nawo pa mwambo opereka ma Degiri. Atatuluka mu galimoto kuyenda pang'ono, maso ake anawona tiziduswa ta mapepala pomwe padalembedwa chiyankhulo cha chiUrdu. Nthawi yomweyo adatola mapepalawo ndikunena kuti "Munthu ayenera kulemekeza mapepala ndi zilembo za chi Arab popeza izi zimagwiritsidwa ntchito posonkhanitsa Quran yoyenera, ma Hadith odalitsika ndi kumasulira (kufotokozera) mabuku amenewa. *(Mufti A'zam ki Istigamat –o- Kalamati, p. 24)*

Timupemphe Allah عَزَّوَجَلَّ kuti amuchitire chisoni iye ndikutikhululukira ife popanda kutiwerengera zochita ztu pachifukwa cha iye.

## Mufti A'zam Hind رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه Atonthoza Anthu Ovutitsidwa

Okondedwa abale Achisilamu! Mwakwanitsa kuzindikira chidwi cha Mufti A'zam Hind pofuna kulemekeza zolembedwa zachisilamu ndi zina. Munthu amene akulemekeza malembo (zilembo) ngakhalenso mapepala osalembedwa kwa iye adzakhala ndi kudziwa kofanana pofuna kuwalemekeza Asilamu ena!

Mufti A'zam Hindi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه sadasiye mwayi uliwonse pofuna kotonthoza ndi kukhudzidwa ndi Asilamu ovutitsidwa. Nthawi zonse ankapewa zochita zoswetsa mitima ya Asilamu ndipo adali okonzeka kwambiri pofuna kuwathandiza Asilamu. Akadalephera bwanji kuchita zimenezi popeza Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amene adali. odzipereka wake adanena kuti "خَيْرُ النَّاسِ اَنْفَعُهُمْ لِلنَّاسِ Nali fanizo lapaderadera lowonetsa mwachidule kagwiritsidwe ntchito ka Hadith imeneyi ku Madani. "*(Al- Jami – us –Saghir, p. 246, Hadith 4044)*

Mufti A'zam Hind رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adayitanidwa kumwambo wapadera pa Madrasah Faiz –ul– Ulum (Jamshedpur, Tharkhand India. Mwambowu utatha adatuluka m'madrasah kuti azibwerera. Panthawiyi atangokwera kumene mu rickshow (chokwera cha matayala atatu) kuti azipita kumalo okwera sitima yapamtunda, apa ndipamene munthu wina adafika ndi kumpempha, "olemekezeka! chonde ndipatseni Ta'wiz pamavuto anga akutiakuti". Otsogolera Madrassah, Allamah Arshad – Ul –Qadri adamuuza munthu ofuna nthandizoyo kuti "Sitima yapamtunda yatsala pang'ono kunyamuka ndiye iwe ukubwera panopa kudzatenga Ta'wiz!

Mufti A'zam Hind رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adamuletsa Allamah Arshad – ul – Qadir (زِيْدَ مَجْدُهٗ) kumukaniza munthuyo zomwe ankafuna. Allamah Arshad –ul– Qadir adapempha," olemekezeka! sitima idzakhala itanyamuka! Pakumva zimene Mufti A'zam Hind رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adayankha, zikusonyeza kumuwopa Mulungu komanso kudzipereka mchikhumbokhumbo chake chofuna kutonthoza kuvutitsidwa kwa Ummah ndipo ndizoyenera kuti zimenezi zilembedwe muzilembo zagolide. Iye (Mufti A'zam Hind) adayankha kuti ilekeni sitima yapamtunda kuti inyamuke, ine ndikwera sitima ina. Ngati angadzandifunse pa tsiku la chiweruzo kuti ndichifukwa ninji sindidamunthandize wakuti ndi wakuti pamene mwa

akapolo ake amene adali m'zovuta, ndidzayankha zofuna ine? Atanena zimenezi, katunduwawo yense adatsitsidwa kuchokera mu rickshaw. *(Mufti A'zam ki istigamat –o– karamat, p. 121)*

Allah عَزَّوَجَلَّ amuchitire chifundo iye ndikutikhululukira ife zochimwa zathu posatiwerengera chifukwa cha iye!

Nkhaniyi inalembedwa Allamah Arshad –ul- Qadiri alimoyo popeza mawu muchi Arabu amakambidwa kwa munthu.

## Madalitso A Pepala Lopatulika

Zifukwa zomwe zidapangitsa Sayyiduna Mansur Bin Ammar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه kuti alape ndizakuti tsiku lina adapeza chidutswa cha pepala patalembedwa بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم lili pansi. Atasowa malo oti asungirepo pepalari, iye adangoganiza zolimeza pepalali ndicholinga choti pepalari lisanyozeke. Mu usiku otsatira Mansur Bin Ammar adali ndi maloto momwe adaona munthu wina akuti "Chifukwa cha madalitso a ulemu umene udaonetsa posamalira pepala lopatulika, Allah wakutsekulira makomo a nzeru". *(Risala –tur- Qushayriyyah, p.48)*

Allah عَزَّوَجَلَّ amuchitire chisoni ndikutikhululukira ife popanda kutiwerengera zolakwa zathu!

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب      صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Okondedwa abale Achisilamu, kodi mudaona munthu amene watola mwaulemu kachidutswa kapepala komwe kalembedwa بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم. Munthuyo adadalitsidwa ndi Allah عَزَّوَجَلَّ polapa machimo komanso popatsidwa udindo wa Wilayah ngankhalenso udindo wa Awtad."

Zikufotokozedwa mu Bahjat-ul-Asrar kuti Sayyiduna Shaykh Abu Bakr Bin Hawar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adanena kuti, "Pali ma Awtad okwana asanu ndi awiri aku Iraq.

1. Sayyiduna Shaykh Ma'ruf Karki رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه
2. Sayyiduna Shaykh Imam Ahmad Bin Hanbal رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه

3. Sayyiduna Shaykh Bishr Hafi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه
4. Sayyiduna Shaykh Mansur Bin Ammar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه
5. Sayyiduna Shaykh Junayd رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه
6. Sayyiduna Shaykh Sahl Bin Abdullah Tusatari رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه
7. Sayyiduna Shaykh Abdul Qadir Jilani رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه

(Okondedwa wathu Ghaus-e-A'zam رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anali asanabadwe pa nthawi imene Sayyiduna Shaykh Abu Bakr Bin Hawar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adayankhula zimenezi. Choncho, anthu atamva nkhani ya nseri imeneyi adanfunsa) "Kodi Abdul Qadir Jilani ndi ndani?" Sayyiduna Shaykh Abu Bakr Bin Hawar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adayankha kuti," Iyeyo (Abdul Qadir Jilani adzakhala Ajami Sharif (Ma Arabu amatchula mibadwo ya Mtumiki Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuti 'Sharif' ndi 'Habibi', pamene dzina lakuti 'Sayyid' limagwiritsidwa ntchito mmalo mwakuti 'Bwana'. ndiye apapa chimene chikutanthauzidwa ndi chakuti Abdul Qadir Jilani adzakhala Sayyid amene si wachiArabu ndipo adzakhala mu Baghdad. Adzabadwa mchaka zana la chisanu cha Hijiri (5th century) ndipo adzakhala mmodzi mwa Siddiqin (Kutanthauza kuti Udindo Wa Pamwamba Kwambiri mwa Oyera Mtima opembedza). Ma Awlâd ndi amene ali ndi ulamuliro pa dziko lapansi komanso ma Qutub adziko lapansi. *(Bahjat-ul-Asrar, p. 385)*

Allah عَزَّوَجَلَّ awachitire chisoni iwowo komanso atikhululukire popanda kutiwerengera zolakwa zathu pachifukwa cha iwo!

Qutub ndi Wali wa Allah amene ali ndi ulamuliro pa kayendetsedwe ka za uzimu kumbali ina ya dziko kapena mu mzinda mwinaso mmalo ena.

## Fanizo La Ma Dua Anayi

Potengera madalitso akulemekeza chidutswa cha pepala pamene palembedwa بِسْمِ اللّٰه, Sayyiduna Mansur Bin Ammar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adakwezedwa kufika mu Udindo wa Oyera Mtima pa Uzimu omwe ndi akulu akulu kwambiri. Modzipereka adali kufalitsa uthenga powaitanira anthu kuti akhale olungama ndipo anthu osawerengeka adali kubwera kudzamvetsera uthenga opereka ulemu mu majlis ake a anthu, munthu wina amene adali opempha adapempha kuti apatsidwe Dirham zinayi. Sayyiduna Mansur Bin Ammar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adalengeza, "Ngati munthu wina angapereka Dirham zinayi kwa

munthuyu, ine ndzamubwenzera anayi. Panthawi yomweyonso kapolo adali kudutsa pamalopo. Pamene kapoloyo adamva mawu a chisoni a munthu oyera Mtima nayenso nthawi yomweyo adabwera ku majlis (gulu la anthu) kuja ndikupereka Dirham zokwana zinayi kwa munthu opempha uja. Sayyiduna Mansur رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه kenako adamufunsa kapolo uja, "Ndi ma Dua anayi ati amene ungafune kuti ine ndikupatse? Kapolo uja adayankha kuti,

1. (Undipangire Dua) kuti ndichoke mu ukapolo
2. Ndilandire zabwino pamwamba pa Dirham izi
3. Ine ndi mbuye wanga (amene amandisunga mnyumba mwake) tidalitsike ndi kulapa kochoka pansi pa mtima.
4. Ine, mbuye wanga, inu ndi ena onse amene alipano akhululukidwe zolakwa zawo

Sayyiduna Mansur Bin Ammar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adakweza manja ndikupanga ma Dua amenewo. Kenako kapoloyo adachoka napita. Popeza kapolo adafika kukhomo komwe ankakhala mochedwa, bwana wake adamufunsa chifukwa chomwe chidamuchititsa iye kuchedwa. Kapolo adafotokonza zonse zimene zidachitika kwa Bwana wake. Pakumva izi bwanayo, "Kodi Dua yako yoyamba idali yotani?" kapolo uja adayankha, "Ndinapempha kuti ine ndi Bwana wanga tidalitsike ndi kulapa kochoka pansi pa mtima."

Bwanayu atangomva zimenezi, nthawi yomweyo adapempha chikhululuko kwa Allah عَزَّوَجَلَّ ponena kuti, "Ndikulapa machimo anga onse kwa Allah." Kenako Bwanayo adafuna kudziwa za Dua yachinayi. Kapolo uja adayankha, "Ndinapempha kuti ine ndi Bwana wanga, Munthu oyera Mtima, ndi anthu ena onse amene adali pa majlis pa, Allah awakhululukire machimo awo." Bwana atamva zimenezi adati, "Ndakwanitsa kupanga zinthu zitatu zomwe ndingakwanitse kutero ndi mphamvu zanga. Chinthu chachinayi chomwe ndi makhululuko kwa onse, mphamvu zanga sizingafikire kumeneko. Usiku umenewu, Bwana adalota akumva mawu onena kuti, "Wakwanitsa kupanga kufikira pomwe mphamvu zako zikufikira. Ine ndine wachisoni kwa achisoni onse; ndakhululukira iwe, kapolo wako. أَرْحَمُ الرَّاحِمِيْن, Mansur komanso onse amene adali pa majlis (za uzimu). *(Raud-ur-Riyahin, p. 222)*.

Allah عَزَّوَجَلَّ awachitire chisoni ndi kukhululukira ife popanda kutiwerengera zolakwa zathu chifukwa cha iwo!

*Chifukwa cha zotsatira za Dua zomwe Mansur adapanga*
*Tsogolo la zikwi za anthu (mu uzimu) zidasintha.*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Mbiya Ya Dothi Yosweka

Tsiku lina, Shaykh Sayyiduna Mujaddid Alf-e-Sani قُدِّسَ سِرُّهُ الرَّبَّانِي, oyera mtima otsatira ndondomeko ya uzimu ya Naqshbandiyyah, adawona zonyasa zikutulutsidwa m'mbiya yaikulu yosweka yomwe idali m'chimbudzi. Mbiyayi imagwiritsidwa pokolopera m'chimbudzimo. Atayandikira, adakhudzika powona kuti pa mbiya paja palembedwa dzina la Allah. Adawerama ndi kunyamula mbiya kenako adamufunsa wa ntchito wake kuti amubweretsere chigubu cha madzi ndipo adagwiritsa ntchito kutsuka mbiyayo ndi manja ake odalitsika ndi kuyiyeretsa mokwanira. Kenako adaikulunga mbiyayo mu nsalu yoyera ndi kuyika pamwamba pa ulemu. Oyera mtima olemekezekayu ankamwa madzi kuchokera mu mbiya imeneyi.

Tsiku lina Shaykh Sayyiduna Mujaddid Alf-e-Sani قُدِّسَ سِرُّهُ الرَّبَّانِي adalandira uthenga (Ilhaam) ochokera kwa Allah, "Chifukwa chakuti walemekeza dzina langa, inenso ndidzakweza dzina lako pa dziko lapansi komanso pambuyo pa moyo uno. Shaykh Sayyiduna Mujaddid nthawi zambiri ankakonda kuyankhula mawu awa; "Udindo waukulu wapamwamba omwe ndaupeza pa chipembedzo (uzimu) chifukwa cha kulemekeza dzina la Allah, sindikanakwanitsa kuupeza ngakhale ndikanapembedza modzipereka kokwanira mazana azaka. *(Zatengedwa kuchokera ku Hazarat-ul-Quds, Duftar duwum, p. 13, mukashafa nambala 35)*.

## Kulemekeza Pepala Losalembedwa

Opembedza oyera mtima wamkulu otsatira ndondomeko ya uzimu ya Naqshbandiyyah, Sayyiduna Shaykh Ahmad Sarhindi odziwika ndi dzina lakuti Mujaddid Alf-e-Sani قُدِّسَ سِرُّهُ الرَّبَّانِي amalemekezanso mapepala osalembedwa. Tsiku lina adali kupuma pa bedi

lake pamene mwadzidzi adatsika mwankhawa ndikunena kuti, "Zikuoneka ngati pansi pa bedilo pali zidutswa za mapepala." *(Zubdaf-ul-Maqamat, p. 192)*

## Osakankha (Osamenya) Mapepala Ndi Mapazi Pamene Mukuyenda

Okondedwa abale Achisilamu, fanizo limene lakambidwa m'mwambamu likusonyeza kuti munthu aliyense ayenera kulemekeza mapepala ngakhale amene ali osalembedwa popeza Quran Yoyera, Mahadith komanso malamulo ena achisilamu amalembedwa pa mapepala omwewo. Kuyamikidwa konse ndi kwa Allah! Fanizo ili likuwonetsa poyera chozizwitsa cha Sayiduna Mujaddid Alf-e-Sani قُدِّسَ سِرُّهُ الرَّبَّانِي. Adazindikira kupezeka kwa kachidutswa ka pepala pansi pa bedi popanda kuliwona pepalalo ndipo anatsika pa bedi pofuna kupereka phunziro lofuna kulemekeza zidutswa za mapepala.

Zikunenedwa mu Bahar-e-Shariat, "Ndizoletsedwa kupanga Istinja 1 (kudzisamalira pambuyo pogwirita ntchito chimbudzi) ndi pepala ngakhale pepalalo litakhala losalembedwa, ngakhale pa pepalapo patalembedwa dzina la Abu Jahl, kapena ndina la munthu wosakhulupirira." *(Matbu'ah Madina-ul-Murshid, gawo Z, p. 114)*

kuti mudziwe zambiri za Istinja, werengani buku (method of Istinja, losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah) Zilembo za chiArabu zomwe zili m'mawu akuti Abu Jahl ali ndi zilembo Alif; Baa; Wawu; Haa, ndi Laam, zilembo zomwe zikupezeka mu Quran. Choncho, mawu olembedwawa womwe ndi Abu Jahl (osati munthuyo Abu Jahl) adzayenera kulemekezedwa munzeru zakuti sizili zololedwa kuika mawuwa pamalo onyansa kapena a utchisi kapena kupondapo. Anthu amene akugwiritsa ntchito mapepala ochokera mu nyuzipepala ngati moyikamo zinthu ayenera kutengera phunziro kuchokera ku lamulo (chigamulo) limeneli. Allah عَزَّوَجَلَّ atiteteze. Ma nyuzipepala amene amagwiritsidwa ntchito ngati matumba oyikamo zinthu amakhala kuti sakulemekezedwa mu njira zambiri. Mwachitsanzo, Mulungu atiteteze, mapepalawa ndi amene amakhala oyamba kuponyedwa mmalo otaya zinyalala zapakhomo, kenako zimapondedwa ndi mapazi mmisewu ndipo pamapeto pake mapepalawa amagwiritsidwa ntchito kuikamo nyansi ndi utchisi ndikukapezeka kumalo kotayira zinyalala.

Powonjezera apo, Allah عَزَّوَجَلَّ atiteteze, ndi makhalidwe osakhala abwino a anthu ena amene amati akamayenda mmisewu, amakankha ndi mapazi zinthu zosiyanasiyana

zomwe pali zolembedwa monga makatoni, mabokosi, manyuzipepala ndi mitundu ina ya mapepalawa. Zoona zenizeni ndizakuti mapepalawa ndi makatoni ziyenera kutoledwa ndi manja ndi kuikidwa malo oyenera pamene nzosatheka kuchitidwa chipongwe (kusalemekezedwa) kapena kuwataya mapepalawa moyenera (mwachitsanzo powataya mnyanja).

Mwa njira ina iliyonse, zili zofunika kwambiri kupewa kukankha zinthuzi ndi mapazi kapena kuziponya apa ndi apo. Chimodzi modzi zili zofunika kwambiri kupewa kutsuka kapena kuumitsa ziwiya kapena matebulo kugwiritsa ntchito manyuzipepala kapena mapepala amene Pali zolembalemba, kuumitsa mmanja, kupondapo kapena kuwayala pansi ndi cholinga chofuna kukhalapo ndi zina zotero.

## Utuchi (Zosongoledwa) Za Pensulo Ya Mtengo

Zikunenedwa m'buku la Bahar-e-Shariat kuti, "zosongoledwa za pensulo yomwe siidagwiritsidwe ntchito zikhoza kutayidwa, koma zosongoledwa zomwe pensulo yagwiritsidwa ntchito, zisataidwe pamalo pomwe zikhoza kusalemekezedwa. (Izi zikusonyeza kuti ngakhale zosongoledwa zayenera kulemekezedwa, nanga ndi chifukwa chiyani kusalemekeza cholembera kapena pensulo yogwiritsidwa ntchito?) Kuwonjezera apo, zili zonyansa (Makruh) kusanjika (kuika) chinthu china chilichonse pamwamba pa pepala lomwe palembedwa dzina la Allah. Komabe, sizili zonyasa kuika ndalama mu jumbo ngakhale maina a Allah atalembedwa pandalamapo. Kupukuta mmanja pogwiritsa ntchito pepala munthu akamaliza kudya ndi mchitidwe onyansa (Makruh) *(Bahar-e-Shariat, part 16, p. 119)*

Komabe ophunzira a Chisilamu olemekezeka adavomereza kugwiritsa ntchito mapepala a minofu pofuna kupukuta m'manja. Zili zoloredwa chimodzimodzi kugwirtsa ntchito mapepala a mchimbudzi pofuna kuumitsa malo obisika pomwe zibuluma palibe. Izi zili choncho popeza mapepala a minofu komanso mapepala amchimbudzi amapangidwa ndi cholinga chogwiritsa ntchito zomwe zatchulidwa mmwambamo (kutanthauza, kupukutira mmanja ndi kuumitsa malo obisika) osati kugwiritsa ntchito polembapo, pamene mapepala enawa ntchito yawo ndi kulembapo.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب          صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kulemekeza Ngakhale Dontho La Inki

Sayyiduna Muhammad Hashim Kishmi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti, "Nthawi ina ndinalinawo m'bwalo la Sayyiduna Mujaddid Alf-e-Sani رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه Shaykh wamkulu wa ndondomeko ya uzimu ya Naqshbandiyyah. Iye adali otangwanika ndi ntchito yake ya zolembalemba ndipo adafuna kupita ku malo opumira (chimbudzi). Adapita koma nthawi yomweyo adatuluka napempha kuti akapatsidwe chigubu cha madzi. Kenako, akutsuka chikhadabo chachala chachikulu cha dzanja lake lolemekezeka lakumanzere, adapitanso ku nyumba yolemekezeka ija (chimbudzi).

Atamaliza kudzithandiza, adatuluka ndikunena kuti, pamene ndidakhala pansi mnyumba ya ulemu (chimbudzi), ndidawona dontho la inki pa chikhadabo cha chala changa chachikulu cha nkono wakumanzere imene ndidaikapo pomwe ndimayesa cholembera (ngati chikulemba kapena ayi). Potengera kuti dontho la pa chikhadadabocho ndidaika ndi inki uja cholembera chomwe ndimagwiritsa ntchito polemba zilembo za Quran, ndinachiwona kuti kusiyabe dontholo pa chala changa kudali kusalemekeza zilembo. (Zilembo zonse za chi Arabu, zambiri mwa izo za chi Persia komanso Urdu ndi zilembo za Quran). Ngakhale ndinali kufunitsitsa kutaya madzi (kukodza) koma kupweteka kwa kusalemekeza dontho la inki zinali zazikulu kuposa kupweteka kofuna kutaya madzi. Choncho, nthawi yomweyo ndidatuluka mchimbudzi ndikuchotsa dontho la inki pa chala change. *(Zubdat-ul-Maqamat, p. 180)*

## Osamata Zikwangwani Mzipupa (Khoma)

Allah! Allah! opembedza oyera mtima mu ndondomeko ya Uzimu ya Naqshbandiyyah, Sayyiduna Mujaddid Alf-e-Sani رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه amalemekeza ngakhale dontho la inki ya cholembera, koma ifeyo machitidwe athu ndi akuti ngati dzanja lathu lapakidwa ndi dontho la inki pomwe tikulemba, zomwe timachita ndi kungosamba pochotsa inkiyo kugwera mu ngalande. Pamene cholembera kapena pensulo zafika posagwiritsa ntchito, timataya mu zotayila zinyalala kumene chili kenako cholemberacho chimakataidwa mu dzenje la zotairamo zinthu zanyasi.

Zolemba zambiri m'mabolodi ndi choko zimafufutidwa mwachangu ngakhale zolemba zopafulika monga Mahadith, mwinanso zolemba zina za wamba, popanda kusamalira ndi kulemekeza zidutswa kapena ufa (fumbi) wa Choko. Mwapoyera, kusalabadira ufulu

wa anthu, mawu osiyanasiyana, mawu achilimbikitso amalembedwa mzipupa, zikwangwani zolembedwa mosiyanasiyana kuphatikizirapo zokamba za chipembedzo, Zimaikidwa m'mabolodi akulu akulu popachika m'mwamba komanso muzipupa za kunja kwamnyumba za anthu, m'ma shopu ndi malo ena otero popanda chilolezo cha eni malowo akhala okhumudwa, nawo mchitidwe umenewu ndiye kuti zidzakhala zochitazi za Haram zolowetsa munthu ku moto.

Kuwonjezera apo, aliyense akudziwa kuti zikwangwani zoikidwa pa zipupa, zimasendeka ndi kugwa pansi mzidutswazidutswa zimene mapeto ake sizilemekezedwa kotero kuti ukaziganizira zimachititsa thupi kunjenjemera. Zikanakhala bwino kwambiri kuti mchitidwe opachika zikwangwani ndi mauthenga, zizikhala malo oyenera amene angakonzedwe m'malo momapachika zikwangwani muzipupa. Zikwangwani zonse zizichotsedwa zikamaliza kugwira ntchito yopachikidwayo. Chimodzimodzi, ma bana nawo azichotsedwa akagwiritsidwa ntchito chifukwa nawonso akhoza kugwa pansi mzidutswa zomwe zingapangitse kubalalika pansi.

## Osagulitsa Ma Nyuzi Pepala Ngati Zinthu Zosafunikira (Zinyalala)

Okondedwa Abale Achisilamu Nyuzipepala masiku ano (M'maiko a Chisilamu) zimakhala patalembedwa بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم, ma Vesi opatulika a Quran Mahadith Odalitsika ndi zolemba zina za Chisilamu, ndipo manyuzipepala amenewa amagulitsidwa kwa anthu amene amatola mapepala osafunikira otha ntchito, ndi cholinga chopezako ndalama. Izi ndi zinthu zodandaulitsa kwambiri! Nyuzipepala za mtundu umenewu zimapezekanso mu njira zoyendamo zonyasa monga ngalande zoyendamo zoipa za m'zimbudzi. Tidayenera kulemekeza zolembedwa zonse zopatulika.

O!! Abale anga olimba mtima. Asilamu! M'malo mogulitsa manyuzipepala ndi cholinga chopeza ndalama zochepa, Chonde kaponyeni manyuzipepalawo mu nyanja mwakuya, mwa chifuniro cha Allah, mudzapeza madalitso a zimenezi mdzikolino lapansi komanso m'moyo umene ukubwerawo pambuyo pa moyo uno. O!! abale anga Achisilamu a malonda! Mupewe kupanga matumba oyikamo zinthu pogwiritsa ntchito ma pepala polemekeza komanso kudzipereka kwanu kwa Allah komanso kwa Mtumiki wake okondedwa (Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم)

Pali anthu ena amene amalekanitsa zolembedwa za chipembedzo zomwe zikapezeka mbali ina ya nyuzipepala ndi kugwiritsa mbali ina yomwe palibe zolemba za

chipembedzo pomanga ma phukusi ndi njira zina, amachita izi poganiza kuti kuteroko sakunyoza malembo. Anthuwa akupephedwa kuti akaponye nyuzipepala yonse mu nyanja popeza kumva ndi nkhani yolembedwa mnyuzipepala kaya ndi zotsatsa (Zolengezetsa) za ma filimu (Kanema), mmenemo mukupezeka maina ambiri a Chisilamu kuonjezerapo mawu oti Allah ndi Muhammad, monga Abdullah, Abdur Rahman, Ghalam Muhammad ndi maina ena.

Kaya ndi Urdu kapena Sindhi, Chingerezi kapena Hindi, pali kuthekera kopezeka maina opatulika mu nyuzipepala iliyonse yopezeka pa dziko la pansi mu chiyankhulo chilichonsecho. Zenizeni ndizakuti, zilembo za chiyankhulo chilichonse m'dziko lapansi, ziyenera kuremekezedwa mogwirizana ndi zimene adanena olemba Tafsir Sawi kuti ziyankhulo zonse zoyankhulidwa mdziko lapansi ndi zochokera ku Iiham. *(Tafsir Sawi, vol. 1, p. 30)* Choncho zili zabwino komanso zotetezeka kukaziponya pa dziwe la Nyanja, Mosakaika, Allah adzikulipilirani inu chifukwa cha ntchito yanu yolemekeza zolembedwa zopatulika.

## Misala Ya Abambo

Mnyamata nthawi ina yake adabwera kwa Sag–e–madina ndikunena kuti, "Chonde ndipangireni Dua ya abambo anga amene ali amisala. Ali ndi chizolowezi.

Olemba bukuli, Amir–e–Sunnat, akudzinena yekha kuti "Sag – e – madinah" pofuna kudzichepetsa yekha. Chopenga chomatenga ma nyuzipepala ndi zidutswa za mapepala olembedwa kuchoka m'misewu, kenako ndikukaziponya zimenezi mnyanja. Samavomera kulandira ndalama zomwe ndimawapatsa. Pozindikira zimene ndinamufusa bambo wachichepereyo "Kodi ndiwe olembedwa ntchito m'boma? "Iye adavomera, Kenako ndidati kwa mnyamatayo, "Mukandipelekere salaam kwa bambo anu olemekezeka komanso ndipemphe kuti akandipangire Dua ya chikhululuko; mukagwire ntchito yothandiza bambo anu komanso mukawasamalire. Chifukwa chomwe amatolera ma nyuzipepala ndi zinthu zina ndi chakuti nyuzipepala zimakhala ndi zolemba zopatulika, komanso chifukwa chomwe savomelera kulandira ndalama zako ndichakuti ndiwe olembedwa ntchito m'boma, ndipo ambiri ogwira ntchito yaboma amalandira malipiro osavomerezeka chifukwa cholephera kukwaniritsa ntchito zawo moyenera. "Atamva izi iye (bambo wachichepere) adavomereza kuti samakwaniritsadi kagwiridwe ka ntchito yake.

Okondedwa Abale Achisilamu! Ngati bambo ake amnyamatayu, كَثَّرَ اللّٰهُ تَعَالٰى اَمْثَالَهُمْ (Allah awonjezere chiwerengero cha anthu otere) Zikanakhala kuti msilamu aliyense atatenga misala ya madani, ndithu ndithu kuwala kwa kupembedza momuopa Allah ndi madalitso ake, adzapambana paliponse, kupanga dera (gulu) lathu kukhala "Gulu la Madani."

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب　　　صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Okondedwa Abale Achisilamu! "Pofuna kukhazikitsa kaganizidwe ka Madani" mudzipange kukhala chizolowezi chanu chomayenda ndi ma Qafilah a Madani ndi akakonda odzipereka a Mtumiki (Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم) Tamvetserani nkhani yochitika yomwe ili yotsitsimutsa chikhulupiliro yokhudza zabwino za mtumiki olemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kwa amene amakhala nawo mma Qafilah a Madani a Dawat –e–Islami.

## Zabwino Za Mtumiki ﷺ Kwa A Paulendo A Madani Qafilah

Ichi ndi chidule cha nkhani yoperekedwa ndi kakonda odzipereka wa Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Iye amafotokoza kuti, "Qafilah wathu wa Madani odzadzidwa ndi sunnah adayenda ulendo ochoka ku Hyderabad (Bad–ul–Islami, Sindh) kupita ku kyber pakhtunkhwa. Titakhala mu mzikiti masiku atatu, tinanyamuka ulendo olowera ku dera lina koma kumeneko tili mu njira, tinasokera ndipo tinazindikira tili ku nkhalango. Kudalibe chizindikiro chilichonse cha kupezeka kwa anthu m'madera apatali ngakhale pafupi. Tidali okhudzika ndi kudandaula nyengo pamene idali kupita, kenako chiyembekezo chokometsera chidatifika pomwe chapatali tidaona mwachidule chinthu chomwe chidaoneka ngati kusuntha kwa nyale. Tidathamangira kumeneko ndi chisangalaro, koma mosayembekezera kuwala kuja kudasowa mwa kanthawi kochepa, nkutisiya ife tili odabwitsidwa ndi nkhawa. Tidalephera kupanga chiganizo kuti titani kapena tilowera kuti?

Tidakhala ndi mantha kwa nthawi. Mwadzidzi, kuwala kuja kudaonekeranso kuchokera mbali yomwe ija tidawona nyale poyamba. Tikutchula dzina la Allah, ndi kulimba mtima, tidayenda mofulumira kulowera komwe timawona kuwala, tili ndi chiyembekezo kuti tikapezako chithandizo kuchokera kwa munthu wina wake. Titayandikira tidawona munthu atayima, ali ndi nyale mmanja mwake, Adakumana

nafe mwachikondi ndi kutitengera kunyumba kwake kumene tidakapeza makapu khumi ndi awiri (12) atakonzedwa kale kukhala makapu a anthu khumi ndi awiri (12) a Madani Qafilah. Mtenthandevu (tiyi) naye adali atakonzedwa kale! Adatipatsa mtenthandevu otentha. Ife tidadabwitsidwa ndi chithandizo cha changu chimenechi chochokera Mseri (Ghayb) komanso dongosolo lopangiratu la makapu khumi ndi awiri a mtenthandevu.

Atafunsidwa mwini khomo amene adali wachilendo kwa ife, Iye adaulula kuti "Ndidali mtulo pomwe Mayi anga omwe adalikugona, adadzuka, Kundidalitsa ndi masomphenya a mtumiki olemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم m'maloto, Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adati, Apaulendo a Madani Qafilah ku Dawat–e–Islami asochera njira. Ima panja ndi nyale kuti uwathandize iwo. Ndidadzuka ndi kuima panja ndi nyale. Ndidakhala chiimilire choncho ndikudikirabe kwa nthawi. Koma sindidawone munthu wina aliyense. Ndidaganiza kuti mwina sindidamvetse malotowo. Ndidayamba kumva tulo kotero ndidabwelera kunyumba ndi kukagonanso.

Maso anga adatsekedwa koma khomo la mtima wanga lidatsekulidwa ndipo ndidachita mwayi kuwona nkhope ya mtumiki wa chisomo, Mkhala pakati wa Ummah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kachiwiri. Milomo yake ya madalitso idagwedezeka ndipo mawu awa adayankhulidwa: O apaulendo a Madani Qafilah okwana khumi ndi awiri (12); Uwakonzekere tiyi ndipo nthawi yomwe ino uyime kunja ndi nyale. Nthawi yomweyo ndinakonza tiyi ndi kuima kunja kwa nyumba ndi nyale, Mosachedwa ma Qafilah a Madani mwa Akakonda odzipereka a mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nawonso adafika.

## CHAKUDYA CHOCHOKERA KWA MTUMIKI ﷺ

Okondedwa abale Achisilamu! Chochitika ichi chikuwonetsa poyera kuti Mtumiki opatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ali ndi kuzindikira kwa mseri (Ghayb) ndipo amakonda Dawat–e–Isilami, bungwe la Asilamu amene ali pachiwongoko. اَلْحَمْدُ لِلّٰه, Mtumiki wathu opatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse amawasunga akakonda ake. Odzipereka powayang'anira muchisoni chake, amawathandiza akakhala m'mavuto ndi kuwadyetsa okhala ndi njara.

Imam Yusuf Bin Ismail Nabhani رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza kuti Shaykh Abul Abbas Ahmad Bin Nafis Tunisi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza motere" Munyengo ya kukhala kwanga mu Madina–tul–munawwarah, nthawi ina ndidamva njala kwambiri. Nditafika pa

mtumbira (Manda) a Mtumiki opatulika, صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndidapempha, ya Rasulallah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ine ndili ndi njala. Mwadzidzidzi, ndinagona. Pa nthawi yomweyo, munthu wina wake adandidutsa nkundiwuza kuti ndipite naye, ndinavomera ndipo ananditengera kunyumba kwake, Adandipatsa tende, Chiponde ndi buledi opangidwa ndi ufa wa Tirigu, ndipo iye adati Idya kufikira utakhuta chifukwa kholo langa Sayyiduna Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, wandilamura ine kuti ndikusamalire iwe. Uzibwera kwa ine nthawi zonse ukamva njala nthawi za mtsogolo” *(Hijjatullahi – alal – vol. 2, p. 573)*

*Zomwe timamwa ndi zochokera m’bwalo mwanu. Zimene timadya ndi zochokera m’bwalo mwanu (Saman – e – Bakhshish)*

## Lemekezani Zilembo Za Chiyankhulo Chilichonse.

Okondedwa Abale Achisilamu! Musamalembe بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم kapena dzina lililonnse lopatulika pa zinthu zomwe pali kuthekera kwa mawuwa ndi mainawo kunyozedwa posalembedwa chilichonse pansi mu chiyankhulo china chilichonse, ndipo lemekezani Zilembo Za Chiyankhulo Chilichonse

Okondedwa Abale Achisilamu! Musamalembe بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم kapena dzina lirilonse lopatulika pamalo ena aliwonse pomwe pali kuthekera konyozetsa (kosalemekeza) mainawo. Pansi (padothi) pasalembedwe china chilichonse mu chiyankhulo china chilichonse ndipo zilembo za chiyankhulo chilichonse zilemekezedwe. Musaponde pa chinthu kapena malo aliwonse pamene palembedwa zinthu mu chiyankhulo china chilichonse. Zopondera zapakhomo zomwe palembedwa mawu akuti MWALANDIRIDWA zochita kusindikizidwa kapena kusokedwa, zisayikidwe kunja kwa chitseko. Ngati dzina la kampani lasindikizidwa pa chovala kuphazi, ngakhale chitakhala chiyankhulo cha chingerezi, ovalayo ayenera kuchotsa kaye dzina la kampanilo asadavale chovalacho.

Nyengo zambiri, zizindikiro zolembedwa zomwe pamakhala dzina la kampane zolembedwa mchingerezi, ChiArabu kapena ChiUrdu zimaikidwa ku mikeka yopempherera. Zomvetsa chisoni zizindikiro zolembedwa zimenezi zimasokedwa moyandikitsa ndi malo oponda mapazi pa mkekapo. Kuwonjezera apo, zizindikiro zolembedwa zimenezi zimawonekanso mmikeka ya pulasitiki, mmagombeza,

mmathawulo ndi zina. Zizindikiro zolembedwa zimenezi zizichotsedwa ndikutaidwa mosamala kapena kuponyedwa mu nyanja.

Zizindikiro zokhala ndi dzina la opanga katundu zimapezeka kawirikawiri pa matiresi. Zikadakhala bwino kuti makampane amenewa asamatiyese ife motere! Mosamala, talingalirani mawu ammalamulo onenedwa pa patsamba 237 mgawo la 16 la Bahar-e-Shariat moikira umboni ndi Rad-dul-Muhtar, "Ngati chinachake chalembedwa pa chogonera kapena pa mkeka opempherera, choterocho sichili chovomerezeka kuchugwiritsa ntchito posatengera kuti mawu asindikizidwa kapena kusokedwa kapena alembedwa ndi inki. Chigamulo chomwecho chidzagwiritsidwa ntchito ngakhale kuti zilembo zitalembedwa molekanitsa pazokhapazokha popeza malembo olekanitsidwa nawo ayenera kulemekezedwa.

Mlembi wa buku la Bahar-e-Shari'at رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anapitiriza kufotokoza ponena kuti,"Zolembedwa zimawoneka pa mikeka yokhalira nthawi yakudya. Mtundu uwu wa mikeka (yokhala ndi dzina la kampane kapena malembo osindikizidwa ndi kulembedwa) isagwiritsidwe ntchito kapena chakudya chisaikidwe pa mikeka imeneyi. (Mmadera ena a Subcontinent) zolemba zimakhala pa mitsamiro (pilo) ya anthu ena; mitsamiro imeneyi isamagwiritsidwe ntchito."

Mwanjira ina iliyonse, kaya ndi mkeka opempherera, kapena zopondapo, zoyala pansi zobwerekedwa kapena zogulidwa zapanyumba, mtsamiro kapena matiresi chilichonse chomwe munthu amakhalapo kapena chomwe amapondapo, chikhale chopanda malembo achiyankhulo china chilichonse, kapenanso chisayikidwe chizindikiro cha kusindikizidwa kulikonse kwa malembo. Dzina ndi keyala ya kampani yopanga katundu nthawi zambiri zimalembedwa pansi pa choyala ndi zopondapo mnyumba; zizindikiro zolembedwa zomatidwa pa katundu ameneyi, muzizinyowetsa ndi madzi kenako nkuzimatula pakapita mphindi zochepa.

Zolembedwa mu chiArabu zizilemekezedwa mwapaderadera chifukwa chiArabu ndichiyankhulo chopatulika cha Mtumiki wathu opatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم komanso ndi chiyankhulo cha Quran Yoyera ndi anthu okhala ku Paradiso. Allah akuletsa, ndipo izi ndizinthu zochotsa ulemu komanso zochotsa mwayi kungotaya zolembedwa za chiArabu kapenanso kuponya zolembazi mmalo otaira nyansi za zinyalala ngakhale

zolembazo zitakhala zili zosindikizidwa pa mapaketi oyikamo zakudya kapena zakumwa.

## Kulumikizana Kopatulika Kokhudza Manambala

Nthawi zina mopanda mawu, nambala nthawi zambiri imalembedwa pa chovala kuphazi. Kakonda odzipereka samakonda kuika phazi lake pa nambala iliyonse chifukwa nambala iliyonse ili ndi kulumikiza kopatulika.

Mwachitsanzo, zanenedwa pa tsamba 22 la Ahsan-ul-Wi'a zokhudza kubwereza Du'a mu manambala osagawika," Allah عَزَّوَجَلَّ ndi 'Witr'(aliyekha) ndipo amakonda Witr (kutanthauza kuti nambala zosagawika ndi 2 monga 1,3,5,7 ndi nambala zina). 5 alibwino ndipo Allah amakonda nambala ya 7 ndipo yomaliza ndi 3. (Mu kanenedwe kena zikutanthauza kuti pamene munthu akupanga Du'a, ayenera kubwereza kokwana kasanu ndi kawiri kapena kasanu kapenanso katatu)

Nambala nazo zili ndi kulumikiza kopatulika kwakukulu. Mwachitsanzo kulumikiza kopatulika kwa nambala 2 ikukhudza 'Urs ya Sayyiduna Ma'ruf Karkhi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ndi Urs ya Sadr-ush-Shari'ah رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, mlembi wa Bahar-e-Shari'at imakhala pa 2 Muharram-ul-Haram ndi 2 Zul-Qa'da-til-Haram mu ndondomeko ya maina ndi miyezi yatchulidwa.

Nambala 4, ikulumikizidwa ndi otsatira okondedwa ndi oyandikira kwambiri a Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Aliyense amene ali kakonda wa omutsatira okondedwa anayi a Mtumikiwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adzakhala opambana mmoyo wadziko lapansi komanso moyo pambuyo pa moyo uno in shaa Allah. Nambala 6 ikulumikizidwa ndi 6 Rajab-ul-Murajjab, tsiku la Urs ya Gharib Nawaz رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه pamene nambala 8 ikulumikizana kuti pali ma Paradiso asanu ndi atatu (8) komanso Urs ya Maulana Hashmat Ali Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه limalemekezedwa pa 8 Muharram-ul-Haram. Kulumikizidwa kwa nambala 10 ndi tsiku la 'Ashura', tsiku lomwe Sayyiduna Imam Husayn رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anakhala shaheed ndiponso ikulumikizidwa ndi Eid-ul-Adha. Kutchuka kwa kulumikiza kopatulika kwa nambala 11 ndi 12 ndikodziwika bwino ndipo masikuwa amakhala achisangalalo kwa akakonda onse.

*Nditalingalira za nambala 11 ndi 12*
*Ndinazindikira za zinthu zenizeni, O Ghaus-e-A'zam* رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه

*Muli ndi mzere wa ubale osaphwanyika ndi Mtumiki* صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم
*Uwu ndi udindo wanu wa ukulu, O Ghaus-e-A'zam* رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه

## NJIRA YOIKIRA MAPEPALA OPATULIKA M'NYANJA

Ali osilirika ndi amwayi Asilamu amene amatola kuchokera padothi manyuzipepala, mapepala opatulika ndi zidutswa za makatoni komanso zinthu zina akaziona zinthu zimenezi nakaziika pa dziwe la nyanja kapena mtsinje ndicholinga cholemekeza. Mapepala opatulika asaikidwe pamalo osaya panyanja popeza zikhoza kupangitsa mapepalawa kuyandama kukafikira pa gombe la nyanja.

Njira ya kaikidwe ka mapepalawa m'nyanja ili motere: Ikani mapepalawa mu thumba kapena m'saka lopanda kanthu ndikuikamo mwala olemera mthumbamo; kenako boolani timabowo pa thumbalo kuti madzi alowe mu thumbalo mwachangu kuti likafike pansi pa nyanja.

Ngati thumba liponyedwa mu nyanja osaboola, madzi am'nyanja sangalowe mwachangu mthumbamo zomwe zingachititse nthawi zina thumbalo kuyandama pa mtunda wautali ndikukafika pa gombe. Nthawi zina anthu a umbuli kapena osakhulupirira amatha kutsekula thumbalo pa gombe ndi mtima ofuna kutenga zomwe zili mmenemo, izi zingapangitse kunyozeka kwakukulu kwa mapepalawa komwe kungapangitse mtima wa kakonda kukhala otunthumira. Pofuna kutsimilizira kuti thumba lokhala ndi mapepala opatulika lafika padziwe la nyanja, ndipofunika kupeza thandizo la Msilamu okhala ndi bwato. Mwanjira iliyonse, mabowo apangidwe pa thumbalo.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Njira Zokwilira Mapepala Opatulika

Ndizovomerezeka kukwilira mapepala opatulika. Pakulongosola njira zoyenera kutsata pokwilira mapepala opatulika, Sadr-ush-Shari'ah afotokoza pa tsamba 121 m'gawo la 16 la Bahar-e-Shari'at ndi kutchulidwa kwa Alamgiri: "Ngati Quran Yopatulika yafika pakutha kufikira kuti siingagwiritsidwenso ntchito kuwerenga, ndipo pali kuthekera kuti masamba ake akhoza kuthothoka ndi kutaika, ndiye kuti Quran yo ikulungidwe mu nsalu yoyera ndi kukakwiliridwa pamalo osamalika (otetezeka). Pofuna kukwilira, kumbani Lahad (dzenje laling'ono mkati mwa dzenje lalikulu mbali ya chipupa choyang'ana ku Qiblah, dzenje lalikulu lokwanira mapepala onse ofunika kukwirira) ndicholinga chakuti dothi pokwirira lisakhudze mapepala opatulika a Quran. Njira ina,

muyike mapepala mu dzenje lokumbidwa) mutseke pamwamba pake ndi thabwa ndi kuthira dothi pamwamba pa thabwalo ndicholinga chakuti dothi lothiridwalo lisagwere pa mapepala opatulika. Ngati Quran yatha kwambiri, isawotchedwe ndi moto."

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Ngale 29 Za Madani Za بِسْمِ اللّٰه

(Ngale khumi zoyambirira za Madani zatengedwa kuchokera mu Tafsir-e-Na'imi, tsamba 44 gawo loyamba)

1. بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndi vesi yachikwanekwane ya Quran osati mbali imodzi ya Surah. بِسْمِ اللّٰه adavumbulutsidwa pofuna kusiyanitsa pakati pa Surah ndi Surah inzake. Ndichifukwa chake amawerengedwa mositsa mawu nthawi ya mapemphero. Komabe amene adaloweza pamtima Quran akamawelenga Quran yonse pa pemphero la Taraweeh, ayenera kuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم mokweza mawu akamawerenga Surah ina iliyonse.

2. Owerenga Quran ayenera kuyamba kuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم kupatula akamawerenga Surah At-Taubah. Komatu ngati ofuna Kuwerenga Quran akuyamba ndi Surah At-Taubah, ndiye kuti ayenera kuyamba ndi بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم pamene akuyamba kumene kuwerenga Quran.

3. Zanenedwa m'buku la Shami kuti ndibwino kusawerenga بِسْمِ اللّٰه munthu asadasute Huqqah, (madzi amupaipi) kapenanso asadadye zakudya za fungo (monga anyezi osaphika, adyo ndi zakudya zina).

4. Ndizoletsedwa kuwerenga بِسْمِ اللّٰه munthu ali pa malo odzithandizira (chimbudzi)

5. Pamene munthu akuswali, (kupemphera), ndizofunika kwambiri kwa iye kuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndi mawu ositsa asadayambe kuwerenga Surah.

6. Ntchito iliyonse yolemekezeka yomwe munthu angapange popanda kuwerenga بِسْمِ اللّٰه, ntchitoyo idzakhala yopanda madalitso.

7. Pa nthawi yoika mtembo mmanda, amene akugwira ntchitoyi ayenera kuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ وَعَلٰى مِلَّةِ رَسُوْلِ اللّٰهِ

8. Khutbah ya Ijuma, Chikwati, ndi ma Eid onse awiri, ziyambidwe ndi mawu akuti اَلْحَمْدُ لِلّٰه mokweza koma بِسْمِ اللّٰه awerengedwe poyambirira motsitsa mawu. Pamene opereka Khutbah (Khatib) akufuna kuwerenga ndime ya Quran pa nthawi yopanga Khutbah, ayambe ndi kuwerenga بِسْمِ اللّٰه mokweza (asadawerenge ndime (vesi) ya Quran).

9. Ndichikakamizo kuwerenga بِسْمِ اللّٰه (kutchula dzina la Allah, عَزَّوَجَلَّ pa nthawi yozinga nyama. Ngati kuwerenga بِسْمِ اللّٰه kwasiidwa mwadala, (dzina la Allah osatchulidwa) chozingidwacho chidzakhala chibudu ndipo nyamayo idzakhala yoletsedwa kudya. Komabe nyamayo idzavomerezedwa kudya ngati munthu wozingayo adachita kuyiwala kuwerenga بِسْمِ اللّٰه.

10. Ngati kumbali ya Zabh-e-Idtirari, (kuzinga kwa chikakamizo), mwachitsanzo ngati munthu akusaka nyama kapena mbalame ndi muvi kapena mkondo, kapena chida chomwe chili chakuthwa ndipo munthuyo nkuwerenga بِسْمِ اللّٰه pamene akuponya muvi, mkondo kapena chida (mwa zida kosaka) nyama yophedwayo idzavomerezeka kudya ngakhale mlenje ataipeza nyamayo itafa kale.

11. Ngati nyama yapakhomo itathawa kuchoka kwa mwini wake nyamayo, mwachitsanzo ng'ombe yasowa ndikugwera mu chitsime, kapena ngamila itathawa ndiye munthu wina nkuipha ndi muvi kapena nkondo kapena ndi lupanga, pambuyo pa kuwerenga بِسْمِ اللّٰه, nyamayo idzakhala yovomerezeka kudya. (Komabe, pambuyo powerenga بِسْمِ اللّٰه, ngati munthu atapha nyama yakuthengo kapena mbalame ndi mtengo kapena mwala kapena ndi chipolopolo cha mfuti, nyama kapena mbalameyo idzakhala yoletsedwa (Haram) kudya chifukwa nyamayo yafa yovulala osati chifukwa chotaya kapena kutuluka magazi zimene zili zololedwa pa kuzinga. Ngati nyamayo inagwidwa yamoyo ili yovulala, idzakhala yovomerezeka kudya potengera Zabh-e-Shari' (Kazingidwe ka Shariah). Zabh-e-Ikhtiyari ili yofunika kuti nyama ya mtchire kapena mbalame yomwe yagwidwa ikhale Halaal, nyamayo kapena mbalame iyenera

kuzingidwa mogwirizana ndi njira zozingira pa Shariah potchula dzina la Allah (عَزَّوَجَلَّ).

12. Sayyiduna Shaykh Abul Abbas Ahmad Bin Ali Buni رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza kuti, " Ngati wina aliyense atawerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم kokwana 786 tsiku lirilonse (ndikuwonjezera Salat Alan-Nabi صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kamodzi koyamba asadawerenge بِسْمِ اللّٰه ndi kumapeto kwa بِسْمِ اللّٰه) kwa masiku okwana asanu ndi awiri (7) motsatizana, in shaa Allah, zofuna zake zonse zidzakwaniritsidwa, kaya ndizolinga zofuna kuthetsa zokhoma kapena kufuna kupeza zabwino kapena kufuna chipambano mu zamalonda zake." *(Shams-ul-Ma'arif, p. 73)*

13. Munthu amene angawerenge بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم asanagone kukwanira 21 (ndikuwonjezera Salat Alan-Nabi صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kamodzi koyamba asadawerenge بِسْمِ اللّٰه ndi kumapeto kwa بِسْمِ اللّٰه), adzatetezedwa usikuwo kuchokera kwa Satana, umbanda, imfa ya dzidzidzi ndi mtundu uliwonse wa tsoka ndi mavuto اِنْ شَآءَ اللّٰه. *(Shams-ul-Ma'arif, p. 73)*

14. Amene angawerenge بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم kokwana ka 50 (ndikuwonjezera Salat Alan-Nabi صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kamodzi koyamba asadawerenge بِسْمِ اللّٰه ndi kumapeto kwa بِسْمِ اللّٰه) pamaso pa munthu opondereza, oponderezayo adzakhala ndi mantha mumtima mwake kwa munthu owerengayo, ndipo owerengayo adzakhala otetezedwa ku zoipa za opondereza. *(Shams-ul-Ma'arif, p. 73)*

15. Kwa munthu amene kuloweza zinthu (kusunga zinthu mmutu) kapena kukumbukira zinthu kumakhala kofooka, munthuyo akawerenga بِسْمِ اللّٰه Rahmanir Rahim kokwana 786 (kuwonjezerapo Salat Alan-Nabi – Kamaodzi poyamba ndi pomaliza pa بِسْمِ اللّٰه) ndikupanga Dam (kuuzira) mmadzi ndi kumwa madziwo, chikumbumtima chake chidzasintha mwa ubwino ndipo adzakhala akukumbukira zonse zomwe akumva اِنْ شَآءَ اللّٰه. *(Shams-ul-Ma'arif, p.73)*

16. Ngati kungachitike chilala, werengani بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم kokwana 61 (Kuwonjezerapo Salat Alan Nabi صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kamodzi poyamba ndi pamapeto pa بِسْمِ اللّٰه kamodzi, kenako pangani Dua). Mvula idzagwa m'dera lomwe kuli chilala, اِنْ شَآءَ اللّٰه. *(Shams-ul-Ma'arif, Pp 73)*

17. Lembani بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم, kokwana 35 pa pepala (limodzi ndi Swalat Alan Nadi صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kamodzi poyamba ndi pomaliza kuwerenga بِسْمِ اللّٰه) ndi kukoloweka mnyumba, In-Shaa Allah, Satana sadzadutsa mnyumbayi, ndipo padzakhala madalitso. Ngati wina atapachika zolembedwazi mu shop, malonda ake adzachita bwino kwambiri. اِنْ شَآءَاللّٰه. *(Shams-ul-Maarif, p. 73)*

18. Lembani بِسْمِ اللّٰه kokwana 130 (kapena mulembe zimenezi pa pepala) patsiku loyamba la mwezi wa Muharram ndi kusunga pepalalo (kapena asunge ngati Ta'wiz poyika mu pulasitiki ndi kusokera nsalu kapena m'chikopa), اِنْ شَآءَاللّٰه, opanga zimenezi ndi banja lake adzakhala otetezedwa kuchokera ku zoopsa nthawi yonse m'moyo mwawo. *(Shams-ul-Ma'arif, p. 74)*

19. Ngati ana amene akumwalira ali akhanda (Sakutha kupulumuka), mayi alembe بِسْمِ اللّٰه kokwana 61 (kapena alembe ndi kudzisunga yekha, In-Shaa Allah, ana ake adzakhala amoyo (akhoza kuikanso mupulasitiki kapena kumata m'pepala lomwe simungalowe madzi kenako nkusokera msalu kapena muchikopa, akhozanso kuvala mkhosi mwake kapena kumanga padzanja. *(Shams-ul-Ma'arif, p. 74)*

20. Lembani بِسْمِ اللّٰه kokwana 70 pa pepala ndi kuika pepalalo mkati mwa sanda ya munthu amene wamwalira, zochitika pakati pa munthu wakufa ndi angelo Munkar ndi Nakir zidzakhala zofewa, اِنْ شَآءَاللّٰه. (Ndibwino kupanga pilala mkhoma (mchipupa) mbali ya Qiblah kutsogolo kwa nkhope ya munthu wakufa ndi kuika zolembedwazi mpilalamo pamodzi ndi Ahd Namah ndi Shajarah ya Pir sahib wa munthu omwalirayo. *(Shams-ul-Ma'arif, p. 84)*

21. Nthawi zonse mudziwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم pomatchula mawu ake molondola komanso mokometsa. Werengani بِسْمِ اللّٰه kwa amene ali akatswiri powerenga Quran kapena kwa ophunzira wa Chisilamu. Ngati zilembo sizikutchulidwa bwino komanso molondola, mwayenera kuphunzira katchulidwe kolondola. Mwinamwake zimaoperedwa kuti munthu akhoza kuluza (kutaya) mmalo mopindula.

22. Sizili zofunika kuika zilembo za m'mwamba kapena mmunsi (mmalembedwe achi Arabu) pamene mukulemba بِسْمِ اللّٰه. Nthawi zonse mukamalemba vesi

kapena mawu omwe mukufuna kugwiritsa ntchito ngati Ta'wiz yofuna kuvala, kumwa kapena kupachika kukoloweka, onesetsani kuti zunguliza za zozunguliza zokhala ndi zilembo zili zotsekulidwa (Osatseka). Mwatchitsanzo, zunguliza wa Ha (ه) m'mawu akuti Allah komanso Min (م) m'mawu akuti رَحمٰن ndi رَحِيم, zikhale zotsekulidwa.

23. Ngati munthu awerenga بِسْمِ اللّٰه asadavule zovala, majini sangawone zobisika zake (Satr). (Aml-ul-yaum wal-Laylah li – Ibn Sunni, p. 8) Paliponse mukamatsekula kapena kutseka chitseko, zenera, kabati kapena mukamatenga kapena kusiya pansi zovala, ziwiya kapena china chilichonse, zikhale chizolowezi chanu kuwerenga بِسْمِ اللّٰه, majini owopsa sadzakwanitsa kulowa mnyumba mwanu, kuba kapena kugwiritsa ntchito katundu wanu, اِنْ شَآءَاللّٰه.

24. Ngati galimoto yanu itelera kapena kunjanja, werengani بِسْمِ اللّٰه.

25. Werengani بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم musadadzodze tsitsi lanu ndi mafuta, apo ayi, asatana 70 alowelera nawo zomwe mukupanga.

26. Werengani بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم mukamatseka chitseko cha nyumba yanu. (Ndi madalitso a بِسْمِ اللّٰه), Satana ndi majini oyipa sadzakwanitsa kulowa mnyumba mwanu, اِنْ شَآءَاللّٰه. *(Sahih Bukhari, vol. 6, p. 312)*

27. Usiku, vindikirani ziwiya zodyeramo ndi zomweramo ndi chinachake pambuyo powerenga بِسْمِ اللّٰه. Ngati palibe chovindikira, werengani بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndi kuika chidutswa kapena china chilichonse m'mbali mwa chiwiya. *(Sahil Bukhari, vol. 6, p. 312)*

28. Malingana ndi kufotokoza kwa Sahih Muslim, "Pa chaka pali usiku umodzi mmene mliri umatsika. Ngati mliri udutsa pa chiwiya chosavindikira kapena thumba la madzi limene pakamwa pake pali potsekula, mliri umalowa m'meneomo." *(Sahih Muslim, p. 1115, Hadith 2114)*

29. Musadagone, muyenera kuwerenga بِسْمِ اللّٰه ndi kupukuta zogonera kokwana katatu. Mukatere, mudzakhala otetedzeka kuchokera ku zinthu zopweteka (zoipa). اِنْ شَآءَاللّٰه.

30. Panthawi yopanga malonda ovomerezeka, pamene mwalandira chinthu kuchokera kwa wina wake, ndi kupereka chinthu kwa munthu wina, werengani بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم. Padzakhala madalitso aakulu kwambiri. اِنْ شَآءَاللّٰه.

Ya Allah! Tipatseni ife madalitso a بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndipo mutipange kukhala akutha kuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم nthawi zonse pomwe tikufuna kugwira ntchito yabwino komanso yovomerezeka.

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

# Mafanizo Asanu Ndi Awiri (7)

## (1) Wodula Nkhuni Asanduka Kukhala Wolemera

Padali bambo uyu amene ntchito yake idali yodula nkhuni, akadula amasonkhanitsa ndi kugulitsa kuthandizira banja lake. Chifukwa chakuti nkhalango idali mbali ina ya mtsinje, iye ankayenda mtunda wautali tsiku lililonse kukafika ku nkhalango kumeneko powoloka mlatho omwe udamangidwa pa mtsinje. Izi zimampangitsa kutenga nthawi yaitali ndipo zinali chipsinjo ku chuma chake.

Tsiku lina, adamva za ulemelero wa بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم pa nyengo ya ulaliki mu mzikiti, nachikhazikitsa m'maganizo kuti ngakhale vuto lalikulu likhonza kuthetsedwa ndi madalitso a بِسْمِ اللّٰه. Choncho, nthawi yopita ku nkhalango itafika, m'malo motenga njira yodutsira pamlatho, adayamba kudutsa pamadzi mu mtsinje akuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم, ndipo posachedwa, amakhala kuti wafika mbali ina ya mtsinje mosavuta. Atadula ndi kusonkhanitsa nkhuni, iye adabwelera kunyumba ngati mmene adabwelera. Chifukwa cha madalitso a بِسْمِ اللّٰه, adalemera mnthawi yochepa. *(Yatengedwa kuchokera ku Shams-ul-Waizin)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Okondedwa abale Achisilamu! Zonsezi ndi zodabwitsa za chikhulupiliro cholimba. Ngati chikhulupiliro ndichosalimba, zotsatira zopindula sizingakwaniritsidwe. Kunena zachikhulupiliro cholimba Hujjat-ul-Islam Sayyiduna Iman Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wafotokoza fanizo lopambana kwambiri pofotokozera Surah Yusuf.

Mu Baghdad, munthu wina adawapempha anthu ndalama (Dirham). Sayyiduna Ibn Sammak, رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه odziwika bwino pa mahadith, adamufunsa munthuyu “Ndi surah iti yomwe ukuidziwa bwino pa mtima?” Iye adayankha “Surah Al-Fatihah,” katswiri olemekezeka wamaphunziro adati “Werengani Surayo kamodzi ndipo undigulitse ine mphoto yake, ukatero ine ndidzakupatsa chuma changa chonse.”

Opemphayu adayankha, “Inu olemekezeka! Ndabwera kuno mokakamizika kuti ndidzapemphe dirham, osati kudzagulitsa Quran!” Pambuyo ponena mawu amenewa, wopemphayu adapita kumanda.

Nthawi yomweyo kudagwa mvula yambiri yosakanikirana ndi matalala. opemphayu adalumphira pansi pa denga kuti abisale kumvula ndipo ali pompo adakumana ndi oyenda pachokwera atavala zovala zobiriwira. Opemphayu adafunsa, “Kodi ndiwe munthu amene udakana kugulitsa mphoto ya surah-Al-fatihah?” opemphayo adayankha movomera. Kenako akumupatsa thumba la ndalama zokwana ma dirham 10,000, wa chokwerayu adati, “Kagwiritse ntchito ndalama izi ndipo ukazimaliza zonse, ndidzakupatsanso 10, 000-dirham zina, In-Shaa Allah. Opemphayu adafunsa, “Koma iwe ndiwe ndani?” Wachokwera adayankha, “Ndine Chikhulupiriro chako cholimba.” Wachokwerayu kenako adachoka. *(Zatengedwa kuchokera ku Tafsir Surah Yusuf, lil Ghazali, p. 17)*

Fanizo ili likupezekanso ndi phunziro kwa amene amapempha ndalama powerenga Quran yopatulika. Chimodzimodzinso amene amakhala nawo mmagulu owerenga Quran, kuyimba makaswida ngati ndikuchita Dhikr ndicholinga chokhala ndi dyera la ndalama ndi chakudya komanso kwa iwo owerenga Quran yopatulika nthawi ya pemphero la tarawih kuti apeze ndalama. Allah atidalitse ife ndi chuma chosawonongeka chodzipereka ndi chikhulupiriro cholimba.

اٰمِين بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

*Ntchito yanu iliyonse ikhale yofuna chisangalalo chanu O inu a Mphamvu.*

*Ndidalitseni ine ndi chuma chodzipereka ndi mtima wonse.*

Okondedwa Abale Achisilamu! Ndithudi kudzipeleka kuchoka pansi pa mtima ndi chuma chamtengo wapatali. Amene angachipedze amakhala opambana. Yendani ndi Madani Qafilah ozadzidwa ndi Sunnah pamodzi ndi Akakonda odzipeleka a mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, kaganizidwe ka madani kogwira ntchito modzipereka kuchoka pansi pa mtima kudzakhazikika. اِنْ شَآءَاللّٰه. Ngati ntchito zili zodzipereka mokhulupirika, اِنْ شَآءَاللّٰه, masomphenya opaturika adzabwera basi kwa amene akuwafunafuna ngati mmene zawonekera mu nkhani ikubwerayi.

## Masomphenya A Mtumiki ﷺ Nthawi Ya Ijtimaa Ya Kaseti

Pamapeto pa Ijtima ya maiko osiyanasiyana ya masiku atatu yodzadzidwa ndi Sunnah ku Dawat-e-Islami (Yomwe idachitikira ku Sahra-e-Madinah, Madina-tul-Auliya Multan) gulu lalikulu la Madani Qafilah la Akakonda odzipereka a mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amapita mmidzi yosiyanasiyana, matawuni ndi mmizinda ndicholinga chophunzira ndi kuphunzitsa Sunnah. Nayu tsatanetsatane wa nkhani yomwe idaperekedwa ndi Kakonda odzipereka kwa mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuchokera ku imodzi mwa Madani Qafilah.

Pambuyo pakutha Ijtimaa yodzadzidwa ndi Sunnah yamasiku atatu yokhudza mayiko osiyanasiyana *(Yomwe idachitika mchaka cha 1423AH)*. Madani Qafilah masiku khumi ndi awiri (12) yodzadzidwa ndi Sunnah ya Akakonda odzipereka a mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, idanyamuka kuchokera ku Sahra-e Madinah, Madin-tul-Auliya Multan ndi kukafika boma la Layyah (Punjab Pakistan)

Mogwirizana ndi dongosolo la Madani Qafilah, pamene Ijtima ya Kaseti inkachitika, Kakonda odzipereka wa mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adakhudzika kwambiri ndi ulaliki ozadzidwa ndi Sunnah kufikira kuti adayamba kulira kosaletseka ndipo mapeto ake adakomoka.

Atatsitsimuka adali okondwa. Iye adakuwa, اَلْحَمْدُ لِلّٰه! Ine ochimwa ndadalitsika ndi masomphenya a mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Tsiku lotsatira pomwe Ijtima ya kaseti idachitikanso, iye adawonanso za uzimu zomwe adawona tsiku lammbuyo ndipo adadalitsika ndi masomphenya a mtumiki okondedwa ndi wamadalitso صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

kachikenanso. Panthawi imeneyi adawona kuti anthu onse amene adali nawo pa Madani Qafilah, adali nawo limodzi ku bwalo la madalitso.

*Maso amakhala otseka koma mwayi umakhala chidzukire. O Hassan!*
*Kwa owafunafuna ndikomwe masomphenya opatulika amapita.*

*(Zauq-e-Na'at)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب　　صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Chinyengo Cha Satana

Anthu ena amafotokoza za maloto awo ndicholinga chofuna kuwasangalatsa ena, ndiye aliyense amene amanena zomuwona mtumiki okondedwa ndi odalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kapena kumuona munthu wina aliyense opatulika mmaloto ake. Asakhulupiliridwe mwachimbulimbuli, ayenera kuuzidwa kuti alumbire zoyankhula zoona.

## Machiritso A Chinyengo Cha Satana

Hadith yoyambilira mu Swahih Bukhari imanena kuti: اِنَّمَا الْاَعْمَالُ بِالنِّيَّاتِ "Ntchito zimadalira zolinga." Ngati munthu atchula za maloto ake kwa anthu ena ndi cholinga chofuna kudzionetsera kapena kutchuka, munthu osakaika akhala ochimwa koma ngati munthu atafotokoza za maloto ake ndi zolinga zabwino, palibe votuta zilizonse kutero. Mwachitsanzo, ngati munthu amene wachita mwayi kukhala ndi maloto abwino mu nyengo ya Madani Qafilah ya Dawat-e-Islami yozadzidwa ndi Sunnah, munthuyo akatchula maloto ake mchaka cha uchimo ndi cholinga chowalimbikitsa ndi kuwanyengelera anthu ena kuti anthu enawo ayende mu njira ya Allah ndi kupeza kukhutitsidwa kwa mtima pozindikira kuti Dawat-e-Islami ndi Bungwe lodzadzidwa ndi Sunnah la Asilamu amene ali pa chiongoko ndi Akakonda odzipereka a Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndikutinso anthu adzalimbikitsidwa kutsatira Dawat-e-Islami ndi kuteteza chikhulupiliro chawo, cholinga chimenechi ndichoyamikilika ndipo munthu amene akufotokoza za maloto ake ndi cholinga chimenechi adzalandira mphoto, اِنْ شَآءَاللّٰه.

Kuwonjezera apo, kufotokoza maloto ndi cholinga chofuna kuwonetsa kuyamika zabwino za Mulungu, izizi ndi zovomerezeka. Komabe, ngati pali mantha odziwonetsera, ndiye kuti munthuyo asatchule dzina popeza izi zidzakhala chitetezo

kwa iye ngati atatero. Mwanjira iliyonse, Allah amadziwa cholinga cha munthu mumtima mwake. Kukhala ndi chikaiko chopanda chifukwa kukhudza Msilamu, ndizinthu zoletsedwa (Haram), zolowetsa munthu ku moto. Mchitidwe wokhala ndi chikaiko, wadzudzulidwa ndi Quran yopatulika ndi Hadith choncho, vesi 12, Surah Al-Hujurat ndime 26, ikunena kuti:

يٰۤاَيُّهَا الَّذِيْنَ اٰمَنُوا اجْتَنِبُوْا كَثِيْرًا مِّنَ الظَّنِّ ۫ اِنَّ بَعْضَ الظَّنِّ اِثْمٌ

**"O inu amene mwakhulupilira! Pewani kukaikira, ndithudi kukaikira kwina ndi tchimo.!"**

*(Kanz-ul-Iman (Tanthauzo la Quran))*

Chimodzimodzi, zikunenedwa mu Hadith, "Pewani kukaikira koipa, popeza kukaikira koipa ndi bodza lalikulu.! *(Sahil Bukhari, vol. 6, p. 166), Hadith 5143)*. Ala Hadhrat Iman Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafotokoza mawu mu Fatawa-e-Razawiyyah, "Sayyiduna Isa عَلَيْهِ السَّلَام nthawi ina adawona wakuba akuba china chake ndiye iye (Isa – عَلَيْهِ السَّلَام) adati, "Kodi sunabe?" wakuba adayankha, "Ndikulumbira mwa Allah, ine sindinabe kalikonse." Atamva izi, Sayyiduna Isa عَلَيْهِ السَّلَام adati, "Zoonadi sudabe, maso anga andipusitsa ine."

Okondedwa abale Achisilamu! Fanizo limene lapitali likuwonetsa kufunika kolemekeza msilamu, popeleka phunziro lakuti munthu ayenera kubisa zolakwa za msilamu pomwe ali olemekeza malamulo a chisilamu (Shariah). Zisachitike kuti msilamu amutchule msilamu mnzake kukhala wabodza ndi oyankhula zofewa ndipo mopanda nzeru kutsekula makomo a chikaiko choipa ndi kuika pa chiopsezo moyo wake pambuyo pa moyo uno ndipo Allah ateteze, kudzipangira iye yekha kukhala okalowa ku moto.

تُوْبُوْا اِلَى الله      اَسْتَغْفِرُ الله

## Chilango Chofotokoza Maloto Odzipangira (Abodza)

Ngakhale munthu atafotokoza maloto abodza ndi odzipangira, munthu oteroyo zili zomukhalira yekha zopanga zakezo komanso ndi munthu ochimwa kwambiri, oyenera chilango chaku moto. Mtumiki olemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم akuchenjeza, "Munthu ofotokoza maloto abodza, adzapatsidwa chilango chomanga mfundo njere ziwiri za

balere patsiku la chiweruzo, ndipo iye sadzakwanitsa kumanga mfundoyo." *(Sahil Bukhari, vol. 8, p. 106, Hadith 7042)*

## Kulankhula Kopanda Kuyeza Mawu Oyankhulidwa

Zikunenedwa mu Hadith ina, "Munthu akamayankhula koma osasinkhasinkha za zimene akuyankhula (Zoyankhula zake kukhala za Haram monga kunama, miseche, kupezera anthu ena zifukwa mwinanso kufotokoza maloto odzipekera ndi zina za Haraam), pachifukwa ichi munthu amagwa m'dzenje lakuya la moto, kuya kwake kwakukulu koposa mtunda pakati pa kum'mawa ndi kumadzulo. *(Sahil Bukhari, vol. 7, p. 236, Hadith 6477)*. Kutengera Sharia, sichikakamizo kulumbilitsa munthuyo ali onama. Akhoza kulumbira zabodza, Allah atiteteze.

## Chinyengo Cha Satana

Mwa zonse, zili zoyenerera kubisa maloto kulekana ndi kuwafotokoza kwa anthu ena.

## Machiritso A Chinyengo Cha Satana

Opembedza moyera mtima olemekeza a Chisilamu adadziwa bwino kuposa ife zoyenera ndi zomwe zili zosayenera. Malamulo a chisilamu (Shariah), sadaletse kufotokoza maloto amene ali abwino, ndiye ife ndi ndani kuti titsekeredze zimenezi! Quran yopatulika, Mahadith ndi mabuku a opembedza oyera mtima ali ndi maloto ambiri. Sayyiduna Iman Abil Qasim Qushayri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه watchulapo maloto okwana makumi asanu ndi limodzi, mphambu zisanu ndi imodzi (66) okhudza opembedza a Chisilamu oyera mtima pa tsamba 368 mpaka 377 mu chaputala 'Ruyal Qawru! Zolembedwa m'buku lake 'Risalah Qushairiyah.'

Chimodzimodzi Hujjat-ul-Islam Sayyiduna Iman Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه nayenso adatchulapo maloto 49 patsamba 540 mpaka 543 mu chaputala 'Manamat-ul-Mashaikli' mu voliyumu (Buku) ya Chinayi ya buku lake 'Ihya-ul-Ulum.'

Kupitirira apo, maloto 14 a A'la Hadhrat Imam-e-Ahl-e-Sunnat, Mtsitsimutso wa Sunnah, ochotsa Bid'ah, Ophunzira wa Shariah, Allamah. Maulana Alhaj, Al-Qari, As-Shah Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, afotokozedwa mmawu ake patsamba 424

mpaka 432 a buku 'Hayat-e-A'la Hadhrat (Losindikizidwa ndi Maktaba Nabawiyyah, Ganj Bakhsh road, Lahore). Amodzi mwa maloto amenewa atchulidwa m'munsimu.

## Loto La A'la Hadrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه

Kufuna kutsimikizira za kuvomerezeka kugwirana mmanja ndi manja onse awiri, A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه analemba masamba 40 abuku lotchedwa (Masamba a Siliva mogwizana ndi kugwirirana chanza ndi zikhatho zonse ziwiri) pa tsamba lachitatu (3) la bukuli, A'la Hadrat watchulapo molongosola bwino za maloto ake omwe adawona Sayyiduna Imam Qadi Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه. Kupitirira, pofuna kupulumutsa Asilamu ku zinyengo za satana, ndikuwaunikira bwino Asilamu, A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wafotokoza ma umboni olimba m'bukumu pofuna kutsimikizira za kuvomerezeka kofotokoza maloto kwa anthu ena.

## Mtumiki ﷺ Atanthauzira Maloto

A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza m'buku lomwe latchulidwa kuti Mahadith odalirika adatsimikiza kuti mtumiki okondedwa ndi waodalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amagwirizanitsa kufunikira kwa maloto ndipo amalingalira za kufunika komvetsera, kufunsa komanso kufotokoza za maloto.

Patchulidwa Hadith yofotokozedwa ndi Samurah Bin Jundab رَضِىَ اللّٰهُ عَنْهُ, mu Sahih Bukharin ndi mabuku ena, "Pambuyo popemphera pemphero la Fajr, Mtumiki okondedwa ndi odalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amafunsa amene adali nawo pa pemphero kuti, "Alipo amene adali ndi maloto? Ndipo amafotokozeredwa, mtumiki opatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amatanthauzira malotowo. *(Sahih Bukhari, vol. 2, p. 127, Hadith 1386)*

A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anapitirizabe kunena kuti, "Abu Sa'id Khudri adafotokoza za Hadith yomwe idanenedwa m'buku la Ahmad, Bukharin di Tirmidh kunena kut Mtumiki opatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adati, "Pamene wina wa inu alota maloto amene ali osangalatsa, malotowo ali ochokera kwa Allah. Olota malotowo ayenera kumukwezeka Allah chifukwa cha maloto abwinowo ndipo awafotokoze malotowo kwa anthu ena." *(Musnad Imam Ahmad, vol.2, p. 502, Hadith 6223)*

## Nkhani za Chisangalalo Zidzapitirira

A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anapitiriza kufotokoza m'buku lomwe latchulidwa kuti mtumiki

opatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adanena kuti "Utumiki wamalizika. Tsopano sipadzakhalanso utumiki pambuyo pa ine koma mauthenga a chisangalalo. Kodi mauthenga a chisangalalo ndiwo ati? (Mauthenga a chisangalalo ndi maloto oyera amene munthu walota yekha kapena maloto amene anthu ena alota okhudza iyeyo (Munthuyo). *(Mu'jam Kabir, vol. 3, p. 179, Hadith 3051)*

## Mphoto Ya Kulota Maloto Abwino

A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adanenanso kuti, "Zatsimikizikanso ndi Sunnah ya otsatira Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuti ngati maloto ena aliwonse adali okomera (ogwirizana) ndi chigamulo chawo, amawakonda malotowo ndi kuwonjezera (kukulitsa) udindo wa munthu olota malotowo.

Zikunenedwa mu Sahihayn (Bukhari ndi Muslim) "Mu nyengo ya Hajj Tammattu' Sayyiduna Abu Jamrah Dabi رَضِیَ اللّٰهُ عَنْه adalota zomwe zidakomera chiphunzitso cha Sayyiduna Ibn Abbas رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُمَا (Zokhudzana ndi zigamulo zowongolera chipembedzo). (Pakumva maloto odalisika) Sayyiduna Ibn Abbas رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُمَا amakonza ndalama zapadera (Kumukonzera Sayyiduna Abu Jamrah Dabi kuchokera mchuma chake (Ibn Abbas). Loto la A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه

Potsimikizira kuloledwa kogwirana chanza ndi manja awiri, A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه walemba kabuku ka masamba 40 pamutu wakuti SWAFAIHU LLIJJAYN FIY KAUNI TASWAFUHI BIKAFFI-IL-YADAYNI (i.e Masamba asiliva okhudzana ndi kugwirana chanza ndi manja awiri). Patsamba la chitatu la kabukuka, A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه watchulapo matsatane tsatane za maloto ake momwe adawona Sayyiduna Imam Qadi Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه. Kuonjezera apo, pofuna kupulumutsa Asilamu ku chinyengo cha Satana ndi kuwaunikila, A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wanena maumboni enieni m'kabukuka otsimikizira kuloledwa kulongosora maloto kwa ena.

## MTUMIKI صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم MALOTO

A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wanena mu kabuku kameneka kuti ma Hadith enieni anatsimikizira kuti Mneneri okondedwa komanso odalitsika adaika kufunikira kwakukulu pamaloto ndipo amaona kuti ndi zofunika kwambiri kumvetsera, kufunsa, ndi kufotokoza maloto.

Zanenedwa ndi hadith yochokera kwa Samurah Bin Jundab رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ mu Sahih Bukhari ndi mabuku ena, "Akamaliza kuswali Salaat-ul-Fajr, Mtumiki okondedwa komanso odalitsika صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم amafunsa osonkhanawo kuti 'Kodi pali wina amene walota maloto usiku wathawu?' amene walota amawafotokoza malotowo ndipo mneneri oyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم amawamasulira." *(Sahih Bukhari, vol. 2, p. 127, Hadis 1386).*

A'la Hadrat رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ wanenanso kut, 'Abu Sa'id Khudri رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ wafotokoza za hadith yolembedwa mu Ahmad, Bukhari ndi Tirmizi kut Mtumiki oyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, "Aliyense mwa inu akalota maloto omwe ali okoma, amakhala achokela kwa Allah عَزَّوَجَلَّ. Alemekeze Allah عَزَّوَجَلَّ chifukwa cha izi ndi kuwafotokonza kwa anthu ena." *(Musnad Imam Ahmad, vol. 2, p. 502, Hadis 6223).*

## Nkhani Yabwino Idzapitilira

A'la Hadrat رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ wanenanso mu kabuku kameneka kuti mneneri oyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, "Uneneri watha. Tsopano sipadzakhala uneneri pambuyo panga, koma nkhani zabwino. Ndiziti? (Nkhani zabwino) ndi maloto oopa Mulungu amene munthu amalota yekha kapena amene (ena) amalota pa iye." *(Mu'jam Kabir, vol. 3, p. 179, Hadis 3051).*

## Mphoto yokhala ndi maloto abwino

A'la Hadrat رَحْمَۃُ اللّٰہِ عَلَیْہ adanenanso kuti "Zikutsimikiziridwanso ndi Sunnah ya maswahaaba رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُمْ kuti ngati maloto alionse angakomere chigamulo chawo, amasangalara nawo ndikukweza udindo wa munthu yemwe walotayo.

Zanenedwa mu Sahihayn, "Munthawi ya Hajj Tamattu' Sayyiduna Abu Jamrah Dab'I رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ adalota maloto omwe adakomera chiphunzitso cha sayyiduna Ibn Abbas رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُمَا (molingana ndi zigamulo zamalamulo). (Atamva loto lodalitsika lija) Sayyiduna Ibn Abbas adamsungila ndalama (Zochokera ku chuma chake) ndipo adayamba kukhala naye sayyiduna Abu Jamrah Dab'I pampando wake wachifumu kuyambira pamenepo." *(Sahih Bukhari, vol. 2, p. 186, Hadis 1567)*

Allah عَزَّوَجَلَّ awachitire chifundo ndi kutikhululukira popanda mlandu chifukwa cha iwo.

## Loto La Amayi Wa Imaam Bukhari عَلَیْہِ رَحْمَۃُ الْبَارِی

Abale okondedwa achisilamu, mwamvera nkhani ziwiri zopezeka mu Sahih Bukhari,

zofotokoza maloto kwa ena. Olemba Sahih Bukhari, Sayyiduna Shaykh Abu Abdullah Muhammad Bin Isma'il Bukhari رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adalemba ma Hadith odalitsika ndi chisamaliro chachikulu komanso modzipereka. Iwo رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati "اَلْحَمْدُ لِلّٰه, Ndasonkhanitsa ma Hadith pafupifupi 6000 mu Sahih Bukhari. Ndimapanga Ghusl, ndikupemphera Nafl swalaat ya ma Rak'at awiri ndisanalembe Hadith iliyonse."

Bambo ake olemekezeka رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adali munthu opemphera kwambiri ndipo mayi ake olemekezeka adalinso mzimayi olungama kwambiri komanso Mustajaba-tud-Dua (amene mapemphero ake amayankhidwa). Mu umwana wake, Sayyiduna Imaam Bukhari رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adasiya kuona. Chifukwa cha chisoni, amayi ake olemekezeka nthawi zambiri ankalira n'kupanga Du'a kuti mwana wawo ayambenso kuona.

Usiku wina atagona, nyenyezi ya chuma chawo idawala, ndikuwadalitsa m'maloto ndi masomphenya a Sayyiduna Ibrahim Khalilullah عَلَيْهِ السَّلَام adati, "Mwakhala mukupemphera kuti mwana wanu ayambenso kuona, Taonani, pemphero lanu layankhidwa, ndipo Allah عَزَّوَجَلَّ wabwezeletsa maso a mwana wanu." M'mawa adaona kuti Sayyiduna Imam Bukhari wayambanso kuona. *(Kuchokera mu Tafhim-ul-Bukhari, vol. 1, p. 4).*

Allah عَزَّوَجَلَّ awachitire chifundo ndi kutikhululukira popanda mlandu chifukwa cha iwo.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## (2) ZOCHITIKA ZOSANGALATSA ZA ANTHU AWIRI OMWE SIASILAMU

Mwamuna osakhala msilamu anali openga m'chikondi ndi mkazi yemwe sanali msilamu, ndipo anali atatsala pang'ono kusiya kudya ndi kumwa m'chikondi chake. Kenako adadza kudzadalitsidwa pabwalo la Sayyiduna 'Ata-ul-Akbar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ndipo anamuuza za momwe zinalili. Oyera wamkuluyu adalemba بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم papepala ndikumpatsa iye nati "mezani pepalali ndikuyembekezera kuti Allah akudalitseni ndi Chipiliro pankhaniyi kapena akupatsani mwayi oti mudzakwatirane naye."

Pamene munthu osakhala msilamu adameza pepalalo, (kusintha kwa Madani kunachitika mu mtima mwake ndipo) adati: "Ee 'Ata! رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه Ndamva kukoma kwa Imaan ndi Nur mu mtima mwanga, ndamasuka ku chikondi cha mkazi. Chonde

ndiwunikireni za chisilamu.” Sayyiduna ‘Ata رَحۡمَۃُ اللّٰہِ عَلَیۡہِ adamuitana kuti alowe chisilamu, ndipo adakhala msilamu ndi madalitso a بِسۡـمِ الـلّٰـہ.

Mayiyu yemwe sanali msilamu atamva za nkhani yolowa m’chisilamu, nayenso adadza pa bwalo lodalitsika la Sayyiduna ‘Ata-ul-Akbar رَحۡمَۃُ اللّٰہِ عَلَیۡہِ nati: “Ee iwe mtsogoleri wa Asilamu! Ndine mzimayi yemwe amakambidwa dzulo ndi Msilamu ongolowa kumene. Dzulo usiku ndidalota maloto omwe wina amandiuza kuti: ‘Ngati ukufuna kuona malo ako ku paradiso, pita ku bwalo lodalitsika la Sayyiduna ‘Ata-ul-Akbar رَحۡمَۃُ اللّٰہِ عَلَیۡہِ akakuonetsa malo ako’

Molimbikitsidwa ndi zimene ndidaona m’maloto amenewa, ndabwera kwa inu; chonde ndiuzeni, Kodi paradiso ili kuti?” Iye رَحۡمَۃُ اللّٰہِ عَلَیۡہِ adayankha, “ngati mukufuna (kupita) ku paradiso, muyeneka kutsegula khomo (chitseko) poyamba, pokhapo ndi pamene inu mukhoza kupita kumeneko.”

Adafunsa, “Ndingatsegule bwanji khomo lake?” Adayankha, “Werenga بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡـمٰنِ الرَّحِیۡمِ.” Atangowerenga بِسۡـمِ الـلّٰـہ (kusintha kwa Madani kudayenda mu mtima mwake ndipo) adati: “Ee ‘Ata! عَلَیۡہِ السَّلَام Ndapeza Nur mu mtima mwanga ndipo ndaona umulungu wa Allah عَزَّوَجَلَّ. Chonde ndiunikire zambiri za chisilamu.” Oyera wamkuluyu adamuitana kuti alowe chisilamu, ndipo adakhala msilamu ndi madalitso a بِسۡـمِ الـلّٰـہ. Kenako anabwelera kunyumba.

Usiku, adagona ndipo adalota maloto omwe adalowa m’paradiso komwe adawona nyumba zachifumu. Zolembedwa pa imodzi mwa nyumba za paradiso anali mawu oti بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡـمٰنِ الرَّحِیۡمِ, لَآ اِلٰهَ اِلَّا اللّٰهُ مُحَمَّدٌ رَّسُوۡلُ اللّٰهِ. Pamene akuwerenga zolembedwazo adamva wina akunena “Ee iwe owerenga! Allah عَزَّوَجَلَّ wakupatsira (zabwino zonse zakumwamba zomwe waziona m’maloto) ndi madalitso azomwe wawerenga.”

Atadzuka m’maloto ake anapempha kuti “Oo Allah عَزَّوَجَلَّ! Mwanditulutsa ku paradiso pambuyo pondilowtesa. Oo Allah! Chifukwa cha mphamvu zanu zonse, ndipulululumutseni ku zowawa za dziko lapansi.” Pamene adamaliza Dua lake, denga la nyumba yake linamugwera ndipo adamwalira mwachikhulupiliro. Choncho Allah عَزَّوَجَلَّ adamuchitira chifundo ndi madalitso a بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡـمٰنِ الرَّحِیۡمِ. *(Qalyubi Hikayat, p. 22)*

Allah عَزَّوَجَلَّ awachitire chifundo ndi kutikhulukira popanda mlandu chifukwa cha iwo!

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

تُوْبُوْا اِلَى الله اَسْتَغْفِرُ الله

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

*بِسْمِ اللّٰه, ki barakat hay, kitni achchi qismat hay*
*Hum nay payi Jannat hay, yeh sab Rab عَزَّوَجَلَّ ki rahmat hay*

*Ndi madalitso a بِسْمِ اللّٰه, ndi chisomo cha Allah*
*Tapeza mwayi ndipo tidzalowa kumwamba posachedwa.*

Abale okondedwa achisilamu! Chifunda cha Allah عَزَّوَجَلَّ ndi chachikulu. Amawatsogolera anthu oipisitsa kupita ku mabwalo a Auliya wake, potero akuwapangitsa kukhala oopa Mulungu komanso opambana.

اَلْحَمْدُ لِلّٰه, iwo amene amagwirizana ndi Dawat-e-Islami, gulu la dziko lonse lapansi komanso losagwirizana ndi ndale lotsata Qur'an ndi Sunnah, amanyadira kukhala ozipereka kwa Awliya a Allah. Odzipereka awa akamayenda ndi zolinga zenizeni mu Madani Qafilah, olimbikitsa Sunnah, kuwaitanira anthu ku chilungamo, nthawi zina, ngakhale osakhulupilira amalowa chisilamu. Izi ndi zodabwitsa za Madani Qafilah.

## Munthu Osakhala Msilamu Adalandira Chisilamu

Mlaliki wa Dawa ochokera ku Khanpur (Punjab, Pakistan) adati: "Madani Qafilah olimbikitsa Sunnah adadza mumzinda wathu kuchokera ku Bab-ul-Madina Karachi. Pamodzi ndi anthu a Madani Qafilah ndinalinso ndi mwayi kutenga nawo gawo pa ulendo oitanira anthu ku chilungamo. Kusonkhanitsa anthu kunja kwa sitolo zosokera tidapereka 'Kuitanila ku chilungamo.' Kuyankhula kutatha, wantchito wachinyamata wamsitoloyo anati 'ine sindine Msilamu. 'Kuitanila ku chilungamo' kwanu kwakhudza

kwambiri moyo wanga. Chonde ndipangitseni kukhala Msilamu.' اَلْحَمْدُ لِلّٰه, kenako adalowa chisilamu."

*Maqbul Jahan bhar ho Dawat-e-Islami*
*Sadaqah tujhay ay Rab-e-Ghaffar Madinay Ka*

*Dawat-e-Islami ikhale yolemekezeka padziko lonse lapansi*
*Chifukwa cha Madinah, Oo mlengi wa dziko*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## (3) Omenya Wachikulile Opembedza

Wachifwamba wina yemwe sanali msilamu analowa m'nyumba yachifumu ndipo sanapeze aliyense kupatulapo munthu wachikulire opembedza komanso mwana wake wamkazi. Wachifwambayo ankafuna kupha munthu wachikulire opembedzayo ndikugwira mwana wake wamkazi ndi chuma chake. Ndi cholinga choipachi, adalimbana ndi nkhalambayo, koma wachikulire ooneka ngati ofooka adasanduka omenya wamphamvu! Nthawi yomweyo analimbana ndi wachifwambayo ndi kumugwesa pansi.

Chigawengacho chinangogudubuzika n'kuukila munthu wachikulile koma chinagonjaso. Kulimbana kudapitilira pakati pawo ndipo bambo wachikulire opembedza adagonjetsa wachifwamba nthawi zonse. Panthawiyi, ataona kuti nkhalambayo ikubwereza mawu chapansipansi, wachifwambayo anafunsa kuti, "Mukunena chiyani?" Poulura chinsinsi cha mphamvu zake, bambo wachikulire opembedzayo adati uku akumwetulira, "Ndine munthu ofooka kwambiri koma ndikuwerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم kotero Allah عَزَّوَجَلَّ wandilora kukugonjetsani."

Chigawenga chija chitangomva izi chidathedwa nzeru ndi kusintha kwa Madani mu mtima mwake ndipo adati: "Chingakhale chachikulu komanso cholemekezeka bwanji chipembedzo chomwe kupemphera kamodzi kokha kwa بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم ndi kodabwitsa kwambiri!" Poyankhula izi, adalowa chisilamu ndi madalitso akumva kuwerenga kwa بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم. Pamenepo unayamba ubale wapamtima pakati pawo.

Pamene nkhalamba yoopa mulungu idamwalira, Msilamu watsopanoyo adakwatiwa ndi mwana wa mkazi wa nkhalambayo ndipo adapatsidwa chuma chake chonse pamodzi ndi nyumba yachifumu. *(Asrar-ul-Fatihah, p. 165)*

Allah عَزَّوَجَلَّ awachitire chifundo ndi kutikhululukira ife popanda mlandu chifukwa cha iwo!

*Hamd hay us zat ko jis nay Musalman ka diya*
*Ishq-e-Sultan-e-Jahan sinay mayn pinhan kar diya*

*Ulemelero ukhale kwa yemwe watidalitsa ndi chisilamu*
*Komanso wadzadza mitima yathu ndi kuzipereka kwa Sultan wapadziko lapansi*

Abale Achisilamu Okondedwa! Ndithu, nkhalamba yoopa Mulungu adali Wali wa Allah. Mobwerezabwereza anagonjetsa munthu yemwe sanali msilamu ndi madalitso a بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ, chomwe chinaliso chozizwitsa chopatulika cha moyo wake. Kupitilira apo, omwe sanali msilamu adadalitsidwanso ndi mphatso yachisilamu ndi madalitso a بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ. mverani fanizo lositsimutsa komanso lolimbikitsa chikhulupiliro la mayi wina opembedza yemwenso anali odzipereka pa بِسْمِ اللّٰه.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## (4) Kupulumutsa Thumba Kuchoka Pachitsime

Panali mayi wina opembedza yemwe nthawi zambiri ankakonda kunena بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ. Mwamuna wake yemwe anali wachinyengo adakwiya kwambiri ndi chizolowezi chakechi. Mokwiya ndi nsanje, anakonza chiwembu chonyazitsa mkazi wake m'njira yakuti asadzaiwale. Tsiku lina popeleka chikwama kwa mkazi wake, iye anati "Chisungeni pamalo otetezeka." Mayiyo anatenga chikwamacho n'kuchisunga pamalo otetezeka. Patapita masiku angapo, mwamunayo anatenga chikwamacho mobisa n'kuchiponya m'chitsime cha panyumba pake kuti mkazi wake asachipeze.

Patapita nthawi, anapempha mkazi wake kuti abweretse chikwamacho. Adafika pomwe adachisunga. Atangowerenga بِسْمِ اللّٰه, Allah عَزَّوَجَلَّ adamulamula Jibrail عَلَيْهِ السَّلَام kuti apite mwachangu ndikukayika chikwamacho pomwe chidali. Mwansangansanga, Sayyiduna Jibrael عَلَيْهِ السَّلَام adatulutsa chikwamacho mtchitsime ndikukachisiya pomwe chidali.

Pamene mkazi opembedza adatambasula dzanja lake kuti atenge chikwama, adapeza momwe adachisungira. Atadabwa ndi chikwamacho, mwamuna wake analapa moona mtima kwa Allah عَزَّوَجَلَّ. *(Qalyubi Hikayat, p. 11)*

Allah عَزَّوَجَلَّ awachitire chifundo ndi kutikhululukila popanda mlandu chifukwa cha iwo!

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Abale okondedwa achisilamu, zonsezi ndi zodabwitsa za بِسْمِ اللّٰه. Wamwayi amene amawerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ asanachite chilichonse chololedwa ndi cholemekezeka, kaya chili chofunika kapena chaching'ono, amathandizidwa ndi Ghayb panthawi yamavuto.

*Mahabbat mayn aysa guma Ya Ilahi*
*Na paun phir apna pata ya Ilahi*

*Ndikhalebe wokhazikika 'mkudzipereka kwa inu, inu wamphamvu zonse*
*Ndikhalebe osayanjanitsika ndi dziko, Oo wamphamvu zonse*

## (5) Nyumba Ya Farao

Asanazinene kuti ndi Mulungu, Farao anamanga nyumba yachifumu ndipo analemba بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ pa khomo lake lakunja. Pamene adazitchula kuti ndi Mulungu, Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام adamupempha kuti akhulupilire mwa Allah عَزَّوَجَلَّ koma adakana. Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام modzichepetsa adati kwa Allah عَزَّوَجَلَّ: "Oo Allah عَزَّوَجَلَّ! Ine ndikumuitanira kwa inu mobwerezabwereza koma sakusiya kunyoza. Sindikuona zisonyezo zabwino mwa iye." Allah عَزَّوَجَلَّ adati: "Ee iwe Musa (عَلَيْهِ السَّلَام) Ukufuna kuti aonongeke monga momwe ukuwonera Kufr (Kusakhulupilira kwake), koma ine ndikuona dzina langa lomwe adaliremba pakhomo pake!" *(Tafsir Kabir, vol. 1, p. 152)*

## Chitetezo Cha Nyumba

Abale okondedwa achisilamu! Tilembe بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ pa khomo lakunja la nyumba zathu. اِنْ شَآءَاللّٰه tidzatetezedwa ku mitundu yonse ya matsoka apadziko lapansi.

Sayyiduna Imam Fakhruddin Razi رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه anati: “Amene alemba بِسۡمِ اللّٰهِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِيۡم pa khomo lalikulu la nyumba yake sadzakhala ndi mantha oonongeka (padziko lapansi) ngakhale atakhala M’kafiri, ndiye chitetezo komanso madalitso pa msilamu yemwe بِسۡمِ اللّٰهِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِيۡم analembedwa pa mtima pake kwa moyo wake onse chingakhale chochuluka bwanj!” *(Tafsir Kabir, vol. 1, p. 152)*

صَلُّوۡا عَلَى الۡحَبِيۡب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## (6) Munthu Kapena Chiwanda?

Zinanenedwa mu ‘Kitab-un-Nasaih’ kut m’dzakazi wa bwenzi lotchuka Sayyiduna Abu Darda رَضِىَ اللّٰهُ عَنۡه nthawi ina adafunsa “Olemekezeka! Ndiuzeni zoona, kodi ndinu munthu kapena chiwanda?” Iye رَضِىَ اللّٰهُ عَنۡه anayankha “ اَلۡحَمۡدُ لِلّٰه Ndine munthu” Wantchito uja anati “Koma inuyo simunthu kwa ine chifukwa ndakhala ndikukupatsirani chiphe kwa masiku makumi anayi otsatizana koma chiphecho sichikukhudzirani inu!” Iye رَضِىَ اللّٰهُ عَنۡه adati “kodi sukudziwa kuti amene akupanga Zikr kwa Allah عَزَّوَجَلَّ m’makhalidwe amtundu uliwonse sangavulazidwe ndi chilichonse? اَلۡحَمۡدُ لِلّٰه Ndimapanga Zikr kwa Allah عَزَّوَجَلَّ ndi Ism-e-A’zam.” Wantchitoyo anafunsa kuti “Ism-e-A’zam ndi chiyani?” Adayankha “Nthawi zonse ndimawerenga mawo utsatirawa ndisanadye kapena kumwa chilichonse”

بِسۡمِ اللّٰهِ الَّذِىۡ لَا يَضُرُّ مَعَ اسۡمِه شَىۡءٌ فِى الۡاَرۡضِ وَلَا فِى السَّمَاءِ وَهُوَ السَّمِيۡعُ الۡعَلِيۡم

**Tanthauzo: Ndikuyamba ndi dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ ndi madalitso amene dzina lake palibe chimene chingabweretse vuto lilironse kuchokera pansi ndi kuthambo. Iye ngwakumva zonse, Ngodziwa zonse.**

Kenaka Olemekezeka uja anamufunsa chifukwa chimene anamuikira poison. Adayankha kuti adatero chifukwa anali ndi chakukhosi. Atamva izi adati: "Ndikukumasulani chifukwa cha chikomerezo cha Allah عَزَّوَجَلَّ ndipo ndakukhululukira pazomwe mwandichitira." *(Hayat-ul-Haywan-ul-Kubra, vol. 1, p. 391)*.

Allah عَزَّوَجَلَّ amukhululukire iye ndi ife popanda kuwerengera chifukwa cha iye.

سُبْحٰنَ اللّٰه! Ubwino ndi ukulu wa abwenzi odalitsika sizingafotozeledwe m'mawu. Makhalidwe a anthu olemekezekawa akuonetseradi tanthazo la lamulo la Mulungu اِدْفَعْ بِالَّتِیْ هِیَ اَحْسَنُ (Tanthauzo kuchoka mu Kanz-ul-Iman: 'Ee, iwe omvera! chotsa choipa ndi kusinthanitsa ndi chabwino'). *(Part 24. Surah Ha-Mim As-Sajdah, verse 34)*

M'malo momulanga m'dzakazi amene adamutulira chiphe mobwerezabwereza, Sayyiduna Abu Darda رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anamumasura ndikumukhululukira. Mvetselani fanizo lina lofanana nalo.

## (7) Chakudya Chakupha

Mdzakazi wa Sayyiduna Abu Muslim Khulani قُدِّسَ سِرُّهُ الرَّبَّانِی amamuikira chiphe iye chifukwa chomukwiira koma chiphecho sichinali ndi mphamvu pa iye. Izi zinapitilira kwa nthawi yaitali kwambiri. Pamapeto pake adati: "ndakhala ndikukuikilani chiphe kwa nthawi yaitali, koma chiphecho sichimagwira ntchito pa inuyo." Olemekezeka oyerayo رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه adafunsa "N'chufukwa chiyani munachita zimenezi?" Iye adayankha: "Chifukwa chakuti mwakalamba kwambri." Adati: "اَلْحَمْدُ لِلّٰه Nthawi zonse ndimawerenga بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْم ndisanadye kapena kumwa chilichonse (Ndi madalitso a izi, ndatetezedwa ku zotsatira za chiphecho)." Kenako anamumasula. *(Qalyubi Hikayat, p. 52)*

*Bay-nawa muflis-o-muhtaj gada kaun? Kay mayn*
*Sahib-e-Jud-o-Karan wasf kis ka? Tyra*

*Ndine osowa chochita*
*Ndipo kuwolowa m'manja ndi chikhalidwe chanu*

*(Zauk-e-Na'at)*

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب صَلَّی اللّٰهُ عَلٰی مُحَمَّد

سُبْحٰنَ اللّٰه! Ndi zazikulu chotani nanga ndi zodabwitsa zanji za بِسْمِ اللّٰه

## Chinyengo Cha Satana

Nzoonekeratu kuchokera mu nkhani zam'mwambazi kuti ngakhale mutadya Chiphe (poizoni) mutawerenga بِسْمِ اللّٰه sizikukhudzeni, koma ndi ndani angaziike pa chiopsezo

chachikuluchi? Tikudziwa kuchokera muzochitika kuti ngati tadya zakudya zokometsera (kwambiri), mwachitsanzo, ngakhale titawerenga بِسۡـمِ الـلّٰـه timakhala ndi vuto la m'mimba.

## Kuchiza Chinyengo Cha Satana

Ngati chitaomberedwa bwino ndi mfuti yapamwamba, chipolopolo chingaphe ngakhale mkango. Momwemonso mapemphero ndi ma Dua ali ngati zipolopolo pomwe lilime la owerenga lili ngati mfuti. Ma Dua ndi ofanana, koma malilime athu sali ngati a Maswahaaba ndi oyera mtima olemekezeka. Kodi kuchita bwino kungapezeke bwanj mwa lilime lochita machimo a kunama, miseche, kutukwana, kuvulaza ndi kuchitira ena zoipa? Timachitaso Dua, koma tikakumana ndi mavuto timapita kwa anthu oopa Mulungu ndikuwapempha kuti atichitire ma Dua. Izi zili choncho chifukwa chakuti aliyense ali ndi maganizo akuti Dua yoyankhulidwa ndi lilime loyera, ndiyothandiza kwambiri.

Mosakaikira, powerenga بِسۡمِ اللّٰهِ الرَّحۡـمٰنِ الرَّحِيۡم Sayyiduna Khalid Bin Walid رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ adamwa chiphe mopanda mantha ndipo sanavulazidwe ndi zotsatira za Chiphecho chifukwa lilime lake, mtima wake komanso thupi lake zonse zinali zoyera ku machimo اَلۡحَمۡدُ لِلّٰه. Uwu ndi Mdalitso wa Allah عَزَّوَجَلَّ kuti chiphe chisamukhudze.

Chimodzimodzi, Sayyiduna Abu Darda ndi Sayyiduna Abu Muslim Khulani رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُمَا ankatchula dzina lodalitsika la Allah عَزَّوَجَلَّ ndi malilime awo oyera, ndipo chiphecho chinkasanduka chopanda vuto kwa iwo. Apo ayi, Chiphe ndi, muzonsezi, chiphe ndipo chikhoza kuvulaza kwambiri thupi la munthu.

Zakupha kwa poizoni tingafotokozenso ndi nkhani yotsatirayi yotengedwa m'buku la 'Kitab-ul-Azkiya', Paulendo wa Haji, gulu la anthu obwera ku Haji linafika pa kasupe wamadzi ndipo adamva kut pafupi ndi pamenepo panali banja la madotolo akatswiri. Chowiringula chimene anapanga choyendera banjali chinali chakuti anakanda nsonga ya mnzawo ndi kanthambi ka m’nkhalango, n’kumusiya akututuluka magazi pang’ono. Ndipo m’mene anapita naye ku khomo la nyumba yao, m’modzi wa iwo anafuwula, nanena, “Kodi pali yemwe amachiza bala lolumidwa ndi njoka pano?” Pokumva izi, kamtsikana kanatuluka m’nyumbamo. Atayang’ana bwinobwino pa balalo, adanena “Palibe njoka yomwe yamuluma munthuyu, m’malo mwake, chibwano chake

chakwapulidwa ndi chinthu chomwe njoka yapoizoni idakodzerapo. Munthuyu sadzakhalaso ndi moyo ndipo adzafa dzuwa likatuluka mawa” Kenako, zomwe mtsikanayo adalosera zidachitika ndipo munthu uja adamwalila dzuwa litangotuluka. *(Hayat-ul-Haywan-ul-Kubra, vol. 1 p. 391)*

E Allah عَزَّوَجَلَّ! Tidalitseni ndi mwayi obwerezabwereza بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم. Tikhululukireni ndi kutimasula ku machimo. E Allah عَزَّوَجَلَّ! Tidalitseni ndi kufera chikhulupiliro pansi pa chimphika chobiliwira pamene tikuwona masomphenya a Mneneri okondedwa ndi odalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, ndi kuikidwa mmanda a Jannat-ul-Baqi, ndi moyandikana ndi Mtumiki wanu okondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ku Jannat-ul-Firdaus! Khululukirani Ummah onse wa Mneneri wanu okondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.

اٰمِيْن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد
تُوْبُوْا اِلَى اللّٰه اَسْتَغْفِرُ اللّٰه
صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

الحمد لله رب العلمين والصلوة والسلام على سيد المرسلين اما بعد فاعوذ بالله من الشيطن الرجيم بسم الله الرحمن الرحيم

## Kukhala msilamu woopa mulungu ndi wopemphera Salah

Khalani usiku onse mu ijtima ya Dawat-e-Islam yolimbikitsa sunna yomwe imachitika lachinayi sabata iliyonse pambuyo pa salat-ul-maghrib m'dera lanu, chifukwa chomusangalatsa Allah عزوجل, ndi zolinga zabwino. Kuti muphunzire ma Sunnah, chipangeni kukhala chizolowezi chanu choyenda ndi Madani Qafilah masiku atatu mwezi uliwonse pamodzi ndi odzipereka a Rasool, kumalizitsa kulemba mkabuku ka Madani In'amaat tsiku lilonse kuchita fikr-e-Madina ndikukapereka kwa m'bale wachisilamu woyenera yemwe ali ndi udindo mdera lanu tsiku loyamba la mwezi uliwonse wa Madani.

**Cholinga changa cha madani**

Ndiyenera kuyesetsa kudzikonza ndekha ndi anthu apadziko lonse lapansi, ان شاء الله. Ndicholinga choti tidzisinthe tokha, tiyenera kuchitapo kanthu pa Madani In'amaat ndikuyesetsa kusintha anthu a dziko lonse lapansi, tiyenera kuyenda ndi Madani Qafilah ان شاء الله.




Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagaran
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan
UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 7213
Web: www.dawateislami.net | E-mail: translation@dawateislami.net